

# *Kuzindikira Kuyankhula*

*Kwa*

*Mulungu*

## **HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a Harvest International Institute ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolera zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	3
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	7
1. Kuzindikira Kuyankhula Kwa Mulungu.....	8
2. Ngati Munthu Wina Achita... Adzazindikira” .....	19
3. Chifuniro Cha Mulungu.....	32
4. Kutenga Njira Yolakwika .....	45
5. Chifaniziro Cha Chifuniro Cha Mulungu.....	55
6. Kodi Mulungu Amayakhula Bwanji Ndi Munthu.....	72
7. Chitsamba Choyaka Moto Chosanyeka.....	86
8. Mchitidwe Okaikitsa .....	100
9. Chifaniziro Cha Baibulo Chakapangidwe Ka Chiganizo.....	111
10. Mwayesa Ndi Kulephera Kodi?.....	117
11. Chifuniro Cha Mulung Ndi Mazuzo.....	126
12. Magawo Asanu Ndi Awiri Amavumbulutso.....	145
13. Mayankho amafunso odziyesa nokha.....	151

## **KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI**

### **KAKONZEDWE KA BUKULI**

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Werengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwaphunzira.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

### **ZOWERENGA ZINA ZOFUNIKA PHUNZIRA PHUNZIROLI**

Mudzafunikira Buku Lopatulika

### **NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU**

#### **MKUMANO WOYAMBA**

**Kutsekulira:** Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Ntchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### **MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO**

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi pa utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzani mayeso pamene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

## **PHUNZIRO: KUZINDIKIRA KUYANKHULA KWA MULUNGU**

### **MAU OYAMBA**

“Kodi cholinga cha Mulungu pa ine ndi chiani?”

Ili ndi funso limene nthawi zambiri okhulupirira amadzifunsa ndipo limene atsogoleri amayenera kulidziwa bwino chifukwa anthu amakhala akubwera kwa iwo kudzafunsira uphungu.

Tsiku ndi tsiku, okhulupirira amakhala akupanga ziganizo zimene zimatha kuonetsera ngati akuchita chifuniro chagwiro cha Mulungu. Chifukwa cha ichi, ndizofunikira kwambiri kuti munthu azindikire kuyankhula kwa Mulungu, kuzindikira chifuniro chake, ndi kupanga ziganizo zoyenera tsiku ndi tsiku. Izi ndi zofunika chifukwa chiganizo chilichonse chaching’ono chimatha kusokoneza kuzindikira chifuniro cha Mulungu pa moyo wathu.

Munthu ayenera kupanga ziganizo Molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Dongosolo limeneli linakhazikitsidwa pachiyambi pomwe pamene Adamu ndi Hava anayikidwa mmunda wa Edeni uja (Genesis 1-3). Chifuniro cha Mulungu pa Adamu ndi Hava chinali choti apereke mayina kwa nyama zonse, asamale munda uja, akhale pa ubwenzi wina ndi mzake, komanso kuti abalane kuti alidzadze dziko lapansi. Koma chinthu chofunikira chinali chakuti akhale pachiyanjano ndi Mulungu. Adamu ndi Hava anachenjezedwanso pa chimene sichinali chifuniro cha Mulungu. Iwo samayenera kudya chipatso cha mtengo wachidziwitso cha chabwino ndi choipa.

Kuonjezera nkhani ya Adamu, Baibulo ndi mbiri ya ziganizo zimene anthu komanso mafuko anapanga molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Ndipo mukhoza kuwerenga za kuchita bwino komanso kulephera kwa anthu amenewa.

Chinthu chimodzi chokondweretsa ndi chakuti, Baibulo limaonetsa kuti, Mulungu ali ndi malingaliro kapena ndondomeko yokhudza munthu wina aliyense. Ndipo kuti mukwanitse malingaliro amenewa, muyenera kuzindikira kulankhula kwa Mulungu. Muyenera kudziwa mmene Mulungu analakhulira kalero ndi mmene akulankhulira lero lino.

Phunziro ili lifotokoza mmene Mulungu analankhulira ndi anthu komanso mmene mungapezere chifuniro cha Mulungu pa moyo wanu. Ndongomeko zakuzindikira kulankhula kwa Mulungu komanso kuchita chifuniro chake zaperekedwa mu Buku limeneli. Chifaniziro cha chifuniro cha Mulungu mu malemba komanso zitsanzo za mmene Mulungu amaonetsera chifuniro chake zikambidwa mu buku limeneli

Chifaniziro chothandiza kupanga chiganizo zifotokozeredwa mu buku limeneli. Ndipo ndondomeko zothandiza kupewa kupanga ziganizo zolakwika zifotokozeredwa, kodi muchite chiani pamene mwasemphana ndi Chifuniro cha Mulungu. komanso tiona mmene mungachitire ndi zinthu zokaikitsa. Njira zokwana zisanu ndi ziwiri zopezera chifuniro cha Mulungu zifukulidwa.

Maphunziro a Harvestime International Institute amatsindika kwambiri pa zimene Yesu anaphunzitsa ndi cholinga chofuna kukonzekereza amayi ndi abambo kuti akalalike dziko lonse lapansi ndi Uthenga Wabwino. Choonadi chimodzi chimene Yesu anavumbulutsa ndi chakuti Mulungu amalankhula.

**Ine ndine Mbusa Wabwino; ndipo ndizindikira zanga, ndi zanga zindizindikira ine, (Yohane 10:14)**

**Ndipo nkhoa zina ndiri nazo, zimene siziri za khola ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo zidzamva mau anga; ndipo zidzakhala gulu limodzi, mbusa mmodzi, (Yohane 10:16)**

**Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine. (Yohane 10:27)**

Mulungu ali ndi chikonzero chofuna kukhala pa ubale waukulu ndi munthu. Munthu amadziwika ndi Mulungu ndipo munthu akhoza kumudziwa Mulungu.

## **ZOLINGA ZA MAPHUNZIRO**

Pamapeto pa maphunziro awa, muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kufotokozero ubale wakudziwa kuyankhula kwa Mulungu ndi kuchita chifuniro chake.
- Kufotokozero kufunikira kodziwa Chifuniro cha Mulungu.
- Kufotokoza mmene Mulungu amavumbulutsira chifuniro chake.
- Kumvetsetsa chifuniro cha Mulungu chopezeka mu Baibulo.
- Kupeza chifuniro cha Mulungu pa zinthu zimene sizinatchulidwe mu Baibulo.
- Kugwiritsa ntchito njira za Baibulo zakapangidwe kachiganizo.
- Kukonza ziganizo zolakwikwa.
- Kufotokozero njira zisanu ndi imodzi za mavumbulutso
- Kugawana ndi ena ndondomeko za Baibulo zothandiza kuzindikira Kulankhula kwa Mulungu.

## **ZOLINGA ZOTI MUKWANILITSE INU MWINI**

Chifukwa chakuti phunziro ili limakamba za kuzindikira kuyankhula kwa Mulungu ndi chifuniro chake, ndi kofunika kuti mukhazikitse zolinga zimene inu ngati munthu mukufuna kukwaniritsa. Cholinga chanu chikhoza kukhala kupeza cholinga cha Mulungu pa zinthu zina zake, kupeza yankho la vuto, kapena kupeza chifuniro cha Mulungu pa moyo, pa ntchito imene mumagwira tsiku ndi tsiku komanso pa utumiki wanu. Tchulani zolinga zimene mukufuna kukwanitsa mu mizere imene ili munsimu.

Tsilizani chiganizo ichi “ndikufuna kumva kuyankhula kwa Mulungu ndi chifuniro chake pa zinthu izi.....”

---

---

---

---

---

## CHAPUTALA 1

### KUZINDIKIRA KUYANKHULA KWA MULUNGU

#### ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili, muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kuonetsera kudzera mu malemba kuti Mulungu amayankhula ndi munthu.
- Kufotokoza ubale wakudziwa kuyankhula kwa Mulungu ndi kuchita chifuniro chake.
- Kusiyanitsa pakati pa “rhema” mau a Mulungu ndi “logos” Mau a Mulungu.
- Kufotokozerana tanthauzo la chifuniro cha Mulungu.

#### VESI YOTSOGOLERA

**Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine. (Yohane 10:27).**

Dzina laphunziro ili “Kuzindikira kuyankhula kwa Mulungu” limatanthauza zinthu zambiri:

**Choyamba:** Kuli Mulungu.

**Chachiwiri:** Amayankhula ndi munthu.

**Chachitatu:** Munthu akhoza kuzindikira kuyankhula kwa Mulungu.

**Chachinayi:** Mulungu ali ndi choti ayankhule

Tiyeni tiunikire mfundo ili yonse yatchulidwa payokha payokha:

**Choyamba:** phunziro ili lakhazikika pa choonadi choti pali Mulungu amene wadzionetsera yekha kudzera mu Mau ake olembedwa amene ndi Baibulo.

**Chachiwiri:** Baibulo ndi mau a Mulungu owuzilidwa amene akuyankhula ndi munthu. Limaonetsera njira zimene anagwiritsa ntchito pofuna kuyankhula ndi Mulungu ndi mmene anthu kapena mafuko anayankhira kapena kuchitira pakumva kuyankhula kumeneku. Nthawi zambiri Baibulo limagwiritsa ntchito mau oti “atero ambuye” pamene Mulungu akuyankhula ndi munthu. Izi zimangochitira umboni kuti Mulungu amayankhula ndi munthu.



Mwachitsanzo, timawerenga nkhani ya Balamu ku Numeri 22. Mulungu anayankhula ndi Balamu koma iye sanafune kumvera. Chifukwa chakuti Mulungu amafuna kuti ayankhule ndi munthu, Iye anangosankha kugwiritsa ntchito ngamira. Ndipo Balamu:

**koma anadzudzulidwa pa kulakwa kwace mwini; buru wopanda mau, wolankhula ndi mau a munthu, analetsa kuyarukakwa mneneriyo. (2 Petro 2:16)**

**Chachitatu:** Baibulo limachitira umboni kuti okhulupirira akhoza kuzindikira kuyankhula kwa Mulungu. Yesu anati:

**Ine ndine Mbusa Wabwino; ndipo ndizindikira zanga, ndi zanga zindizindikira ine,**

**Ndipo nkhosa zina ndiri nazo, zimene siziri za khola ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo zidzamva mau anga; ndipo zidzakhala gulu limodzi, mbusa mmodzi,**

**Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine. (Yohane 10:14,16,27)**

**Chachinayi:** Mulungu ali ndi chinachake choti ayankhule kwa Munthu ndipo tikuchenjezedwa:

**Momwemo, monga anena Mzimu Woyera, Lero ngati mudzamva mau ace,**

**umo anenamo, Lero ngati mudzamva mau ace, Musaumitse mitima yanu, monga pa kupsetsa mtima. (Ahebri 3:7,15)**

Chiyesero ndi kupsetsa mtima Mulungu zatchulidwa apazi zikufotokozerana kusamvera kwa ana a Israeli.

Israeli atalanditsidwa mu ukapolo wa Ku Ayigupto, iwo sanali kumvera Mulungu akayankhula. Mu vesi imeneyo, Mulungu akuchenjeza kuti tiyenera kuchitapo kanthu pamene iye wayankhula ndikuti tisakhale osamvera ngati mmene anachitira Israeli.

Mau oti “Lero, ngati mumve mau ake,” akuchitira umboni kuti Mulungu akuyankhulabe ndi anthu ake lero lino ngati mmene ankachitira kale. Chenjezo ili likuchitira umboni kuti zimene iye amafuna kuti ayankhule ndi zofunika kwambiri.

## **MAU AMBIRI**

Baibulo limaonetsera kuti pali mau oyankhulidwa ambirimбири ofuna kuti amvedwe ndi anthu:

**Iripo, kaya, mitundu yambiri yotere ya mau pa dziko lapansi, ndipo palibe kanthu kasowa mau. (1Akorinto 14:10)**

Kodi mau amenewa ndi chani pa dziko lapansi?

### **MAU A MUNTHU:**

Mau amunthu ndi osavuta kuwazindikira. Ndi mau amene amamveka ndi makutu athu.

**Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati, Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu. (Macitidwe 5:29)**

Nthawi zina mau amunthu amatha kupereka uphungu wabwino, koma nthawi zina mau amunthu amatsutsana ndi mau a Mulungu ndipo inuyo muyenera kumvera Mulungu.

### **MAU A SATANA**

Mau a Satana anamveka koyamba pamene anayankhula ndi Hava mmunda wa Edeni (Genesis3:1,4,5). Koma mau a Satana ndi abodza, ndi onyenga ndipo nthawi zonse cholinga chake ndi kumutsogolera munthu kuti achimwe pa maso pa Mulungu. Mukhoza kuona izi mutawerenga kuyesedwa kwa Yesu ndi Satana mu buku la Mateyu 4:1-13. Mukhonza kuphunzira za kulankhulana pakati pa Satana ndi Mulungu powerenga Yobu 1:7-12 ndi 2:1-6.

Mizimu yoipa kapena ziwanda nazo zimalankhula:

**Pakuti ambiri a iwo akukhala nayo mizimu yonyansa inawaturukira, (Macitidwe) 8:7**

**Ndipo munali m'sunagoge munthu, wokhala naco ciwanda conyansa; napfuula ndi mau olimba, kuti, Ha! tiri ndi ciani ndi Inu, Yesu wa ku N azarete? kodi munadza kutiononga ife? ndikudziwani Inu muli yani, ndinu Woyera wace wa Mulungu. (Luka 4:33-34)**

Nthawi zina mau a Satana mukhoza kuwamva pamene ziwanda zigwiritsa ntchito mawu a munthu ogwida ndi ziwanda. Koma nthawi zambiri Satana amayankhula mau osamveka. Iye amayankhula bodza, chinyengo, ndi maganizo oipa kudzera mmaganizo anu.

## MAU AYINU MWINI

Mau a inu mwini ndi pamene munthu ayankhula yekha. Mukhoza kuwerenga zitsanzo zopezeka pa Luka 16:3, 18:4 ndi Yona 4:8 pamene Yona analakalaka atafa. Koma Baibulo limachenjeza mau a ife mwini.

**Inu Yehova, ndidziwa kuti njira ya munthu siri mwa iye mwini; sikuli kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ace. (Yeremiya 10:23)**

### MAU A MULUNGU:

Yesu anati okhulupirira akhoza kudziwa Mau a Mulungu komanso ndi kuwasiyanitsa ndi mau a zinthu zina.

**Iyeyu, wapakhomo amtsegulira ndi nkhoa zimva mau ace; ndipo aitana nkhoa za iye yekha maina ao, nazitsogolera kunjira. Pamene adaturutsa zonse za iye yekha, azitsogolera; ndi nkhoa zimtsata iye; cifukwa zidziwa mau ace. Koma mlendo sizidzamsata, koma zidzamtshawa; cifukwasizidziwa mau a alendo. (Yohane 10:3-5)**

Okhulupirira akufananitsidwa ndi nkhoa. Chikhalidwe cha nkhoa ndichakuti simadziwa kumene ikupita kotero kuti iyenera kutsogozedwa. Yesu anati iye ndi m'busa kapena kuti wotsogolera nkhoa. Ndipo anati nkhoa zake zimamva mau ake ndikutsata iye osati mau a anthu, kapena a Satana.

### KUMVA MAU A MULUNGU

Tsekulani Baibulo lanu ndipo muwerenge Genesis chaputala 1-3. Ma chaputala amenewa amaonetsera za kulengedwa kwa dziko lapansi ndi munthu oyamba amene ndi Adamu ndi Hava. Pamene Mulungu analenga, Iye anayankhula chifuniro chake kwa Munthu. Iye anapereka malangizo olunjika kwa Adamu ndi Hava. Iwo amayenera kupereka mayina kwa nyama zonse, kulima munda uja, kukhala pa ubale wina ndi mzake, kubalana ndikulidzadza dziko lonse lapansi. Koma choposa zonse, iwo amayenera kukhala paubwenzi kapena paubale ndi Mulungu. Pamene Mulungu anayankhula, Iye anafotokozera zolinga zake kwa Adamu ndi Hava:

**Ndipo Yehova Mulungu anamuza munthuyo, nati, Mitengo yonse ya m'munda udyeko; koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa, usadye umenewo; cifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu. (Genesis 2:16-17)**

Kudzera mu mau ake, chifuniro cha Mulungu chinavumbulutsidwa kwa Adamu ndi Hava. Iwo anali ndi ufulu odyo chipatso china chilichonse kupatula chipatso cha mtengo wa chidziwitso cha choipa ndi chabwino.

Koma Adamu ndi Hava sanatsate dongosolo la Mulungu. Ndipo iwo anasankha kumvera mau a Satana pakudya chipatso choletsedwa. Iwo atazindikira kulakwitsa kwao, anabisala posafuna kupezeka pamaso pa Mulungu.

**Ndipo anamva mau a Yehova Mulungu alinkuyendayenda m'munda nthawi yamadzulo: ndipo anabisala Adamu ndi mkazi wace pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda. Ndipo Yehova Mulungu anaitana mwamunayo nati kwa iye, Uli kuti? (Genesis 3:8-9)**

Ndi tchimo limene limamulekanitsa munthu ndi Mulungu. Sikuti Mulungu anachotsa kupezeka kwake pa munthu chifukwa cha tchimo, koma munthu anabisala yekha pamaso pa Mulungu. Tchimo limabweretsa kuumitsa kwa mtima ndipo baibulo limachenjeza:

**Umo anenamo, Lero ngati mudzamva mau ace, Musaumitse mitima yanu, monga pa kupsetsa mtima. (Ahebri 3:15)**

Mulungu akufuna kuti ayankhule ndi munthu, koma kuti iye atero pakufunika kuti pakhale ubale. Koma tchimo ndi limene limamuchotsa munthu pa ubale ndi Mulungu, limamuumitsa mtima wake, komanso kumulepheleretsa kuti adziwe kuyankhula kwa Mulungu.

## **MAU NDI CHIFUNIRO CHA MULUNGU.**

Nthawi zambiri okhulupirira amakhala akufunsa. “Kodi chifuniro cha Mulungu ndi chiani” kodi timatanthauza chani pamene tikuti tikufuna kudziwa chifuniro cha Mulungu? Zimatanthauza kuti tikufuna kudziwa cholinga cha Mulungu pa moyo wathu. Timakhala kuti tikufuna chitsogozo pa ziganizo zosiyanasiyana ndi cholinga choti tipange ziganizo zoyenera. Cholinga chenicheni ndi kukhala ndi chitsogozo chake munyengo ina ili yonse. Funso loyenera kufunsa ndi loti: “kodi ndingadziwe bwanji mau kapena kuyankhula kwa Mulungu?” Zotsatira za kuzindikira mau a Mulungu ndi kudziwa chifuniro cha Mulungu.

Cholinga cha Mulungu ndi chakuti mudziwe chifuniro chake:

**Cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani. (Aefeso 5:17)**

Kuzindikira mau a Mulungu kumathandiza kuti tidziwe chifuniro chake pamene akutiyanhula. Kuphunzira kulandira chitsogozo cha Mulungu ndi chimodzimodzi kuphunzira kuyenda ndi Mulungu nthawi zonse. Baibulo limafotokoza kuti:

**Koma Iye anayankha nati, Kwalembedwa, Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mau onse akuturuka m'kamwa mwa Mulungu. (Mateyu 4:4)**

Mau oti “otuluka” amatanthauza chinthu chimene chinachitika kale, chimene chikuchitika pakadali pano ndipo chidzapitilirabe kuchitika mtsogolo. Mulungu amayankhula ndi cholinga choti awonetsere chifuniro chake kwa munthu. Ichi ndi chifukwa chake chili chinthu chofunika kuzindikira kuyankhula kwa Mulungu.

## **MULUNGU AKAYANKHULA**

Pali mau awiri achioleni amene amatanthauza kuti “mau.” Mau awiri amenewa ndi “logos” ndi “rhema.” “Logos” ndi mau a Mulungu olembedwa pamene “rhema ndi mau amoyo kapena opatsa moyo a Mulungu. Izi zinafotokozeredwa kwa okhulupirira aku Bereya

**Amenewa anali mfulu koposa a m'Tesalonika, popeza analandira mau ndi kufunitsa kwa mtima wonse, nasanthula m'malembo masiku onse, ngati zinthu zinali zotero. (Macitidwe 17:11)**

Vesi iyi ikuonetsera ubale wa “logos” ndi “rhema” Logos kapena kuti mau a Mulungu olembedwa amagwirizana ndi “rhema” kapena mau opatsa moyo. Iyi ndi njira imene mungadziwire kuti mau amene mukumvawo akuchokera kwa Mulungu. “Rhema” mau ochokera kwa Mulungu ndipo amakhala ogwirizana ndi nyengo zathu komanso amakumana ndi zosowa zathu ndikupereka chitsogozo pa moyo wathu. Pamene mwazindikira kuti mau a Mulungu akuyankhula ku nyengo zanu, mauwo amakhala opereka moyo.

Mau a “rhema” akhoza kuperekedwa kudzera mu ulaliki, kapena vesi ya Mu baibulo imene tanthauzo lake lakupatsani chidwi kwambiri. Mau amenewa akhoza kuyankhulidwa kwa inu kudzera mphatso zauzimu. Mauwa akhozanso kuyankhulidwa mkati mwamzimu wanu ndi Mulungu. (muphunzira zambiri zokhudza mmene Mulungu amayankhulira pogwiritsa ntchito mphatso zauzimu mu chaputala chapatsogolo).

Koma muyenera kudziwa kuti mau a “rhema” kapena kuti olankhulidwa nthawi zonse amagwirizana ndi mau olembedwa a Mulungu. Mau olembedwa a Mulungu ndi athunthu kapena kuti ndi achikwanekwane. Palibe chimene chiyenera kuchotsedwa kapena kuonjezedwa (Chibvumbulutso 22: 18-19). Pamene Mulungu wayankhula kudzera m' mau a “rhema,” nthawi zonse mauwa amagwirizana ndi mau ake olembedwa.

## MITUNDI YA ANTHU OMVERA

Baibulo limakamba za magulu awiri a anthu pakumva mau:

**Cifukwa cimeneci yense amene akamva mau anga amenewa, ndi kuwacita, ndidzamfanizira iye ndi munthu wocenjera, amene anamanga nyumba yace pathanthwe; ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo, zinagunda pa nyumbayo; koma siinagwa; cifukwa inakhazikika pathanthwepo. Ndipo yense akamva mau anga amenewa, ndi kusawacita, adzafanizidwa ndi munthu wopusa, yemwe anamanga nyumba yace pamcenga; (Mateyu 7:24-26)**

Wakumva mau opusa ndi amene amangomva mau koma osachitapo kanthu. Pamene munthu wakumva mau ochenjera ndi amene amamva mau ndikuchitapo kanthu. Wina wongomva chabe pamene wina ndi wakumva ndi kuchita komwe.

Simukuyenera kungodziwa mau a Mulungu okha ayi, koma muyenera kuphunzira kumvera zimene mau akufototozoza.

**Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha. Pakuti ngati munthu ali wakumva mau wosati wakucita, iyeyu afanana ndi munthu wakuyang'anira nkhope yace ya cibadwidwe cace m'kalirole; pakuti wadziyang'anira yekha nacoka, naiwala pompaja nali wotani. Koma iye wakupenyereera m'lamulo langwiwo, ndilo laufulu, natero cipenyereera, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakucita nchito, adzakhala wodala m'kucita kwace. (Yakobo 1:22-25)**

Yesu anafotokozeranso za mitundu ya anthu akumva mau pogwiritsa ntchito fanizo la ofesa amene anafesa mbeu zake pa dothi losiyanasiyana. Iye anafananitsa mitundu ya dothi losiyanasiyana ndi mmene anthu osiyanasiyana amachititira akamva mau a Mulungu.

### **MBEU YOGWERA M'MBALI MWANJIRA:**

Mbeu zimene zinagwera m'mbali mwanjira zinatoledwa ndi mbalame kotero kuti sizinamere. Ichi ndi chitsanzo cha munthu amene amamva mau a Mulungu koma sakhazikika mkati mwake. Satana amabwera ndikuwalanda mauwo.

### **MBEU YOGWERA PAMWALA.**

Mbeu imene inagwera pa mwala inamera mwachangu koma dzuwa litaomba, mbeuyi inauma chifukwa inalibe mizu. Ichi ndi chitsanzo cha anthu amene amamva mau a Mulungu ndi

kuwalandira mwansangala. Koma mauwa sakhazikika mwa iwo pamene zinthu zayamba kulimba pamoyo wao.

### **MBEU YOGWERA PA MINGA:**

Njere zimene zinagwera pa minga zinatsamwidwa ndi mingazo. Ichi ndi chitsanzo cha anthu amene amamva mau a Mulungu koma mauwo amatsamwidwa chifukwa chosamala zinthu za dziko lapansi ndi zakuthupi.

### **MBEU YOGWERA PA NTHAKA YA CHONDE:**

Mbeu ina inagwera pa nthaka yachonde ndipo zotsatira zake zinali zokolora zambiri. Ichi ndi chitsanzo cha anthu amene amawandira mau a Mulungu ndi kukhazika pa mau amenewa. Munthu ameneyu amakula muuzimu komanso ndi kubala zipatso.

### **KODI MUNGADZIWE BANJI MAU A MULUNGU**

Kodi mukufuna kukhala ndikuthekera kozindikira mau a Mulungu komanso chifuniro chake? Mu chaputala chikubwerachi, muphunzira zinthu zimene zimamuyenereza munthu kuti amve mau a Mulungu ndi kuzindikira chifuniro chake.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

---

---

2. Kodi mau oti “rhema amatanthauza chiani?”

---

---

3. Kodi mau oti “logos” amatanthauza chiani?

---

---

4. Kodi kuzindikira mau a Mulungu kumagwirizana bwanji ndi kuchita chifuniro chake?

---

---

5. Perekani umboni opezeka ku buku la Ahebri umene ukuonetsa kuti Mulungu anayankhula ndi anthu kalero ndipo akuyankhulabe ndi munthu lero lino

6. Kodi chifuniro cha Mulungu ndi chiani?

---

7. Kodi “rhema” kapena mau a Mulungu amagwirizana ndi chiani?

---

8. Kodi chinamulekanitsa munthu pamaso pa Mulungu ndi chiani?

---

9. Muyenera kukhala munthu \_\_\_\_\_ osati \_\_\_\_\_ kokha.

(mayankho amafunso awa akupezeka kumapeto kwa buku ili)



## ZOWONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pali ma vesi angapo mu Baibulo amene amafotokoza za mau a Mulungu. Werengani ndime zili munsimu ndipo fotokozani mau amene akufotokoza kuyankhula kwa Mulungu. Vesi yoyamba yaperekedwa ngati chitsanzo choti inu mutsatire. Ndipo mukuwerenga kwanu kwa Baibulo, mukhoza kuonjezera ma vesi ena ndi zimene zikufotokozeredwa pa ndime zimenezi

### VESI KUFOTOKOZERA KWA MAU A MULUNGU

II Samueli 22:14 Chiphaliwari chakumwamba

I Mafumu 19:12-13

Salimo 18:1

Salimo 29:3-9

Salimo 68:33

Danieli 10:6-9

2. Mulungu anayankhula zokhudza Yesu. Mukhoza kupeza zimene anayankhula mu ndime izi:  
II Petro

1:17-18; Mateyu 3:17; Marko 1:1.

3. Zimene Mulungu amayankhula zimakwanilitsidwa. Werengani Ezeieli 12:25-28.
4. Werengani mau a Yesu mu mabuku a Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane. Ndipo onani mmene Yesu amayankhira mafunso, kufunsira mafunso, kufotokoza mafanizo komanso kulalikira kwake.
5. Mulungu samangoyankhula kwa anthu okha, amayankhulanso kwa mafuko. Werengani Yermiah 18:7-10.
6. Werengani zotsatira zosamvera mau a Mulungu mu ndime zili pansizi.

### Vesi

### Zotsatira Zakusamvera

Ekisodo 15:26

Deteronome 28:15-68

I Samueli 12:15

7. Werengani ndime zili munsimu ndipo lembani zotsatira zakumvera Mulungu.

Deteronome 28:1-14: \_\_\_\_\_

I Samueli 12:14: \_\_\_\_\_

8. Baibulo lonse limaonetsera mmene anthu ndi mafuko anachitira atamva mau kapena kuyankhula kwa Mulungu. Malizitsani m'ndandanda uli munsiwu powonetsera mmene munthu anachitira atamva Mau a Mulungu. Vesi yoyamba yaperekedwa ngati chitsanzo choti mutsate. Ndikofunika kuti muwerenge ma vesi aperekedwawo musanamalizitse mndandanda uli munsiwu. Ndipo mukhoza kuonjezera ndime kapena ma vesi ena amene mwapeza nokha mu Baibulo.

<b>Vesi</b>	<b>Munthu</b>	<b>Yankho</b>	<b>Zotsatira</b>
Genesis 26:5 adziko lapansi	Abraham	Anamvera	Mbeu yake ndi mafuko onse
			Anadalalitsidwa

Genesis 22:18

Deteronome 8:20

Oweruza 2:2,4,20-23

Oweruza 6:10

I Samueli 15:1,19,22,24

I Samueli 28:18

Salimo 106:25

Yeremiya 32:23

Danieli 9:10-14

Zefaniya 3:2

Hagai 1:12

## CHAPUTALA 2

### “NGATI MUNTHU WINA ACHITA.... ADZAZINDIKIRA”

#### ZOLINGA

Pamapeto pamaphunziro awa muyenera kukwaniritsa zinthu izi.

- Kulemba vesi Yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “choyenera”
- Kutchula zinthu zoyenera kudziwa mau a Mulungu.
- Kufotokoza tanthauzo la kubadwa mwatsopano.
- Kuzindikira kufunika kwa Mzimu Woyera pakuzindikira mau a Mulungu.
- Kuonetsera kukhwima ndi kusinthika muuzimu.

#### MA VESI OTSOGOLERA

**Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiwo.**  
(Aroma 12:1-2)

#### MAU OYAMBA

Pali zinthu zoyenera zofunika kuti munthu akazindikire mau a Mulungu. Mau oti choyenera amatanthauza chinthu chimene muyenera kuchita musanachite chinthu china. Kapena kuti ndi chinthu chimene chimafunika kuti mukwaniritse cholinga chinachake.

Cholinga chanu mu phunziro ili ndi chakuti mukazindikire mau a Mulungu. Ndipo chaputalachi chikufotokozera zinthu zokuyenerezani kuti mukwanilitse cholinga chimenechi. Yesu anati:

**Ngati munthu ali yense afuna kucita cifuniro cace, adzazindikira za ciphunzitsoco, ngati cicokera kwa Mulungu, kapena ndilankhula zocokera kwa Ine ndekha.**  
(Yohane 7:17)

Vesi Yotsogolera mu chaputala ichi ndi Aroma 12:1-2 ndipo imafotokoza zinthu zimene Mulungu amafuna kuti muchite. Ngati mungakwaniritse zoyenera zimenezi, ndiye kuti mwakwaniritsa kudziwa kapena kuzindikira mau a Mulungu ndi chifuniro chake pa moyo wanu.

## KUBADWA MWATSOPANO

**Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. (Aroma 12:1)**

Monga mwaphunzira mu chaputala chapitachi, tchimo limamulekanitsa munthu pa maso pa Mulungu. chifukwa cha tchimo, zimakhala zovuta kuti mukamve kuyankhula kwa Mulungu ndi kuchitapo kanthu moyenera.

Ku dziko lakuthupi kumakhala kovuta kuti mukazindikire mau a munthu wa chilendo. Kumakhala kosavuta kuzindikira mau a anthu amene muli nao paubale. Iziso ndi chimodzimidzi ku dziko lauzimu. Kuti mukazindikire mau a Mulungu muyenera kumudziwa kaye Mulungu ndipo simungakhale ndi ubale ndi Mulungu ngati mukhalabe mu uchimo.

**Akutifunsa ife kuti tisendere kwa Mulungu popereka moyo wathu kwa (Aroma 12:1).**

Iye Mulungu anayankhula kale kudzera m' mau ake olembedwa ndipo iye waonetseranso chifuniro chake ndi cholinga choti tikhale naye paubale.

**Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)**

Sicholinga cha Mulugu kuti moyo wanu onse mukhale mu uchimo. Cholinga Chake ndi chakuti muyende malinga ndi cholinga chake.:

**kuti nthawi yotsalira simukakhalenso ndi moyo m'thupi kutsata zilakolako za anthu, koma cifuniro ca Mulungu. (1 Petro 4:2)**

Mulungu akuonetsedwa atayima pakhomo la moyo wanu ndi cholinga choti akhale nanu paubale:

**Taona, ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine. (Cibvumbulutso 3:20)**

Cholinga cha Mulungu kuchokera pachiyambi cha dziko ndi chakuti akamudziwe Yesu:

**Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)**

Munasonkhanitsidwa mwa khristu pokhala gawo limodzi la banja la Mulungu. Chimodzimodzi mmene munthu amabadwira kuthupi, chomwechonso munabadwanso mwatsopano muuzimu mu banja lauzimu la Mulungu.

Werengani Yohane chaputala 3. Chaputala ichi chimafotokoza mwatsatanetsatane tanthauzo lakukhala obadwa mwatsopano. Kuti mubadwe mwatsopano, muyenera kuchita zinthu izi:

1. Kubvomereza kuti ndinu munthu ochimwa.

**Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu; (Aroma 3:23)**

2. Kuzindikira kuti chilango cha tchimo ndi imfa.

Mulungu anachenjeza Adamu ndi Hava kuti akadzangochimwa adzafa ndithu. Izi zimatanthauza imfa yauzimu (imene ili kulekanitsidwa kwa munthu pamaso pa Mulungu) komanso imfa yakuthupi. Pamene Yesu amafa pamtanda paja, iye anafa mmalo mwa ife kapena kuti anafera machimo athu ndikuti tikhale nawo moyo wasatha.

**Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 6:23)**

Ngati mungavomereze msembe Yake yamachimo anu, ndiye kuti simulonso panso pa chilango cha imfa.

3. Muyenera kuvomereza machimo anu, kulapa ndi kukhulupirira kuti anafera machimo anu:

**Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutsambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:8-9)**

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. (Yohane 3:16)**

Pamene mwapereka moyo wanu kwa Mulungu, mumabadwanso mwatsopano.

**Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano. (2 Akorinto 5:17)**

Pamene mwabadwanso mwatsopano, mumakhala mbali imodzi ya banja lauzimu la Mulungu. Si inunso olekanitsidwa pamaso pa Mulungu ayi. Angakhale mudzafa kuthupi, koma mudzakhala ndi Mulungu kwa muyaya.

Mukafika pamenepa mumakhala kuti mwakhazikitsa ubale ndi Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu. Mwamva ndi kulandira uthenga wabwino. Chifukwa cha ichi, mukhoza kukwanitsa kuphunzira kuzindikira mau a Mulungu.

**.... Yense wakukhala mwa coonadi amva mau anga. (Yohane 18:37)**

### **CHOKHALAMO CHA MZIMU OYERA**

Pali choyenerenza china chimene chingakuthandizireni kuti muzindikire mau a Mulungu. Baibulo limakamba za ubatizo wa Mzimu Woyera. Zotsatira za ubatizo wamzimu Woyera ndi chakuti, Iye amagonera mwa inu ndipo izi zimachitika kuti mukhale m'moyo wachiyero komanso oyenera pamaso pa Mulungu.

Ntchito kapena utumiki wa Mzimu Woyera pa moyo wa Munthu okhulupilira ndi ochuluka kwambiri. Chifukwa cha ichi, pali phunziro lapadera lofotokoza *Utumiki wa Mzimu Woyera*. Ndipo phunziro ili limafotokoza mmene mungalandilire ubatizo wa Mzimu Woyera.

Nchito imodzi yakudzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi yakuti zithandize okhulupirira kuchita chifuniro cha Mulungu.

**Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse; pakuti sadzalankhula za iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani. Iyeyo adzalemekeza Ine; cifukwa adzatenga za mwa Ine, nadzalalikira kwa inu. (Yohane 16:13-14)**

Baibulo limafotokoza kuti:

**Anayankha Yesu nati kwa iwo, Ndingakhale ndicita umboni wa Ine ndekha umboni wanga uli woona; cifukwa ndidziwa kumene ndinacokera ndi kumene ndimukako; koma e inu, simudziwa kumene ndicokera, ndi kumene ndimukako. (Yohane 8:14)**

Pali ubale waukulu pakati pa kubadwa mwatsopano ndi kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Munthu wakuthupi amene sanabadwe mwatsopano sangalandire chitsogozo cha mzimu Oyera. Chifukwa chakuti sanabadwe mwatsopano. Iye sangazindikire mau a Mulungu.

**Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu. (1 Akorinto 2:14)**

Zitsanzo zili munsimu zochokera mu Buku la Machitidwe zikuonetsera chitsogozo chimene Mzimu Woyera amapereka pa moyo wa okhulupirira.

### **FILIPO:**

Mkulu wampingo otchedwa Filipi anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

**Ndipo Mzimu anati kwa Filipino, Yandikira, nudziphatike ku gareta uyu. (Macitidwe 8:29)**

Filipo anamvera chitsogozo cha Mzimu Woyera ndipo izi zinabweretsa zotsatira zake zomwe zinali chipulumutso ndi ubatizo wa madzi wa mdindo wa ku Etiyopia.

### **Petro:**

Peturo anauzidwa kuti apite ndi amuna atatu ochokera ku sizareya. Peturo anati:

**Ndipo Mzimu anandiuza ndinke nao, wosasiyanitsa konse. Ndipo abale awa asanu ndi mmodzi anandiperekezanso anamuka nane; ndipo tinalowa m'nyumba ya munthuyo; (Macitidwe 11:12)**

Peturo anazindikira chitsogozo cha Mzimu Woyera. Pachiyambi anali ndi kukaika pamene mzimu anamuyankhula mkati mwa mzimu wake ndi kuonetsera chifuniro chake kwa iye. Iye anamvera ndipo zotsatira zake zinali utumiki kwa anthu amitundu.

### **PAULO:**

Paulo anasintha dongosolo la utumiki wake ndi chitsogozo cha Mzimu Woyera. Paulo anakonza kuti apite ku ..... koma Mzimu Woyera unampatsa iye kwina koti akatumikire.

Zitsanzo ziwiri zomwe zaperekedwazi ndi zochepa chabe pazitsanzo zambiri zopezeka mu Baibulo zimene zimaonetsera mmene Mzimu Woyera amathangatira kuti muzindikire mau a

Mulungu. Yesu Khristu anaonetsera kuti Mzimu Woyera amatenga chifuniro cha Mulungu ndikuchivumbulutsa kwa inu.

## **KUKHWIMA MUUZIMU**

### **Ndipo adapha ndi lupanga Yakobo mbale wa Yohane. (Macitidwe12:2)**

Ku dziko lakuthupi, mwana asanayambe kuzindikira mau amakolo ake, iye ayenera kufika mlingo wina wake wakukhwima. Izi ndi chimodzimodzi ku dziko lauzimu. Pamene mwangobadwa kumene mwatsopano, zimakhala zovuta kuti muthe kuzindikira mau a Mulungu pamene akuyankhula ndi inu. Ndipo pamene mwalandira Mzimu Woyera, simungathe kumvetsa zonse zimene Mulungu akuonetsera. Koma pamene mukukula muuzimu, mumayamba kuzindikira mau a Mulungu mkati mwa mzimu wanu.

Baibulo limaotsera kufanana kwa zinthu zauzimu ndi zakuthupi:

**Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda. Koma cakudya cotafuna ciri ca anthu akulu misinkhu, amene mwa kucita nazo anazoloweretsa zizindikiritso zao kusiyanitsa cabwino ndi coipa. (Ahebri 5:13-14)**

Mkaka ndi nyama zimene zikufotokozeredwa apazi zikuimira mau a Mulungu olembedwa, Buku lopatulika. Pamene mwabadwa kumene mwatsopano, mumayamba kuphunzira mfundo zing'onozing'ono za choonadi (mkaka) cha mau a Mulungu olembedwa. Ndipo pamene mukukula muuzimu, mumayamba kumvetsa mfundo zikuluzikulu (nyama) za choonadi cha Mau a Mulungu.

Pamene mukupitiriza kuwerenga mau a Mulungu olembedwa, kumvetsetsa kwanu kwa mau kumakula. Mumayamba kugwiritsa ntchito mau a Mulungu pozindikira chabwino ndi choipa. Izi zikutanthauza kuti mumatha kuzindikira chifuniro cha Mulungu ndi njira zake komanso ndikusiyantsa njira zake ndi zinthu zosayenera. Ichi ndi chifukwa chake ndizofunika kuti muziwerenga mau a Mulungu.

Pamene mukukula muuzimu, simumafanizidwanso ndi dziko lapansi. Kufanizidwa ndi dziko lapansi kumatanthauza kuchita zinthu molingana ndi dziko lapansi. Kukhwima muuzimu kumakuthandizani kuti mufanizidwe ndi chifaniziro cha Khristu Yesu osati chifaniziro cha dziko lapansi. Komanso kukula muuzimu kumathandiza kuti mukule munzeru ndipo izi zimathandiza kuti muzipanga ziganizo zoyenera.



Kukula muuzimu kumathandizanso kuti mubale zipatso za Mzimu Woyera. Ndipo zipatso za Mzimu Woyera zoonetsera kukulu muuzimu ndi izi:

### **KUSANDULIKA**

**.... koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:2)**

Kukula muuzimu kumabweretsa kusandulika, ndipo ichi ndi chinthu chimodzi chimene chimathandiza kuzindikira mau a Mulungu. Zimene thupi lathu limalakalaka kuchita ndi zimene Mulungu akhumba kuti tichite zimakhala zosiyana. Chifukwa cha ichi, pamakhala kulimbana pakati pa mzimu ndi thupi.

Paulo anafotokozera za kulimbana kumeneku:

**Pakuti thupi lilakalaka potsutsana naye Mzimu, ndi Mzimu potsutsana nalo thupi; pakuti izi sizilingana; kuti zimene muzifuna musazicite. (Agalatiya 5:17)**

Paulo akuzindikira kuti pali kulimbana pakati pa Mzimu ndi thupi pa nkhani yokwaniritsa chifuniro cha Mulungu. Ndipo nkondo imeneyi ndi ya mmaganizo:

**koma ndiona lamulo lina m'ziwalo zanga, lirikulimbana ndi lamulo la mtima wanga, ndi kundigonjetsa kapolo wa lamulo la m'ziwalo zanga. (Aroma 7:23 )**

Chifukwa cha ichi, iye akudandaulira:

**Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:1-2)**

Mau oti “ndikupemphani” amatanthauza kudandaulira. Ndipo mau oti “kupereka matupi anu ngati nsembe yamoyo” amaonetsera kudzipereka kwa Mulungu mosadukiza.

Kupereka kanthu ngati nsembe kumatanthauza kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu. Mu Chipangano chakale nsembe ikaperekedwa, imaperekedwa yonse kwa Mulungu kuti iwotchedwe

ndi moto, idyedwe ndi ansebe molingana ndi chilamulo. Ndipo panalibe chilichonse chimene opereka nsembeyo amatengapo chifukwa panalibe chake.

Chimodzimidzi nafenso, kudzipereka kwathu kwa Mulungu kuyenera kukhala kwathunthu. Munthu wakaleyo ayenera kufa. Izizi ndi zimene zimatanthauza tikakamba za kusandulika. Kusandulika ndi kusintha ndi kukhala molingana ndi chifaniziro cholingana ndi ambuye wathu Yesu Khristu.

**Ndinapacikidwa ndi Kristu; (Agalatiya 2:20)**

**Koma iwo a Kristu Yesu adapacika thupi, ndi zokhumba zace, ndi zilakolako zace. (Agalatiya 5:24)**

**Onseamene afuna kuonekera okoma m'thupi, iwowa akukangamizani inu mudulidwe; cokhaco, cakuti angazunzike cifukwa ca mtanda wa Kristu. (Agalatiya 6:12)**

**Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okondedwa, tidzikonzere tokha kuleka codetsa conse ca thupi ndi ca mzimu, ndi kutsirfza ciyero m'kuopa Mulungu. (2 Akorinto 7:1)**

**Cotero inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu. (Aroma 6:11)**

Kupachikidwa kumene Yesu anapachikidwa sinali imfa yachilengedwe. Ndizofunika kuti munthu amfe imfa imene yaperekedwa kuti tifetse thupi lathu ndi kupachikadwa. Thupi la munthu silingafe imfa yachilengedwe komanso silingafe lokha. Thupi lanu liyenera kufa kudzera mukupachikidwa.

Molingana ndi Aroma 12:1-2, kudzipereka ndi choyenera choti tikazindikire mau a Mulungu. Ngati mukufuna kuzindikira mau a Mulungu komanso chifuniro chake, muyenera kudzipereka. Koma nthawi zambiri anthu timasemphanitsa, timafuna tidziwe kaye chifuniro chake, kenako ndikupanga chiganizo choti tidzipereke kwa Mulungu. Koma molingana ndi Aroma 12:1-2, kudzipereka ndi chinthu choyambirira.

Chifukwa chimene anthu amachita chidodo kudzipereka kwa Mulungu ndi chakuti sitimvetsa kuti chifuniro cha Mulungu ndi chabwino komanso changwiro. Timachita mantha kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu chifukwa chakuti sitinamvetsetse mfundo imeneyi.

**Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezero. (Yeremiya 29:11)**

## **KUKONZANSO MAGANIZO ANU**

Maganizo anthu amafanizidwa ndi mfundo za dziko lapansi limene mwazungulidwa nalo. Izi zimachitika chifukwa cha chikhalidwe chauchimo komanso chifukwa cha chikhalidwe chatu ngati anthu.

Koma Baibulo limafotokoza kuti tisafanizidwe ndi dziko lapansi koma tikhale osandulika, mau oti kusandulika amatanthauza kusinthika ndikukhala chifanizo chatsopano. Chifanizo chatsopano chimene muyenera kukhala ndi Khristu Yesu.

**Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyenera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzihunzi comweci kucokera kuulenerero kumka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu. (2 Akorinto 3:18)**

Molingana ndi Aroma 12:1-2, kusandulika kumabwera kudzera kukonza kwa maganizo athu. Izi zikutanthauza kuti muyenera kulekana ndi mfundo zachikunja ndikuyamba kufanizidwa ndi mfundo zimene zaonetsedwa mu mau a Mulungu.

Maganizo anu amasandulika pamene mwayamba kukhala ndi maganizo a Khristu Yesu.

Lolani kuti maganizo omwe anali mwa Yesu Mkhristu akhalenso mwa inu. (Afilipi 2:5)

Mau akuti “mukhale nao” akauonetsa kuti muyenera kupanga chiganizo kuti mukhale ndi mtima wa Khristu Yesu. Muyenera kulora kuti kusinthika kwa mtima wanu kuchitike. Izi sikuti Mulungu amangokuchitirani ayi kapena kuti sizimachitika zokha.

**Mwa ici, podzimanga m'cuuno, kunena za mtima wanu, (1 Peturo 1:13)**

Kudzimanga mtima wanu kumatanthauza kuteteza maganizidwe anu. Kuti musandulike maganizo muyenera kuzama m' mau a Mulungu. Santhulani Baibulo kuti mupeze mtima umene anali nawo Yesu. Gawo la maphunziro oonjezera likuthandizani kuti mukwanitse izi.

Mtima wanu umasandulika pamene Mulungu amaika chilamulo chake mkati mwanu.

**Ndidzapatsa malamulo anga kuwalonga m'nzeru zao, Ndipo pamtima pao ndidzawalemba iwo; (Ahebri 8:10)**

Gwiritsani mphamvu ya maganizo kuti mukalimbane ndi kugonjetsa maganizo ena onse olakwika.

**ndi kugwetsa matsutsano, ndi cokwezeka conse cimene cidzikweza pokana ddziwitso ca Mulungu, ndi kugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Kristu; (2Akorinto 10:5)**

Muli ndi udindo owongolera maganizo a moyo wanu.

**Cotsalira, abale, zinthu ziri zonse zoonza, ziri zonse zolemekezeka, ziri zonse zolungama, ziri zonse zoyera, ziri zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma; ngati kuli cokoma mtima cina, kapena citamando cina, zilingirireni izi. (Afilipi 4:8)**

Ndipo kenako mukhoza kugwirizana ndi Paulo:

**Koma tilankhula nzeru mwa angwiro; koma si nzeru ya nthawi yino ya pansi pano, kapena ya akulu a nthawi yino ya pansi pano, amene alinkuthedwa; (1 Akorinto 2:6)**

Mtima wa khritsu umakhazika pakuchita chifuniro cha Mulungu.

## **KUONETSERA CHIFUNIRO CHA MULUNGU**

Onani chithuzi chili pansichi. Chikuthandizani kuti muzindikire zoyenereza zimene zakambidwa pa Aroma 12:1-2:

Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale,  
mwa zifundo za Mulungu,  
kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo,  
yopatulika, yokondweretsa, Mulungu,  
ndiko kupembedza kwanu koyenera.

Timabwera kwa Mulungu kudzera muchifundo  
Choperekedwa ndi nsembe ya Khristu Yesu  
Mzimu Oyera amatithandizira kuti tikule muuzimu

Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe  
a panso pano: koma mukhale osandulika,  
mwa kukonzanso kwa mtima wanu,

Timasandulika ndi mau a Mulungu

Kubadwa mwatsopano, kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, kukula muuzimu, ndi kusandulika kwa mtima zimathandizira kuti mukadziwe chifuniro cha Mulungu. Malinga ndi Aroma 12 zinthu zimenezi ndi zoyenerereza kuti munthu akhale ndi chidziwitso cha chifuniro cha Mulungu.

. . . kuti mukazindikire chimene chili chifuniro cha Mulungu, chovomerezeka, choyenera ndi changwiwo. (Aroma 12:2)

Mau oti “kutsimikizika” amanthauza kukhala otsimikizika pa chinthu ndipo ichi ndi choyenera chimene chimathandiza kuti tikhale otsimikizika pa chifuniro cha Mulungu.

Koma kodi mau oti “chifuniro cha Mulungu” amanthauzani? Kodi chifuniro chabwino, changwiwo ndi chovomelezeka cha Mulungu ndi chiani? Kodi ndi chifukwa chiani muyenera kuonetsera chifuniro cha Mulungu.

Tiunguza mayankho amafunso awa mu machaputala akubwerawa.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsolera osaonera

---

---

2. Kodi mau oti choyenereza amanthauza chiani?

---

---

3. Kodi ndi zoyenereza ziti zimene zatchulidwa mu chaputala ichi zimene zimathandza kuti muzindikire chifuniro cha Mulungu?

---

4. Kodi udindo wa Mzimu Woyera ndi chiani malingana ndikuzindikira mau a Mulungu?

---

5. Kodi kubadwa mwatsopano kumatathauza chiani?

---

---

6. Kodi ndi zofunika bwanji kuti mubadwe mwatsopano ndi cholinga choti muzindikire mau a Mulungu.

---

---

7. Kodi tanthauzo lakukula kapena kukhwima muuzimu ndi chiani?

---

---

8. Kodi mau oti “kusandulika” amanthauza chiani malinga ndi chaputala ichi?

---

9. Kodi chiganizo ichi ndi cholondola kapena chasalondola: Molingana ndi Aroma 12:1-2, kudzipereka kumamuyenereza munthu kuti azindikire chifuniro cha Mulungu. Chiganizo chimenechi ndi \_\_\_\_\_

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku limeneli)

## MAPHUNZIRO OONJEZERA

1. Kuti muphunzire zambiri zokhudza kubadwa mwatsopano ndi kukula muuzimu, pezani phunziro lina la Haverstime International lotchedwa “*Maziko Achikhulupiriro.*” Ndipo kuti muphunzire zambiri zokhudza Mzimu Woyera, pezani phunziro lina lotchedwa “*Utumiki wa Mzimu Woyera*”.
2. Chaputala ichi chinakamba zakufunika kosandulika maganizo. Malemba amafotokoza kuti okhulupirira sayenera kukhala ndi mtima wotere:

Wolimba:	Danieli 5:20
wokanika:	Aroma 1:28
Athupi:	Aroma 8:6
Wokaika:	Luka 12:29
Wakhungu:	II Akorinto 3:14; 4:14
Oipsidwa:	II Akorinto 11:3
Wakuthupi:	Aefeso 2:3; Akolose 2:18
M'chitsiru cha mtima wao	Aefeso 4:17
Apadziko:	Afilipi 3:19
Olekanitsidwa ndi ntchito zoipa:	Akolose 1:21
Mitima iwiri:	Yakobo 1:8; 4:8
Odetsedwa:	Tito 1:15

3. Baibulo limafotokoza kuti okhulupira osandulika mtima ayenera kukhala:

Auzimu:	Aroma 8:6
Okonzeka:	I Petro 5:2
Owoona mtima:	II Petro 3:1
Mtima wokhazikika:	Yesaya 26:3
Amtendere:	Afilipo 4:7
Kusandulika:	Aefeso 4:23
Odzichepetsa:	Akolose 3:12
Makhalidwe oyenera:	Tito 2:6
Okhazikika:	II Timoteyo 1:7
Okonda:	Mateyu 22:37
Otumikira:	Romans 7:25
Ogwirizana:	I Petro 3:8; 4:1; Aroma 15:6; I Akorinto 1:10
Okhulupirira ndi akonzeka:	I Mbiri 28:9
Ophunzitsidwa kugwira ntchito:	Nehemia 4:6

## CHAPUTALA 3

### CHIFUNIRO CHA MULUNGU

#### ZOLINGA

Pamapeto pamaphunziro amenewa muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la chifuniro.
- Kuzindikira mitundu itatu yachifuniro imene imagwira ntchito pa dziko lapansi.
- Kufotokoza tanthauzo la chifuniro cha Mulungu.
- Kupeza zolinga zoyenera zochitira chifuniro cha Mulungu.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 6:38)**

#### MAU OYAMBA

Chaputala ichi chifotokozera mitundu iwiri yachifuniro imene imagwira ntchito pa dziko lapansi. Komanso tifotokozera tanthauzo la mau oti “chifuniro cha Mulungu,” kuunikira moyo wa khristu Yesu molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Pomaliza, tiona kufunika kwa chifuniro cha Mulungu.

#### TANTHAUZO LA CHIFUNIRO

Tanthauzo la chifuniro ndi kuthekera kopanga chiganizo kapena kuti mphamvu yotha kupanga chisankho. Pali mitundu itatu ya chifuniro imene imagwira ntchito pa dziko lapansi:

#### CHIFUNIRO CHA IWE MWINI:

Ichi ndi chifuniro cha munthu, kapena kuti chikhalidwe cha iwe mwini chimene chimafuna kupanga zimene iwe mwini ukufuna. Ngati moyo wanu umatsogozedwa ndi chifuniro chanu, mumapanga ziganizo zanu molingana ndi mmene inuyo mukufunira osati mmene Mulungu akufunira.

**Inu Yehova, ndidziwa kuti njira ya munthu siri mwa iye mwini; sikuli kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ace. (Yeremiya 10:23)**



Chifuniro cha iwe mwini chimagwira ntchito kwa munthu wakuthupi:

**kama makamaka iwo akutsata zathupi, m'cilakolako ca zodetsa, napeputsa cilamuliro; osaopa kanthu, otsata cifuniro ca iwo eni, santhunthumira kucitira mwano akulu; (2 Petro 2:10).**

Baibulo limafotokoza zotsatira za chifuniro cha iwe mwini:

**Potero ndinawaperekera kuuma mtima kwao, Ayende monga mwa uphungu wao wao. (Masalmo 81:12)**

Uchimo, kusautsika ndi mavuto pa dziko lapansi ndi zotsatira za munthu okhala moyo osamvera Mulungu. Davite anafotokoza kuti chifuniro cha iwe mwini chimagwira ntchito mmoyo wa anthu oipa.

**Musandipereke ku cifuniro ca akundisautsa; Cifukwa zinandiukira mboni zonama ndi iwo akupumira zaciwawa. (Masalmo 27:12)**

Baibulo limafotokoza kuti atsogoleri a mpingo sayenera kukhala a chifuniro cha iwo:

**Pakuti woyang'anira ayenera kukhala wopanda cirema, ngati mdindo wa Mulungu; wosati waliuma, wosapsa mtima msanga, wosati waciwawa, wopanda ndeu, wosati wa cisiriro conyansa; (Tito 1:7)**

### **CHIFUNIRO CHA SATANA:**

Satana nayenso ali ndi chifuniro ndipo iye chokhumba chake ndi chakuti awononge chilichonse chabwino chili mwa inu. Yesu anachenjeza Peturo za izi:

**Simoni, Simoni, taona, Satana anafunsa akutengeni kuti akupeteni ngati tirigu (Luka 22:31)**

Cholinga cha Satana ndi kutenga zonse zabwino zimene zili mwa inu: Yesu anati:

**Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)**

Paulo akufotokoza kuti okhulupirira ena ndi omangidwa ndi chifuniro cha Satana:

**Ndipo akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace. (2 Timoteo 2:26)**

### **CHIFUNIRO CHA MULUNGU:**

Chifuniro chachitatu chimene chimagwira ntchito pa dziko lapansi ndi chifuniro cha Mulungu ndipo izi ndi zimene tikukambirana muphunziro limeli.

### **TANTHAUZO LA CHIFUNIRO CHA MULUNGU**

Chipangano chatsopano chinalembedwa muchiyankhulo cha chiheleni. Ndipo mu chiheleni, pali mau awiri amene amatanthauza “chifuniro” molingana ndi chifuniro cha Mulungu.

Amodzi mwa mau amenewa ndi “boulema.” Ichi ndi chifuniro cha “iye yekha” Mulungu. Ichi ndi chikonzero cha Mulungu pa chinthu chilichonse chimene chimachitika pa dziko lapansi. Chifuniro ichi chimakwaniritsidwa posayang’anira chiganizo chilichonse chopangidwa ndi munthu. Ndi dongosolo lonse la dziko lapansi.

Chifuniro cha “boulema” sichimatengera kutengapo mbali kulikonse kwa munthu ndipo zotsatira zake zimakhala kuti zinakhazikitsikidwa kale. Chifuniro cha “baulema” cha Mulungu chinalembedwa mu Malemba ndipo ndi chomveka mwachindunji. Sikumakhala kofunika kofunafuna chifuniro chimenechi chifukwa chinavumbulutsidwa kale mu Baibulo.

Mau ena ndi otchedwa “thelema” chimene chili chikhumbokhumbo cha Mulungu kuti Munthu akhale molingana ndi chifuniro cha Mulungu kapena kuti chikonzero cha Mulungu pa munthu wina aliyense. Kutu Mulungu akwaniritse chifuniro chake cha “thelema” zimafunika kuti inuyo muchitepo kanthu. Muli ndi mwayi osankha kuyenda muchifuniro cha Mulungu chimenechi kapena ayi ndipo chifuniro cha “thelema” ndichimene timanena tikamakamba za kufunafuna kwa chifuniro cha Mulungu”

Chifuniro china cha Mulungu chimatchedwa “moral.” Ichi ndi chifuniro chimene chimaonetsa mmene okhulupirira ayenera kukhalira molingana ndi mau a Mulungu. Chifuniro cha Mulungu ndi cha munthu sichimasemphana ndi chifuniro cha mmene munthu ayenera kukhalira molingana ndi Baibulo. Chithuzi chili munsimu chikufotokozerana matanthauzo osiyanasiyana a chifuniro cha Mulungu.

<b>“Chifuniro cha iye yekha” (boulema)</b>	<b>Chifuniro chake pa munthu (Thelema)</b>	<b>moral(chikhalidwe)</b>
Chikonzero cha Mulungu Cha dziko lonse lapansi	dongosolo lonse la Mulungu pa munthu wina aliyese	malamulo a Mulungu olembedwa m’Baibulo amene amaphunzitsa Mmene tikuyenera kukhalira komanso mmene tiyenera kukhulupirira
Sichimakhudzidwa ndi ziganizo Zopanga munthu makhalidwe	chimakhudzidwa ndi ziganizo zopanga munthu	chifuniro cha pa munthu cha Mulungu ndi chogwirizana ndi chifuniro chake cha

## YESU NDI CHIFUNIRO CHA MULUNGU

Kuchita chifuniro cha Mulungu chinali cholinga chachikulu mu utumiki wa Yesu Khristu. Iye analengeza:

**Koma cifuniro ca Iye amene anandituma Ine ndi ici, kuti za ici conse Iye anandipatsa Ine ndisatayeko kanthu, koma ndiciukitse tsiku lomariza. (Yohane 6:39)**

Chifuniro cha Mulungu ndi chakuti anthu onse akhale pa ubwenzi woyenera ndi Iye.

**Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 6:38)**

**Pakuti cifuniro ca Atate wanga ndi ici, kuti yense wakuyang'ana Mwana, ndi kukhulupirira iye, akhale nao moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomariza. (Yohane 6:40)**

Cholinga cha moyo wa Khristu chinali kukwalitsa chifuniro cha Mulungu. Angakhale Yesu ali mwana, iye cholinga chake chinali kukwanilitsa chifuniro cha Mulungu. Pamene makolo ake anali kumuyang'anayang'ana atapita kukachisi, iye anati:

**Ndipo iye anati kwa iwo, Kuli bwanji kuti munalikundifunafuna Ine? Simunadziwa kodi kuti kundiyenera Ine 5 ndikhale m'zace za Atate wanga? (Luka 2:49)**

Chinsinsi cha mphamvu zake zauzimu chinali kuchita chifuniro cha Mulungu:

**Yesu ananena nao, Cakudya canga ndico kuti ndicite cifuniro ca iye amene anandituma Ine, ndi kutsiriza nchito yace. (Yohane 4:34)**

Ndime imeneyi ikuonetsera chikhumbokhumbo chake chofuna kumalizitsa ntchito ya Mulungu kudzera mu utumiki ndi moyo wake.

Mphamvu imene imaonekera mu utumiki wa khristu Yesu inali yogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu:

**Sindikhoza kucita kanthu kwa Ine ndekha; monga momwe ndimva ndiweruza; ndipo maweruzidwe anga ali olungama; cifukwa kuti sinditsata cifuniro canga, koma cifuniro ca Iye ondituma Ine. (Yohane 5:30)**

Mau a Khristu ndi zochitika zake sizinali zake. Iye amayankhula ndi kuchita zinthu molingana ndi chifuniro cha Mulungu.

**Pamenepo Yesu anayankha iwo, nati, Ciphunzitso canga siciri canga, koma ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 7:16)**

**Wosandikonda Ine sasunga mau anga; ndipo 1 mau amene mumva sali mau anga, koma a Atate wondituma Ine. (Yohane 14:24)**

**Cifukwa cace Yesu anati, Pamene mutadzamkweza Mwana wa munthu, pomwepo mudzazindikira kuti Ine ndine, ndipo sindicita kanthu kwa Ine ndekha, koma monga anandiphunzitsa Atate, ndilankhula izi. (Yohane 8:28)**

**Sindikhoza kucita kanthu kwa Ine ndekha; monga momwe ndimva ndiweruza; ndipo maweruzidwe anga ali olungama; cifukwa kuti sinditsata cifuniro canga, koma cifuniro ca Iye ondituma Ine. (Yohane 5:30)**

Angakhale Yesu amayembekezera imfa yake pakupachikidwa.

**Ndipo anamuka patsogolo pang'ono, nagwa nkhope yace pansi, napemphera, nati, Atate, ngati nkutheka, cikho ici cindipitirire Ine; koma si monga ndifuna Ine, koma lou. (Mateyu 26:39)**

Yesu Khristu anali okonzeka kufa chifukwa chinali chifuniro cha Mulungu. chifukwa cha ichi, moyo wa Yesu ndi chitsanzo chabwino chochita zinthu molingana ndi chifuniro cha Mulungu mu magawo onse a moyo wake.

## **KUFUNIKA KWA CHIFUNIRO CHA MULUNGU**

Chifuniro cha Mulungu ndi chofunika motere:

### **CHIMAOANETSERA TSOGOLO LANU LA MOYO WAMUYAYA.**

Mapeto amoyo wanu umatengera chifuniro cha Mulungu kotero muyenera kuvomerezana ndi chifuniro cha Mulungu moyenera kuti moyo wanu upulumutsidwe...

**Pakuti cipata ciri copapatiza, ndi icepetsa njirayo yakumuka nayo kumoyo, ndimo akucipeza cimeneco ali owerengeka. (Mateyu 7:14)**

**Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. (Mateyu 7:21)**

**Ndipo dziko lapansi lipita, ndi cilakolako cace; koma iye amene acita cifuniro ca Mulungu akhala ku nthawi yonse. (1 Yohane 2:17)**

### **NDI MAZIKO A UBALE WANU NDI MULUNGU.**

**Ubale wathu ndi Yesu wakhazikika pakuchita chifuniro chake”**

**Buku Lopatulika 1992 Marko 3:35 Pakuti ali yense acita cifuniro ca Mulungu, yemweyo ndiye mbale wanga, ndi mlongo, ndi amai.**

### **CHIMAPEREKA CHITSOGOZO:**

Chifuniro cha Mulungu ndi chofunika kwambiri chifukwa simungathe kuyendetsa moyo wanu panokha.

**Inu Yehova, ndidziwa kuti njira ya munthu siri mwa iye mwini; sikuli kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ace. (Yeremiya 10:23)**

Munthu alibe kuthekera koyendetsa moyo wake pa iye yekha. Popanda chitsogozo cha Mulungu, munthu amasemphana ndi chikonzero cha Mulungu.

**Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse. (Yesaya 53:6)**

### **CHIMAPEREKA CHIDZIWITSO CHA TSOGOLO**

Ndi Mulungu yekha amene amadziwa zinthu zamtsogolo. Iye amadziwa misampha imene satana waikiza, mmene chuma chadziko chiyendere angakhale ndale zimene. Amadziwanso zinthu zimene mudzakumane nazo mtsogolo.

Kumbukirani zinthu zoyamba zakale, kuti Ine ndine Mulungu, ndipo palibenso wina; Ine ndine Yehova, ndipo palibenso wina wofana ndi Ine; ndilalikira za cimariziro kuyambira paciyambi, ndi kuyambira nthawi zakale ndinena zinthu zimene zisanacidwe; ndi kunena, Uphungu wanga udzakhala, ndipo ndidzacita zofuna zanga zonse; (Yesaya 46:9-10)

Munthu amangodziwa zinthu za nthawi yatsopano komanso ndi kukumbukira zimene zinachitika kale. Iye amathanso kukonzekera zinthu zamtsogolo, koma ndi Mulungu yekha amene ali ndi chidziwitso cha zimene zidzachitike mtsogolo.

Anthu ena amaona ngati Satana ali ndi chidziwitso cha zinthu zamtsogolo. Izi zikanakhala choncho, iye sakanakonza zoti Yesu apachikidwe. Iye akanatha kuona zamtsogolo kuti kudzera mu imfa ndi kupachikidwa kwa Yesu, chipulumutso kuchimo chidzaperekedwa kwa munthu. Satana amadziwa zinthu zokhazo zimene Mulungu wazionetsera zokhudza tsogolo. Mwachitsanzo, iye anadziwa kuti chimaliziro chake ndi Gahena chifukwa Mulungu izi anazionetseratu kale.

### **NDI LAMULO KUTI TICHIDZIWE**

Kudziwa chifuniro cha Mulungu ndikofunika chifukwa ndi chilamulo kuti tichidziwe ndikuchita:

**Cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani. (Aefeso 5:17)**

**Si monga mwa ukapolo wa pamaso, monga okondweretsa anthu, komatu monga akapolo a Kristu, akucita cifuniro ca Mulungu cocokera kumtima; (Aefeso 6:6)**

Mulungu amafuna kuti tizimvera chifuniro chake kuposa msembe kapena matamando kwa Iye:

**Ndipo Samueli anati, Kodi Yehova akondwera ndi nsembe zopsereza ndi nsembe zophera, monga ndi kumvera mau a Yehova? Taonani, kumvera ndiko kokoma koposa nsembe, kuchera khutu koposa mafuta a nkhosa zamphongo, Pakuti kupanduka kuli ngati coipa ca kucita nyanga, ndi mtima waliuma uli ngati kupembedza milungu yacabe ndi maula. Popeza inu munakaniza mau a Yehova, Iyenso anakaniza inu, kuti simudzakhalanso mfumu. (1 Samueli 15:22-23)**

Mulungu akufuna kuti tikhale angwiro ndi athunthu pakuchita chifuniro chake:

**Akulankhulani inu Epafra ndiye wa kwa inu ndiye kapolo wa Yesu Kristu, wakulimbira cifukwa ca inu m'mapemphero ace znasiku onse, kuti mukaima amphumphu ndi odzazidwa m'cifuniro conse ca Mulungu. (Akolose 4:12)**

## **CHIMWABWERETSA CHIPHUNZITSO CHOYENERA:**

Yesu anati:

**Ngati munthu ali yense afuna kucita cifuniro cace, adzazindikira za ciphunzitsoco, ngati cicokera kwa Mulungu, kapena ndilankhula zocokera kwa Ine ndekha. (Yohane 7:17)**

Ngati mumachita chifuniro cha Mulungu, izi zimathandizira kuti mukakule muuzimu ndikutha kukwanitsa kuzindikira chiphunzitso choyenera. Ndipo izi zimathandiza kuti musanyengeke ndi chiphunzitso chabodza.

## **CHIMABWERETSA KUYANKHIDWA KWA MAPEPHERO:**

Pamene mukukhala molingana ndi chifuniro cha Mulungu, mumakhala nako kulimbika mtima kuti mukhoza kupemphera ndikuyankhidwa zopempha zanu.

**Ndipo cimene ciri conse tipempha, tilandira kwa iye, cifukwa tisunga malamulo ace, ndipo ticita zomkondweretsa pamaso pace. (1 Yohane 3:22)**

**Tidziwa kuti Mulungu samvera ocimwa. Koma ngati munthu ali yense akhala wopembedza Mulungu nacita cifuniro cace, amvera ameneyo. (Yohane 9:31)**

**Ndipo uku ndi kulimbika mrima kumene tiri nako kwa iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa cifuniro cace, atimvera; (1 Yohane 5:14)**

## **CHIMABWERETSA MADALITSO AUZIMU:**

Pali malonjezano amadalitso auzimu ngati muchita chifuniro cha Mulungu:

**Pakuti cikusowani cipiriro, kuti pamene mwacita cifuniro ca Mulungu, mukalandire lonjezano. (Ahebri 10:36)**

Ndipo m'dalitso ndi umene umakulondolani:

**Ndipo kudzali, mukadzamvera mau a Yehova Mulungu wanu mwacangu, ndi kusamalira kucita malamulo ace onse amene ndikuuzani lero, kuti Yehova Mulungu wanu adzakukulitsani koposa amitundu onse a pa dziko lapansi; ndipo madalitso awa onse adzakugwerani, ndi kukupezani, mukadzamvera mau a Yehova Mulungu wanu. (Deuteronomo 28:1-2)**



## **CHIMATITHANDIZA KUTI TIPEWE KULANGIDWA:**

Chilango ndi kulandira mwambo, chidzudzulo ndi chikonzero. Onse amene samvera chifuniro cha Mulungu mwadala amalangidwa.

**Koma kudzali, mukapanda kumvera mau a Yehova Mulungu wanu, kusamalira kucita malamulo ace onse ndi malemba ace amene ndikuuzani lero, kuti matemberero awa onse adzakugwerani ndi kukupezani, (Deuteronomo 28:15)**

**ndipo mwaiwala dandauliro limene linena nanu monga ndi ana, Mwana wanga, usayese copepuka kulanga kwa Ambuye, Kapena usakomoke podzudzulidwa ndi iye; Pakuti iye amene Ambuye amkonda amlanga, Nakwapula mwana ali yense amlandira. Mukapirira kufikira kulangidwa Mulungu acitira inu monga ngati ana; pakuti mwana wanji amene atate wace wosamlanga? Koma ngati mukhala opanda cilango, cimene onse adalawako, pamenepo muli am'thengo, si ana ai. Komanso, tinali nao atate a thupi lathu akutilanga, ndipo tinawalemekeza; kodi sitidzagonjera Atate wa mizimu koposa nanga, ndi kukhala ndi moyo? (Ahebri 12:5-9)**

Yesu anachenjezanso:

**Ndipo kapolo uyo, wodziwa cifuniro ca mbuye wace, ndipo sanakonza, ndi kusacita zonga za cifuniro caceco, adzakwapulidwa mikwapulo yambiri. (Luka 12:47)**

Kudziwa chifuniro cha Mulungu ndi chinthu chofunika kwa iwo amene akufuna kukhala moyo osefukira kapena ochita bwino komanso kupewa chilango cha Mulungu.

## **CHIMABWERETSA CHIPAMBANO:**

Langizo limodzi limene Yoswa anapatsidwa atasenza utsogoleri wa fuko la Israeli linali kusunga Malamulo a Mulungu ndi kuyenda munjira za Yehova. Zinali zotsikimizika kuti ngati iye amvere, izi zidzamutsata:

**popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. (Yoswa 1:8)**

Buku la Masalimo limaonetseranso kuti munthu amene amayenda munjira za Mulungu amachita bwino (Salimo 1:3) Mudziko lodzala ndi zolepheretsa zambiri, kudziwa Mulungu ndi kuchita chifuniro chake ndiye chinsinsi chakuchita bwino.

## **CHOLINGA CHOYENERA**

Chikondi pa Mulungu ndiye chifukwa choyenera chokwanilitsira chifuniro cha Mulungu. Chikondi chimalakalaka kukondweretsa Mulungu amene ndi mwini chikondi:

**Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga. (Yohane 14:15)**

**Iye wakukhala nao malamulo anga, ndi kuwasunga, iyeyu ndiye wondikonda Ine; koma wondikonda Ine adzakonedwa ndi Atate wanga, ndipo line ndidzamkonda, ndipo ndidzadzionetsandekha kwa iye. (Yohane 14:21)**

**Yesu anayankha nati kwa iye, Ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo. (Yohane 14:23)**

**MAYESO ODZIYESA NOKHA:**

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.  
\_\_\_\_\_
2. Kodi cholinga chenicheni chochitira chifuniro cha Mulunug ndi chiani?  
\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_
3. Kodi chifuniro cha Mulungu ndi chofunika bwanji, tchulani mfundo khumi?  
\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_
4. Kodi chifuniro ndi chiani?  
\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_
5. Perekani matanthauzo awiri a chifuniro cha Mulungu.?  
\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_
6. Tchulani mitundu itatu ya chifuniro chimene chimagwira ntchito pa dziko lapansi  
\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_
7. Werengani ziganizo ndipo mulembe **T** kutsogolo kwa chiganizo chimene ndi cholondora. Lembani **F** kutsogolo kwachiganizo chimene ndi chosalandola.
  - a. \_\_\_\_ Yesu samakhudzika ndi kuchita chifuniro cha Mulungu.
  - b. \_\_\_\_ Baibulo limaonetsera kuti munthu alibe kuthekera koyendetsa moyo wake moyenera.
  - c. \_\_\_\_ Chifuniro cha munthu nthawi zina chimasephana ndi chifuniro cha Mulungu.
  - d. \_\_\_\_ Ndi Mulungu yekha amene amadziwa zonse zamtsogolo.
  - e. Mukhoza kukhala ndi mdalitso waukulu pakuchita molingana ndi chifuniro cha Mulungu.  
(Mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa bukuli)

## MAPHUNZIRO OONJEZERA

Mtumwi Paulo anatsindika kwambiri chifuniro cha Mulungu. Werengani ma vesi ali munsuwa:

Machitidwe 16:6-10; Aroma 1:10; 15:32; I Akorinto 1:1; 4:19; 16:7;

II Akorinto 1:1; Aefeso 1:1; Akolose 1:1; II Timoteyo 1:1

<b>Tanthauzo la Chifuniro cha Mulungu</b>		
<b>Chifuniro cha iye yekha Mulungu (Boulema)</b>	<b>Chifuniro pa Munthu (Thelema)</b>	<b>(makhalidwe)</b>
chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi	Chikonzero cha Mulungu pa munthu wina aliyense	Malamulo akakhalidwe ovumbulutsidwa mu Baibulo amene amaphunzitsa mmene tiyenera kukhalira ndi kukhulupirira
Samakhudzidwa ndi ziganizo zopanga munthu	amakhudzidwa ndi ziganizo zopanga munthu	Chifuniro cha Mulungu chimagwirizana ndi malamulo ake akakhalidwe
Aroma 11:33-36	Genesis 24	Zitsanzo:
Machitidwe 2:23	Miyambo 16:9	II Akorinto 6:14
Machitidwe 4:27-28	Masalimo 2:8	Aroma 2:18
Aroma 9:19	Miyambo 3:5-6 I	Atesalonika 5:18
Miyambo 16:33	Aefeso 5:17 I	Atesalonika 4:3
Aefeso 1:11	Aefeso 6:6	(ndi ena ambiri
Chibvu 4:11	Aroma 12:2	olembedwa
Miyambo 21:1	Akolose 1:9	mu Baibulo)
Danieli 4:35	Akolose 4:12	

## CHAPUTALA 4

### KUTENGA NJIRA YOLAKWIKWA

#### ZOLINGA

Pamapeto pa chaputalachi muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kupeza njira zachikunja zopezera chitsogozo.
- Kusiyanyitsa pakati pa aneneri onyenga ndi enieni.
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti “kutengera”

#### VESI YOTSOGOLERA.

**Inu Yehova, ndidziwa kuti njira ya munthu siri mwa iye mwini; sikuli kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ace. (Yeremiya 10:23)**

#### MAU OYAMBA

Ndi zofunika kusadziwa kachitidwe kazinthu chimodzimodzinso ndikofunika kudziwa kachitidwe kazinthu.

Katswiri wina waku America otchedwa Thoms Edison anachita kafukufuku olephereka kokwana zikwi khumi kuti apange nyali zoyendera magetsi. Ndipo atafunsidwa ngati amanong’oneza bondo kuti wataya nthawi yake pachabe, iye anayankha nati: “Ayi ndapeza njira 1000 zosayenera zakapangidwe ka nyali.” Mtsogolo iye sanataye nthawi kugwiritsa ntchito njira zolakwika zija.

Mulungu mu Baibulo akuchenjeza njira zimene sitiyenera kutsata pamene tikufuna chitsogozo cha moyo wathu. Ndipo ngati mungatsate njira zimenezi ndiye kuti simuononga nthawi yanu ndi njira zosavomelezeka pamaso pa Mulungu. Izi zikuthandizani kuti musapange ziganizo zolakwika zokusocheretsani.

Mu chaputala ichi, tiona mmene Mulungu anadzionetsera yekha kale komanso mmene akuyankhulira ndi anthu lero lino. Koma poyamba tiyenera kuona zinthu zimene muyenera kutsata kapena kufunsira uphungu.

## NYANGA

Pali zichitochito zambiri za Satana zimene ndi zanyanga. Ndipo zambiri mwanjira zimenezi zimagwiritsidwa ntchito pofuna kupeza chitsogozo. Zinthu zanyanga zimasiyana pakati pa anthu amitundu yosiyanasiyana koma zina mwa zinthu zanyanga zimakhala ndi zinthu ngati asing'anga, afiti, owombeza, olojera mwayi, matsenga, kusamalira mitambo ndi kubwebweta. Zinthu zamatsenga ndi china chilichonse chimene pamakhala kugwiritsa ntchito mphamvu yauzimu yasalumikizana ndi Mulungu. Zinthu ngati zimenezi zimakhala zochokera kwa Satana.

Mulungu anachenjeza anthu ake kuti asamachite zinthu zimenezi. Mukhoza kuwerenga machenjezo amenewa pa Deteronome 18:9:14 ndi Eksodo 22:18.

Ufiti ndi mtchitidwe wa afiti umakhazikika pa kuombeza, kulodza, kupepetulana, ndi makhalidwe ena. Komanso ufiti umakhala ndi gawo lakupembedza Satana. Ufiti ndi mtchitidwe wina uli onse wa Satana umene umadana ndi kuuka kwa Mulungu.

Baibulo limaonetsera kuti amatsenga amachotsa chikhulupiriro pa ambuye.

**Koma Elima watsengayo (pakuti dzina lace litera posandulika) anawakaniza, nayasa kupatutsa kazembe asakhulupire. (Macitidwe 13:8)**

### UFITI UMASOKONEZA ANTHU A MULUNGU.

Amatsenga sakalowa Ufumu wakumwamba:

**Pakuti ndi nyanga yako mitundu yonse inasokeretsedwa. (Cibvumbulutso 18:23)**

Buku la Chibvumbulutso limawoatsnetsera mathero a anthu onse ochita zinthu za usatana.

**Koma onyansa, ndi ambanda, ndi acigololo, colandira cao cidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure; ndiyo imfa (Cibvumbulutso 21:8)**

Mwana weniweni wa Mulungu sayenera kutenga gawo lina lililone ndi zinthu zanyanga pofuna kufunsira chitsogozo kapena pa china chilichonse.

### NJIRA ZOOMBEZA/MAULA

Kuchita mayere inali njira imodzi yofuna kudziwa chifuniro cha Mulungu mu Chipangano Chakale. Mukhoza kuwerenga zokhudza zimenezi powerenga Levitiko 16:7-10, Numeri 26: 55, 27:21, ndi Yoswa 18:10.

Njira iyi yofuna kudziwa chifuniro cha Mulungu inali Yovomerezeka mu Chipangao Chakale. Koma nthawi yokhayo mayere anachitika mu Chipangano Chatsopano inali nthawi imene Mzimu Woyera asanafike. Iyi inali nthawi imene atumwi a Yesu anali kufuna kupeza mlowa mmalo wa Yudasi amene anamupereka Yesu kenako ndi kudzipha. Anthu awiri anasankhidwa kuti apezepo mmodzi.

**Ndipo anayesa maere pa iwo; ndipo anagwera Matiyasi; ndipo anawerengedwa pamodzi ndi khumi ndi mmodziwo. (Macitidwe 1:26)**

Matiyasi anasankhidwa ngati mulowa mmalo wa Yudasi, koma dzina lake silimatchulidwanso mu Chipangano Chatsopano. Koma mtumwi Paulo ndi amene anatenga malo a Matiyasi pakati pa atumwi. Matiyasi chinali chisankho cha anthu kudzera mu mayere. Koma Paulo chinali chisankho cha Mulungu kudzera mu Mzimu Woyera

**CHIKOPA**

Pali nkhani imodzi mu Chipangano Chakale imene imaonetsa kuti chikopa chinagwiritsidwa ntchito pofuna kudziwa chifuniro cha Mulungu. Mukhoza kuwerenga nkhani imeneyi pa Oweruza 6:36-40.

Mulungu anayankhula ndi Gidiyoni ndi kumudziwitsa chifuniro chake. Pofuna kutsikimiza zimene Mulungu anayankhula, Gidiyoni anayika chikopa pansu. Koyamba anapempha Mulungu kuti anyowetse nthaka ndi mame osati chikopacho ndipo kachiwiri, iye anapempha Mulungu kuti anyowetse nthaka yozungulira chikopacho ndi mame ndipo kuti chikopacho chikhale chouma.

Palibenso ndime ina imene Mulungu anauza okhulupirira kuti agwiritse ntchito njira ngati imene anagwiritsa ntchito Gidiyoni munthawi imene Israeli anali pa mavuto. Kugwiritsa ntchito chikopa ndi mayere kunachitika kamodzi kokha mu Baibulo. Komanso kugwiritsidwa ntchito kwa mayere kunachitika Mzimu Woyera asanabwere mu Chipangano Chatsopano.

Sitikuyenera kugwiritsa ntchitp chikopa ndi cholinga choti tidziwe chifuniro cha Mulungu. Kugwiritsa ntchito chikopa lero lino kukhoza kukhala kumanena kuti “ngati chinachake chichitike, ndiye kuti ndi chifuniro cha Mulungu”- koma chikopa chathu nthawi zambiri chimakhala zinthu zimene zimachitika zokha pachilengedwe.

Molingana ndi kugwiritsidwa ntchito kwa Chikopa kumene Gidiyoni anagwiritsa ntchito, Iye anali akudziwa kale chifuniro cha Mulungu. Chikopacho chinangogwira ntchito yofuna kungotsikimiza chifuniro cha Mulungu osati kupeza chitsogozo cha Mulungu. Komanso ichi chinali chinthu chimene yankho lake limayenera kubwera kudzera mu mphamvu za umulungu.

Mu Chipangano Chatsopano, Zakariya atapempha chizindikiro kuti pofuna kutsikimiza zakubadwa kwa Yohane M'batizi, iye anakhala munthu osayankhula. Izi zinali chonchi chifukwa iye sanakhulupilire mau a Mulungu popempha chizindikiro (Luka 1:18-20)

Yesu ananena kuti “akubadwa oipa achigololo afunafuna chizindikiro” (Mateyu 12: 39). Chikopa chikhoza kukhala chizindikiro chasafuna kusakhulupirira kapena kusafuna kuchita chifuniro cha Mulungu. Chikopa chimene chimayankhidwa mwa njira zakuthupi zikhoza kukhala chosokoneza komanso chabodza.

### **ANANERI ONYENGA**

Baibulo liri ndi nkhani za aneneri a Mulungu. Limaonetsa kuti Mulungu amasankha aneneri mu mpingo komanso limafotokozera mphatso yauzimu yauneneri (Aefeso 4:11 ndi 1 Akorinto 12:10)

Kunenera ndi kuyankhula pansu pa kuthandizidwa ndi Mulungu. Kapena kuti ndi kuthekera kolandira ndi kuyankhula mau a Mulungu kwa anthu ake kudzera muzoyankhula zimene ndi zozodzedwa ndi Mulungu. Mau amene mneneri amayankhula mothandizidwa ndi Mulungu amatchedwa uneneri. Kunenera kumatanthauza kuyankhula mau ochokera mkamwa mwa Mulungu amene amatonthoza, kulimbikitsa komanso kutithandiza.

**Koma iye wakunenera alankhula ndi anthu comangirira ndi colimbikitsa, ndi cosangalatsa, (1 Akorinto 14:3)**

Sikuti uneneri umatenga malo a Mau a Mulungu olembedwa ayi chifukwa Baibulo limati maulosi adzayima koma mau a Mulungu adzakhalapobe chikhalire. (1 Akorinto 13:8 ndi 1 Peutro 1:25).

Mu Chipangano Chakale, anthu amapita kwa aneneri kuti apeze chitsogozo. Izi zimachitika chifukwa chakuti pa nthawiyi mphatso ya Mzimu woyera inali isanaperekedwe. Sikoyeneranso lero lino kupita kwa mneneri ndi cholinga chofunsira chifuniro cha Mulungu cha moyo wathu. Izi zili chomwechi chifuka chakuti ndi ntchito ya Mzimu Woyera kupereka chitsogozo kwa okhulupirira wina aliyense. Okhulupirira aliyense ayenera kuphunzira kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

Mzimu Woyera utaperekedwa, Palibe ndime imene imaonetsa okhulupirira akufunsira chitsogozo kwa mneneri. Koma Mulungu agwiritsabe ntchito mphatso imeneyi pofuna



kutsimikiza zamtsogolo. Mukhoza kuwerenga zitsanzo monga: Machitidwe 21:1-14 Agabasi anapereka uneneri kwa Paulo.

Paulo anali akudziwa kale zimene zidzamuchitikire Ku Yerusalemu ndipo izi zinangochitira umboni pa zimene zimayenera kuchitika. Uwu sunali uneneri wachitsogoo omuuza Paulo ngati amayenera kupita ku Yerusalemu kapena ayi.

Baibulo limachenjeza za ananeri onyenga pa dziko lapansi (Mateyu 24:11, 24: Marko 13:22). Chifukwa cha ichi, Mulungu anapereka njira zozindikira uneneri weniweni. Baibulo limafotokoza kuti:

**Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; (Aroma 12:6)**

Mau oti “molingana ndi muyeso wachikhulupiriro” akutanthauza kuti molingana ndi muyeso oyenera wachikhulupiro. Njira imodzi yotha kuzindikira ngati uneneri uli oyenera ndi ngati uneneriwo ukugwirizana kapena kusemphana ndi mau a Mulungu.

**Ndipo aneneri alankhule awiri kapena atatu, ndi ena azindikire. (1 Akorinto 14:29)**

Apa tikuuzidwa kuti uneneri uyenera kuunikidwa. Muyeso weniweni wa uneneri ndi mau a Mulungu.

Mulungu wapereka njira zambiri zothandiza kuzindikira aneneri abodza. Aneneri abodza amadziwika chifukwa zimene amanenera sizimakwaniritsidwa.

**Koma mneneri wakucita modzikuza ndi kunena mau m'dzina langa, amene sindinamlamulira anene, kapena kunena m'dzina la milungu yina, mneneri ameneyo afe. Ndipo mukati m'mtima mwanu, Tidzazindikira bwanji mau amene Yehova sananena? Mneneri akanena m'dzina la Yehova, koma mau adanenawa sacitika, nisafika, ndiwo mau Yehova sanawanena; mneneriyo ananena modzikuza, musamuopa iye. (Deuteronomo 18:20-22)**

Santhulani ndime zili munsimu mu Baibulo zimene zimafotokoza njira zimene tingadziwire aneneri onyenga.

- Aneneri abodza savomereza umulungu wa Yesu Khristu: 1 Yohane 4:1-3.

- Aneneri abodza amaphunzitsa ziphunzitsa zonyenga: 2 Peturo 2:1-3
- Aneneri abodza amasocheretsa anthu pamaso pa Mulungu Deteronome 13: 1-5.
- Aneneri abodza amanyenga anthu ndi zizindiuro za zozizwitsa zabodza: Mateyu 24: 23-24.
- Moyo wao sumaonetsa chipatso chabwino. Njiri imodzi yabwino yosiyanita mneneri weniweni ndi wachinyengo ndi kuyang'anitsitsa mmene amakhalira moyo wao. "Baibulo limafotokoza kuti ndi zipatso zao mudzawadziwa." Aneneri onyenga samaonetsera umboni uli onse wachipatso chauzimu mmoyo wao: Mateyu 7:16.
- Aneneri onyenga amadziyenereza ndi zinthu zabodza: Mateyu 24:23

Chifukwa chakuti kuli aneneri abodza pa dziko lapansi, muyenera kukhala osamalitsa pamene mukulandira uneneri. Nthawi zambiri ulosi wagwiritsidwa ntchito molakwika ndi ongofuna kuwalamulira okhulupirira mosayenera. Pamene talandira uneneri okhudza ife, tiyenera kuunikira molingana ndi mau a Mulungu olembedwa ndipo uneneriwo uyenera kugwirizana ndi mau a Mulungu. Ikakhala nkhani yopereka chitsogozo, uneneri uyenera kutsikimizidwa osati kulamula munthu kapena kumuuzza choti achite mokakamiza.

Chifukwa chakugwiritsa ntchito mphatso zauzimu molakwika, anthu ena okhulupirira amakanitsitsa kuti uneneri ulipo. Koma sikoyenera kukana utumiki wa Mzimu Oyera chifukwa chakuti munakumana ndi zitsanzo zingapo zolakwikwa.

### **UPHUNGU OLAKWIKWA**

Palibe munthu amene angazindikire chifuniro cha Mulungu pa anthu ena popanda zimene zaonetseredwa mu Baibulo. Mwachitsanzo, timadziwa kuti munthu wina aliyense ayenera kulapa chifukwa izi limaphunzitsa ndi Baibulo.

Uphungu wauzimu operekedwa ndi atsogoleri oopa Mulungu uli m'gawo lake pa moyo wa munthu okhulupirira, koma munthu opereka uphungu alibe ulamuliro owuza munthu chochita kapena kufotokozera chifuniro cha Mulungu pa zinthu zimene Baibulo silinafotokozere.

Pamene Paulo anakhazikitsa mkati mwake kuti apita ku Yerusalemu, abale ena ku Sizareya anamuletsa iye kuti asatero. Iwo amamuchenjeza za mavuto amene akhoza kumugwera kumeneko. Koma pamene Paulo anakana uphungu wao, iwo anavomeleza chiganizo chake ndipo anati:

**Ndipo pokana iye kukopeka, tinaleka, ndi kuti, Kufuna kwa Ambuye kucitidwe.  
(Macitidwe 21:14)**

Iwo anazindikira kuti ngakhale kuti chinali chifuniro chao kuti Paulo asapite, koma iwo anazindikira kuti Paulo amayenera kuti azindikire chifuniro cha Mulungu.

Ndizofunika kuti muzindikire nokha chifuniro cha Mulungu. Simungakhulupilire anthu ena kuti apereke chitsogozo cha moyo wanu. Izi zili chomwechi chifukwa pali mizimu yoipa imene cholinga chake ndi kusocheretsa inu.

**Okonedwa, musamakhulupirira mzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati icokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi. (Yohane 4:1)**

Pamene mwalandira uphungu kwa munthu, uphungu umeneu uyenera kuyesedwa ndi njira zina zimene zimagwira ntchito pofuna kuzindikira chifuniro cha Mulungu. Izi zifotokozeredwa mwatsatanetsatane mu chaputala chikubwerachi.

### **KUTENGERA/ KADUKA**

Kutengera ndi limodzi mwa ntchito zakuthupi zotchulidwa pa Agalitiya 5:20. Ntchito za thupi ndi zinthu zosiyanasiyana zosakondweretsa Mulungu.

Nsanje ndi chikhumbitso chofuna kutengera zimene ena akuchita kapena kufuna kuwapitirira. Izi gwero lake ndi udani komanso nsanje. Anthu ena amatengera mautumiki ena amene akuoneka kuti akuchita bwino mmalo moti afunsire chifuniro cha Mulungu pa moyo wao. Palibe okhulupirira awiri amene amakhala ndi ntchito yofanana. Mzinu Woyera amaitana munthu wina aliyense ku utumiki wakewake.

**Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako. (Macitidwe 13:2)**

Baibulo limafotokoza kuti okhulupirira ali ndi mphatso zauzimu zosiyanasiyana:

**Ndipo pali mphatso zosiyana, koma Mzimu yemweyo. (1 Akorinto 12:4)**

**Koma zonse izi acita Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna. (1 Akorinto 12:11)**

Ngakhale tikuuzidwa kuti tifunitsitse mphatso zoposa (1 Akorinto 12:31) komanso kuti tifunitsitse mphatso zauzimu. (1 Akorinto 14:1), koma izi sitikutanthauza kuti titengere zimene

anthu ena amene ali ndi mautumiki akuluakulu. Pamene Peturo amaoneka okhudzika ndi utumuki wa Yohane, Yesu anati kwa iye:

**Yesu ananena naye, Ngati ndifuna uyu akhale kufikira ndidza Ine, kuli ciani ndi iwe? unditsate Ine iwe. (Yohane 21:22)**

Mulungu anapereka dongosolo la chombo kwa Nowa, anapereka dongosolo la likasa kwa Mose, anapereka dongosolo lakamangidwe ka kachisi kwa Solomoni. Yeremiya anapatsidwa dongosolo la kumangaso zikupa za mzinda wa Yerusalemu. Mulungu sanauze inu kuti mumange chombo, kachisi kapena zikupa za mzinda wa Yerusalemu, Iye ali ndi dongosolo lapaderadera pa ife. Ngati mungagwe mutchimo la kaduka kapena kutengera anthu ena, ndiye kuti musemphana ndi chimene Mulungu akufuna.

Mukatenga anthu ena ngati chifaniziro cha moyo wanu, mukhala kuti mwazungulidwa ndi zikhalidwe za anthu zimene zimalepheretsa kuti mulandire mavumbulutso a Mulungu.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

---

---

2. Kodi kutengera kapena kaduka ndi chiyani?

---

---

3. Werengani ziganizo zili munsimu ndipo lembani T kutsogolo kwa chiganizo chimene chili cholondola ndipo lemba F kutsogolo kwa chinganizo chimene sicholondola.

- a. \_\_\_ Baibulo limaphunzitsa kuti ndi zovomelezeka kufunsira uphungu pogwiritsa ntchito nyanga kapena matsenga.
- b. \_\_\_ Ngati simungapeze uphungu kuchokera kwa Mulungu, palibe vuto kudalira anthu ena kuti mupeze chitsogozo cha moyo wanu.
- c. \_\_\_ Muyenera kuvomera nthawi zonse zimene mneneri angakuuzeni kuti ndi choonadi ndi chifuniro cha Mulungu pa moyo wanu.
- d. \_\_\_ Zikhalidwe za anthu zimabisa mavumbulutso a Mulungu.
- e. \_\_\_ Kuchita mayere ndi njira zina zotengera mwayi ndi zambwino pofuna kuzindikira chifuniro cha Mulungu.
- f. \_\_\_ Baibulo limaphunzitsa kuti kugwiritsa ntchito chikopa ndi njira zotsikimizika yodziwira chifuniro cha Mulungu.
- g. \_\_\_ Njira imodzi yabwino yosiyanyisa aneneri onyenga ndi enieni ndi kuonetsetsa chikhalidwe chao.
- h. \_\_\_ Uneneri nthawi zonse uyenera kugwirizana ndi mau a Mulungu.
- i. \_\_\_ Uneneri okhudza moyo wathu suyenera kubwera mokakamiza koma ubwere ngati chitsikimizo chokha.

(Mayankho amafunso ali kumapeto kwa bukuli)

## ZOONJERA POPHUNZIRA

Baibulo lili ndi nkhani za anthu a Mulungu amene anatenga njira yolakwika chifukwa chosamvera mau a Mulungu. Werengani ndipo fotokozani mwachidule zimene muwerengezi.

Mfumu Saulo inapita kwa mfiti kuti ikapeze chitsogozo 1 Samueli 28

---

---

---

Manase anafunsira wanyanga II mbiri 33:16

---

---

---

Balamu anamvera upungu olakwika wa munthu: Numeri 22.

---

---

---

## CHAPUTALA 5

### CHIFANIZIRO CHA CHIFUNIRO CHA MULUNGU.

#### ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kutchula mfundo zokhudza chifuniro cha Mulungu.
- Kupeza akuluakulu awiri achifuniro cha Mulungu.
- Kugwiritsa ntchito mau a Mulungu olembedwa pofuna kupanga ziganizo mmoyo wanu
- Kufotokozero chifanizo cha chifuniro cha Mulungu.
- Kupereka zitsanzo okhulupirira akufanizidwa ndi chifuniro cha Mulungu.
- Kupirizabe kuphunzira za chifuniro cha Mulungu mu Baibulo.

#### VESI YOTSOGOLERA

**Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. Mwa iye tinayesedwa colowa cace, popeza tinakonzekeratu monga mwa citsimikizo mtima ca iye wakucita zonse monga mwa uphungu wa cifuniro cace; (Aefeso 1:9-11)**

#### MAU OYAMBA

Tisanaone njira zimene Mulungu amagwiritsa ntchito pofuna kuonetsera chifuniro chake, ndikoyenera kudziwa mfundo za chifuniro cha Mulungu. Chaputala changopitachi, tianaona tanthuzo la chifuniro cha Mulungu komanso ndi kuunikira njira zolakwika zozindikira chifuniro cha Mulungu pa moyo wathu.

#### MFUNDO ZA CHIFUNIRO CHA MULUNGU

Zina mwa mfundo za chifuniro cha Mulungu ndi izi:

#### MULUNGU AKUFUNA KUTI MUDZIWE CHIFUNIRO CHAKE:

Chikhulupiriro chimene chikhoza kuzindikira chifuniro cha Mulungu chakhazikika pa mfundo ziwiri zikuluzikulu:

**Yoyamba:** kukhulupirira kuti Mulungu ali ndi dongosolo la moyo wanu.

**Chachiwiri:** Kuthekera kwa Mulungu kuti ayankhule nanu.

Ma chaputala awiri akubwerawa afotokoza njira zimene Mulungu amagwiritsa ntchito pofuna kuyankhula ndi munthu. Monga mmene tinakambira chaputala chapitacho, Mulungu akufuna atayankhula ndi munthu kufikira kuti nthawi ina anagwiritsa ntchito bulu pofuna kuyankhula kwa mneneri (Numeri 22)

Baibulo limatitamula kuti:

**Cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani.  
(Aefeso 5:17)**

Paulo analemba ku Akolose:

**(Akolose 1:9) Mwa ici ifenso, kuyambira tsiku limene tidamva, sitileka kupembedzera ndi kupempherera inu, kuti mukadzazidwe ndi cizindikiritso ca cifuniro cace mu nzeru zonse ndi cidziwitso ca mzimu,**

Ku buku la Machitidwe, Paulo anayakhula ndi munthu wina ndipo anati:

**Ndipo anati, Mulungu wa makolo athu anakusankhiratu udziwe cifuniro cace, nuone Wolungamayo, numve mau oturuka m'kamwa mwace. (Macitidwe 22:14)**

Kuonjezera ma vesi amenewa, Mulungu wapereka malonjezano a chitsogozo chake mu Baibulo (ndipo zina mwa izi tizona patsogolo). Malingana ndi ndime zimenezi, tikhoza kutsindika kuti ndi cholinga cha Mulungu kuti tikadziwe chifuniro chake.

### **CHIFUNIRO CHA MULUNGU NDI CHOKONZEDWA:**

Mulungu akugwira ntchito pa dziko lapansi ndi cholinga choti akwaniritse chikonzero chake:

**Mwa iye tinayesedwa colowa cace, popeza tinakonzekeratu monga mwa citsimikizo mtima ca iye wakucita zonse monga mwa uphungu wa cifuniro cace; (Aefeso 1:11).**

Mulungu ali ndi chikonzero komanso dongosolo lonse la dziko lapansi. Chikonzero cha Mulungu chili pansu pa chifuniro cha iye mwini ngati Mulungu komanso molingana ndi chifuniro chake cha mmene munthu ayenera kukhalira



## **CHIFUNIRO CHA MULUNGU PA MUNTHU PAYEKHAPAYEKHA:**

Chifuniro cha Mulungu pa munthu wina aliyense chili ndi chikonzero chake chofuna kupulumutsa munthu:

**Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)**

Kupatula kuti chifuniro cha Mulungu pa munthu wina aliyense ndi chakuti apulumutsidwe, koma Iye alinso ndi dongosolo kapena chikonzero chapaderadera pa munthu wina aliyense payekhapayekha. Baibulo limachitira umboni kudzera nkhani zoonetsera Mulungu akugwira ntchito pa moyo wa anthu osiyanasiyana. Iye Anaika anthu munyengo zosiyanasiyana munthawi yake ndi cholinga choti akwanilitse chinachake. Nkhani ina iliyonse yopezeka mu baibulo ndi yosiyana ndi nkhani zina:

Mulungu anauza mnenero Yereimiya kuti:

**Ndisanakulenge iwe m'mimba ndinakudziwa, ndipo usanabadwe ndinakupatula iwe; ndinakuika kuti ukhale mneneri wa mitundu ya anthu. (Yereimiya 1:5)**

Kodi pali umboni wanji waukulu pa dongosolo la Mulungu pa munthu?

Pamene Peturo anali ndi kukhudzika ndi utumuki wa Yohane, Yesu anamuyankha iye nati:

**Yesu ananena naye, Ngati ndifuna uyu akhale kufikira ndidza Ine, kuli ciani ndi iwe? unditsate Ine iwe. (Yohane 21:22)**

Yesu anali ndi chikonzero chosiyanasiyana pa moyo wa Petro ndi Yohane.

Tikalayang'anitsitsa dziko, zimaonetsa kuti pali dongosolo lapaderadera. Mwachitsanzo kayendedwe ka nyenyezi ndi dzuwa, mapangidwe a zinthu ngati maluwa, nyanja ndi zina zambiri amaonetsa kuti pali chikonzero chapaderadera cha Mulungu pa zinthu zonsezi. Chimodzimodzinsu, Mulungu ali ndi chikonzero kapena dongosolo lapadera pa munthu wina aliyense, chifukwa munthu aposa chilengedwe chonse. Mulungu analonjeza:

**Ine ndidzakulangiza ndi kuphunzitsa iwe za njira ukayendayo; Ndidzakupangira ndi diso langa lakuyang'ana iwe. (Masalmo 32:8)**

Njira ya munthu wina aliyense ikuoneka mu ndime imeneyi:

Pa Masalimo 37, amafotokoza kuti Yehova akhazikitsa mayendwe a munthu olungama:

**Yehova akhazikitsa mayendedwe a munthu; Ndipo akondwera nayo njira yace (Masalmo 37:23).**

Mau oti kukhazikitsa akugwiranso ntchito pa Salimo 8:3 mogwirizana ndi mwezi ndi nyenyezi zimene Mulungu analenga. Kafukufuku wa sayansi amafotoza zakayendedwe ka zinthu mlengalenga ngati mmene akufotokozera apa.

Ngati mmene zinthu zamulengalenga ziyendera, chimodzimodzinsu mayendedwe a anthu olungama amakhazikitsidwa ndi Mulungu.

**Ndipo makutu ako adzamva mau kumbuyo kwa iwe akuti, Njira ndi iyi, yendani inu m'menemo: potembenukira inu kulamanja, ndi potembenukira kulamanzere. (Yesaya 30:21)**

Mulungu sikuti amangokhazikitsa zinthu zikuluzikukulu zokha ayi, koma china chilichonse chimakhazikitsidwa ndi Mulungu.

## **CHIFUNIRO CHA MULUNGU SI CHIFUNIRO CHA MUNTHU**

Chifuniro cha munthu nthawi zambiri chimasemphana ndi chifuniro cha Mulungu.

**Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova. Pakuti monga kumwamba kuli kutari ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu. (Yesaya 55:8-9)**

Chifuniro cha Mulungu nthawi zambiri si njira imene muntha amatha kuyisankha pachikhalidwe chake ngati munthu. Ichi ndi chifukwa chake zili zofunika kuzindikira kuyankhula kwa Mulungu. Sikuti izi zikutanthauza kuti chifuniro cha Mulungu chimabweretsa chisoni ayi.

## **CHIFUNIRO CHA MULUNGU NDI CHABWINO:**

Baibulo linaphunzitsa kuti chifuniro cha Mulungu ndi chabwino nthawi zonse. Ngakhale kuti njira zake sizimene inu mukhoza kusankha mwainu nokha, koma Mulungu amadziwa chimene chili chabwino kwa ife. Pa Salimo 37:23 amafotokoza kuti tidzakondwera mu njira yake yokhazikitsidwa ndi Mulungu.

Paulo akufotokoza kuti chifuniro cha Mulungu ndi chabwino:

**Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:2)**

## **DONGOSOLO LA MULUNGU NDI LOPITILIRABE**

Aefeso 2:10 amafotokoza kuti “ife ndi chipango chake.” Mau oti ndife akuonetsera kuti Mulungu akupitirizabe kugwirabe tchito mmoyo wathu. Kuvumbulutsa chifuniro chake ndi ntchito imene Mulungu akugwirabe.

**Pakuti wakucita mwa inu kufuna ndi kucita komwe, cifukwa ca kukoma mtima kwace, ndiye Mulungu, (Afilipi 2:13)**

Paulo analemba okhulupirira achiheberi kuti chinali chifuniro cha Mulungu kuti:

**Akuyeseni inu opanda cirema m'cinthu ciri conse cabwino, kuti mucite cifuniro cacej ndi kucita mwa ife comkondweretsa pamaso pace, mwa Yesu Kristu; kwa Iyeyu ukhale ulemmerero ku nthawi za nthawi. (Ahebri 13:21)**

Kugwira ntchito ndi mau amene akuonetsera nthawi yatsopano. Mulungu akupitilira kupereka chitsogozo chake, kukuza ndi kuyankhula molinga ndi dongosolo lake. Mulungu walonjeza chitsogozo chopitira:

**Ndipo Yehova adzakutsogolera posalekai (Yesaya 58:11)**

## **MAGAWO AWIRI A CHIFUNIRO CHA MULUNGU**

Tikakamba za chifuniro cha Mulungu, tikuyenera kuzindikira kuti pali magawo awiri a chifuniro cha Mulungu ndipo gawo lina lilironse limagwirizana ndi linzake.

## **CHOYAMBA: CHOYUMBULUTSIDWA MU BAIBULO**

Gawo loyamba la chifuniro cha Mulungu ndi chimene chimapezeka mu Baibulo. Mu chaputala chapitachi, tinakambirana matantauzo atatu a chifuniro cha Mulungu. Tinaona kuti Pali chifuniro cha iye yekha Mulungu, chifuniro cha chikhalidwe cha Mulungu ndi chifuniro cha Mulungu pa munthu. Mitundu ya chifuniro yonseyi ikuonetsedwa mu chithunzi chili muchithunzi ichi.

## Chifuniro cha Iye yekha Mulungu

Chifuniro cha khalidwe la mulungu

chifuniro cha Mulungu pa munthu

Chithuzi chili pamwambachi, chikuonetsera kuti chifuniro cha Mulungu pa munthu wina aliyense chili pansu pa chichifuniro chamakhalidwe ndi chifuniro cha iye yekha Mulungu chovumbulutsidwa mu mau ake olembedwa. Mau ake olembedwa ali ndi mavumbulutso a malamulo a chikhalidwe chake. Mkati mwa izi muli malamulo onse a mene muyenera kukhalira moyo wanu. Monga mmene mukuonera pachithuzichi, Chifuniro cha Mulungu cha iye yekha chili pamwamba pa chifuniro cha chikhalidwe. Ndi chifuniro cha iye Mulungu kuti munthu wina aliyense akhale molinga ndi mulingo wachikhalidwe cha mau ake. Mau ake olembedwa muli chifuniro chake cha iye yekha chimene wasankha kuululira kwa ife komanso chikonzero chake cha dziko lonse lapansi komanso ndi anthu onse.

Kufotokoza mwachidwe kwa chikonzero chimenechi kukupezeka mu ma vesi a chaputala ichi.

**Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. Mwa iye tinayesedwa colowa cace, popeza tinakonzekeratu monga mwa citsimikizo mtima ca iye wakucita zonse monga mwa uphungu wa cifuniro cace; (Aefeso 1:9-11)**

Mu gawo la zophunzira zoonjezera, ma vesi oonetsera chifuniro cha Mulungu aperekedwa ngati chitsanzo chabe.

### **CHACHIWIRI: CHIFUNIRO CHAVUMBULUTSUDWA MU MAU AKE:**

Gawo lachiwiri la chifuniro cha Mulungu ndi chifuniro chimene sichinalembedwe mu malemba. Izi ndi chikonzero chake pa moyo wa munthu okhulupirira wina aliyense. Mulungu samavumbulutsa mwachindunji utumiki wanu, tchito imene mudzagwire, munthu amene mudzamukwatire ndi zina zambiri. Koma zinthu zonsezi ndi zofunika kwambiri. Chifukwa cha ichi, mukuyenera kufunsira chifuniro chake pa zinthu ngati izi ndikutha kuzindikira mau ake pamene alakhula nanu.

## **KUFANANITSA MITUNDU IWIRIYI:**

Pamene mukufuna kudziwa chifuniro cha Mulungu pa zinthu zimene mukukumana nazo, chinthu choyamba ndi kusanthula mau a Mulungu kuti muone ngati mayankho ake mungawapeze mu Baibulo. Palibe chifukwa chofunira chifuniro cha Mulungu kapena kufunafuna chitsikimizo pamene Mulungu anayakhula kale mu malemba ake. Muyenera kusanthula malemba ake mosamala pamene mukufunafuna chitsogozo, ndipo kenako vomelezani Mau ake ngati mau amene akulankulidwa kwa inu. Ngati simuvomeleza chitsogozo chimene Mulungu akupereka mu mau ake, ndiye mukhala kuti mwatsekula khomo loti munamizidwe kapena kupusitsidwa.

Mu nyengo zambiri Baibulo liri ndi mfundo zimene titati tazimvetse bwino ndi kuzigwiritsa ntchito, zikhoza kuthandiza kuti tipange chiganizo chogwirizana ndi mau a Mulungu. Ndipo mfundo zimezi zimagwira ntchito mu nyengo zosiyasiyana. Mwachitsanzo, Paulo akuchenjeza kuti:

**Musakhale omangidwa m'goli ndi osakhulupira osiyana; pakuti cilungamo cigawanabwanji ndi cosalungama? Kapena kuunika kuyanjana bwanji nw mdima? Ndipo Kristu abvomerezana bwanji ndi Beliyali? Kapena wokhulupira ali nalo gawo lanji pamodzi ndi wosakhulupira? (2 Akorinto 6:14-15)**

Apa Baibulo likufotokoza mfundo yaikulu yoti okhulupirira asamangidwe goli kapena kuti kuphatikizidwa ndi anthu osakhulupirira. Mfundo imeneyi ikhoza kugwiritsidwa ntchito munyengo zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, kukwatirana ndi munthu osakhulupirira, kuchita Malonda ndi munthu osakhulupirira, komanso kukhala ndi bwenzi lapamtima limene ndi losakhulupirira.

Muyera kusanthula Baibulo ndikuona zitsanzo zimene zikugwirizana ndi nyengo yanu. Komanso werengani nkhani za anthu a Baibulo ndi kuona ziganizo zimene anapanga ndi kuona ngati ziganizo zimene anapanga zinali zogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu.

MA GAWO AWIRI A CHIFUNIRO CHA MULUNGU

**chifuniro Chovumbulutsidwa  
(cholembedwa mu Baibulo)**

chifuniro cha Iye yekha Mulungu  
ndi chakakhalidwe  
chovumbulutsidwa  
mu Malemba. ndipo  
chili ndi zinthu izi:

chifuniro chake pa anthu onse  
komanso dongosolo lake  
lalikulu la dziko lonse lapansi.

Malamulo osiyanasiya  
ndi malonjezano oyendetsa moyo.

mfundo zikulu-zikulu za moyo  
zimene zothandiza kupanga ziganizo zina

**Chifuniro Chosavumbulutsidwa**

chikonzero cha moyo wa okhulupirira wina aliense

izi ndi gawo limodzi ziganizo monga, utumuki wathu, kumene  
Tikufuna kukhala, maphunziro kapena ukwati, komanso chitsogozo  
Munyengo zosiyanasiyana.

ziganizo zina zamunthu zikhoza kupangidwa potsatira mfundo  
zimenezi. Zitsanzo ndi malaumulo ena aperekedwa mu Baibulo

**CHIFANIZIRO CHA CHIFUNIRO CHA MULUNGU**

Gawo loyamba la phunziro ili linakhazikika kwambiri pa Aroma 12:1-2:

**Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:1-2)**

Mutafunsidwa kuti, “kodi chifuniro cha Mulungu cha ngwiro, chabwino ndi chovomelezeka ndi chiani.” Tikhala tikuyanka mafunso amenewa, ndipo izi zitithandizira kuti tizindikire chifaniziro cha chifuniro cha Mulungu.

## **CHIFUNIRO CHA MULUNGU CHANGWIRO**

Chifuniro cha Mulungu changwiro chimakwanilitsidwa pamene okhulupirira achita zinthu molingana ndi chifuniro chonse cha Mulungu.

Munthu okhulupirira amakhala kuti wavomereza chifaniziro cha iye yekha Mulungu cha chipulumutso chake kudzera mukubabwanso mwatsopano. Akuyenera kukhalanso molingana **ndi** malamulo akakhalidwe a Mulungu olembedwa mu Baibulo. Ndipo iye amakhala kuti wazindikira chitsogozo cha Mulungu pa chikonzero kapena dongosolo la moyo wake.

## **CHIFUNIRO CHABWINO CHA MULUNGU:**

Ichi ndi chifuniro cha Mulungu chimene okhulupirira akuyenda mu chikonzero cha mulungu changwiro, koma sakusemphana ndi chifuniro cha iye yekha Mulungu ndi chifuniro cha kakhalidwe cha Mulungu. Sikuti iye amakhala kuti sakumvera chifuniro cha Mulungu chovumbulutsidwa mumalemba, koma amakhala kuti akufunafunabe chikonzero cha Mulungu chagwiro pa moyo wake.

## **CHIFUNIRO CHA MULUNGU CHONGOVOMELEZA.**

Apa ndi pamene okhulupirira amakhala kuti akusemphana ndi chifuniro cha ngwiro cha Mulungu cha Moyo wake. Komabe iye amakhala kuti mulungu wangomulora kuti akhale mu dera limene akukhalaro kapena kuchita zimene akuchitazo ngakhale kuti sichifuniro chake cha Mulungu.

## **KUNJA KWA CHIFUNIRO CHA MULUNGU:**

Apa ndi pamene okhulupirira amakhala akusemphana ndi chifuniro cha Mulungu kapena kuti sakumvera chifuniro cha Mulungu.

### **Zitsanzo zopezeka mu Baibulo**

Nkhani ya Balamu imene anapempha mneneri Balamu kuti anenere motsutsana ndi anthu a Mulungu, Koma Mulungu anayankhula ndi Balamu ndikumuzu kuti asapite:

**Koma Mulungu anati kwa Balamu, Usapita nao; usatemberera anthuwa; pakuti adalitsika. (Numeri 22:12)**

Chinali chifuniro chagwiro cha Mulungu kuti Balamu asapite. Koma Balamu sanamvere mau a Mulungu anapita ndi azibambo aja. Pamane iye anachita izi, iye amachita zinthu kunjwa kwa chifuniro cha Mulungu chimene chinavumbulutsidwa.


Chifuniro cha Mulungu chinali choti Balamu adziwe chifuniro chake kufikira kuti Iye anagwiritsa ntchito bulu ndi cholinga choti azindikire tchimo lake. Izi zitachitika, Mulungu anamulola Balamu kuti apitilire ulendo wake koma ndi cholinga choti akadalitse ana a Israeli osati kutembelera. Munthawi imeneyi, Balamu amachita zinthu zake pansi pa chifuniro cha Mulungu chongovomeleza.

Ulendo wake unakumana ndi nyengo zosowetsa mtendere chifukwa cha munthu otchedwa Balaki. Koma zinthu zonsezi zikanatha kupewedwa akanamvera mau a Mulungu kuti asapite pachiyambi pomwe.

Fanizani nkhani imeneyi ndi “chifaniziro cha chifuniro cha Mulungu.” chifuniro chagwiro cha Mulungu pa Balamu chinali choti asapite ndi azibambo aku Moabu. Koma Balamu anachita kusamvera ndikuyamba kuyenda kunjwa kwa chifuniro cha Mulungu chagwiro. Iye samayenda muchifuniro chabwino cha Mulungu. Apa ndi pamene okhulupirira amasepmphana ndi chifuniro cha Mulungu koma chonsecho akuchifunafuna. Iye anali akuchita kusamvera ndi mau a Mulungu. Ngakhale izi zinali choncho, chifuniro cha Mulungu chongovolereza chinamulora Balamu kuti apitire ndi Ulendo wake posatengera kuti ichi sichinali chifuniro chagwiro cha Mulungu.

### **KUYENDA MUCHIFUNIRO CHA MULUNGU**


Kutsatira kubadwanso mwatsopano komanso kukopeka ndi chikondi cha Mulungu, cholinga cha okhulupirira ndi kuyenda molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Nthawi zambiri, chifaniziro cha okhulupirira ofanizidwa ndi Mulungu chiyenera chimaoneka ngati chithuzi chili pansichi:





Chifuniro cha Mulungu chikuonetseredwa mu chithuzi ndi mzere owongoka umene ndi osaduka pena paliponse (\_\_\_\_\_). Machitidwe a munthu molingana nd chifuniro cha Mulungu akuonetseredwa muchithunzichi ndi akalozera.

Pamene munthu asanabadwe mwatsopano amayenda munjira zake zimene zimakhala zosemphana ndi chfuniro cha Mulungu. Koma pamene munthu abadwa matsopano, okhulupirira amayembekezera kuyenda malingana ndi chifuniro cha Mulungu. Chifukwa chakuti okhulupirira amakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu, chiyembekezo chimakhala kuti azichita molingana ndi chifaniziro cha chifuniro cha Mulungu. Koma zoonadi za moyo uno ndi zakuti, chifaniziro chake chotsata chifuniro cha Mulungu chimaoneka chonchi.



Okhulupirira amakuma ndi nyengo zina zabwino zina zoipa pamene akufuna kuchita chifuniro cha Mulungu. Nthawi zina amamva kuyankhula kwa Mulungu ndikuchita chifuniro chake koma nthawi zina sizimakhala chonchi. Nthawi zina amakhumudwa akachita zinthu zolakwika komanso akasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Ena amangosiya kumene kufuna kumva mau a Mulungu.


Mukachiyanga'anitsitsa chithunzichi, mupeza kuti pali chinthu chofunika chimene tikusemphana nacho. Ngakhale kuti ndi zoonadi kuti okhulupirira amasemphana ndi chifuniro cha Mulungu, koma mukhoza kuona kuti mzere umene uli ndi mlozo ukuonetsa mayendedwe a okhulupirira amakhala opita chitsogolo. Angakhale kuti nthawi zina okhulupirira amatha kusemphana ndi chifuniro cha Mulungu, koma amakhala kuti akupitabe chitsogolo.

Mizere yodukadukayo ikuonetsera kuti nthawi zina okhulupirira amasepmphana ndi chifuniro cha Mulungu ndipo amazindikira izi, kuphunziri phunziro ndikubwelera pakuchita chifuniro cha Mulungu. Kudzera mukulephera komanso kuchita bwino, okhulupirira amakhala akuphunzira kumva kapena kuti kuzindikira mau a Mulungu. Zabwino ndi zoipa zimathandiza okhulupirira kuti apitirire kukula pakumvetsetsa mfundo za moyo otsogozedwa ndi Mulungu.

Chifuniro cha Mulungu chikaonedwa motere chimakhala chotipatsa ufulu, sichimaonedwa ngati malamulo chabe oti atsacidwe. Ndipo ife udindo wathu umakhala kuphunzira kulumikizitsa moyo wathu ndi chifuniro cha Mulungu.

### CHITSANZO CHA BAIBULO

Ganizirani za moyo wa mfumu Davide amene pachiyambi cha moyo wake ochita chifuniro cha Mulungu umaoneka chonchi.



Pamene Davide anakhala mfumu iye amayenda malingana ndi chifuniro cha Mulungu. Ndipo mulungu anamutcha munthu wapamtima pa ambuye. Koma Davide anachimwa ndi mkazi wa mwini wake ndipo anabala mwana osayenera. Uku kunali kusamvera mau a Mulungu olembedwa. Davide anabwera pamaso pa Mulungu ndikulapa machimo ake. Iye anakhululukidwa ndikuyambanso kuyenda malinga ndi chifuniro cha Mulungu.

Pamene tikhale tikuunikira mmene Mulungu amalakhulira kwa anthu mumachaputala awiri akubwerawa, mukhale mukukumbukirabe chithunzi chachiri. Chithunzi chimechi chimaonetsera chifaniziro chanu pakuchita chifunira cha Mulungu.

Pamene mukuphunzira kuyenda ndi Mulungu, zabwino ndi zoipa zimene mumakumana nazo zimakuthandizani kuti mupitilire kuzindikira chifuniro cha Mulungu. Musasiye kuchita chifuniro cha Mulungu posatengera kuti nthawi zina mumalephera. Simukuyenera kusiya.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani veso yotsogolera osaonera

---

---

---

2. Malizitsani ziganizo zili munsizi poika mau amemene achotsedwa pa mpata umene waperekedwa.

Magawo awiri a chifuniro cha Mulungu ndi chimene chimavumbulutsidwa mu \_\_\_\_\_  
ndi chosavumbulutsidwa mu \_\_\_\_\_

3. Perekani mfundo ya Baibulo imene ikhoza kugwirizana ndi nyengo iyi:

“Ndapalana ubwenzi ndi mzibambo osapulumsidwa. Iye ndi wachifumu komanso ali ndi khalidwe labwino. Ngakhale kuti ine ndi okhulupirira, iye amati palibe vuto kuti ndidzidzapita kutchalitchi ndipo iye akuti akhoza kumadzapita nane. Ndikupephelera chifuniro cha Mulungu pa nkhani imeneyi”

Mfundo ya Baibulo imene ikhoza kugwira ntchito apa ndi:

---

---

---

4. Fotokozani mfundo zisanu ndi ziwiri zimene zatchulidwa mu chaputala chimenechi:

---

---

---

---

---

---

---


5. Kodi chiganizo ichi ndi cholondola kapena ayi: ngati Mulungu analakhula chifuniro chake nkhani ina ya mu Baibulo, ndikofunikabe kuti mufunefunebe chitsikimizo.

Chiganizo chimenechi ndi \_\_\_\_\_

6. Kodi ndi chithunzi chiti chimene chikuonetsera chithunzithunzi chenicheni cha kuchita chifuniro cha Mulungu pa moyo wa okhulupirira.

Chithunzi A

Kubadwa mwatsopano



Chithunzi B



7. Kodi ndi madera ati anayi amene afotokozeredwa ngati chifuniro cha Mulngu mu chaputala ichi

---

---

(Mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

## **ZOONJEZERA POPHUNZIRA**

Mau a Mulungu olembedwa ali ndi mfundo komanso zitsanzo zimene Mulungu akukhula zachifuniro chake pa munthu. Palinso malangizo kapena kuti uphungu pa nkhani zosiyanasiyana umene walembedwa mu Baibulo. Zina mwa izi ndi malonjezano ndi malamulo a Baibulo. Ma vesi ena akuyakhula mwachindunji chifukwa Mulungu akuchita kuneneratu kuti “ichi ndi chifuniro changa.” Ndime zimenezi zaperekededwa ndi cholinga choti mukathe kuzisanthula.

Kodi ndi zinthu zina ziti zimene Mulungu wakuulirani ngati chifuniro chake? Werengani ndime zili munsizi:

### **IYE ALI NDI CHIKONZERO PA INU**

**(Pakuti cifuniro ca Atate wanga ndi ici, kuti yense wakuyang'ana Mwana, ndi kukhulupirira iye, akhale nao moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomariza. Yohane 6:40)**

**Koma cifuniro ca Iye amene anandituma Ine ndi ici, kuti za ici conse Iye anandipatsa Ine ndisatayeko kanthu, koma ndiciukitse tsiku lomariza. (Yohane 6:39)**

**Cinthu conse cimene anandipatsa Ine Atate cidzadza kwa Ine; ndipo wakudza kwa Ine sindidzamtaya iye kunja. (Yohane 6:37)**

**Anatikonzeratu tilandiridwe ngati ana, a iye yekha mwa Yesu Kristu, monga umo kunakomera cifuniro cace, (Aefeso 1:5)**

**Anatizindikiritisa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. Mwa iye tinayesedwa colowa cace, popeza tinakonzekeratu monga mwa citsimikizo mtima ca iye wakucita zonse monga mwa uphungu wa cifuniro cace; (Aefeso 1:9-11)**

**Mwa cifuniro cace mwini anatibala ife ndi mau a coonadi, kuti tikhale ife ngati zipatso zoundukula za zolengedwa zace. (Yakobo 1:18)**

### **CHIFUNIRO CHAKE PA OKONDEKA ANTHU:**

**Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (Petro 3:9)**

**CHIFUNIRO CHAKE KUTI TIKAYERETSEDWE:**

**Pakuti ici ndi cifuniro ca Mulungu, ciyeretso canu, kuti mudzipatule kudama; (1 Atesalonika 4:3)**

**CHIFUNIRO CHAKE PA MAPEMPHERO NDI CHIYAMIKO:**

**Pempherani kosaleka; M'zonse yamikani; pakuti ici ndi cifuniro ca Mulungu ca kwa inu, mwa Kristu Yesu. (1 Atesalonika 5:17-18)**

**(Mateyu 16:19) Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba.**

**CHIFUNIRO CHAKE PAMAKHALIDWE ANTHU:**

**(1 Petro 2:15) Pakuti cifuniro ca Mulungu citere, kuti ndi kucita zabwino mukatontholetse cipulukiro ca anthu opusa;**

**CHIFUNIRO CHAKE PA IFE CHOKHUDZA MZIMU WOYERA:**

**Ndipo kudzali m'masiku otsiriza, anena Mulungu, Ndidzathira ca Mzimu wansa pa thupi liri lonse, Ndipo ana anu amuna, ndi akazi adzanenera, Ndipo anyamata anu adzaona masomphenya, Ndi akulu anu adzalota maloto; Ndiponso pa akapolo anga ndi pa adzakazi anga m'masiku awa Ndidzathira ca Mzimu wanga; ndipo adzanenera. (Macitidwe 2:17-18)**

**CHIFUNIRO CHAKE PAKUCHITIRA UMMBONI:**

**Ndipo Yesu ananena nao, Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzokusandutsani inu asodzi a anthu. (Marko 1:17)**

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)**

#### **CHIFUNIRO CHAKE PA MAKANDA NDI ANA MWAKHRITSU:**

**Comweco siciri cifuniro ca Atate wanu wa Kumwamba kuti mmodzi wa ang'ono awa atayike. (Mateyu 18:14)**

#### **CHIFUNIRO CHAKE PAMAZUZO:**

**Koteronso iwo akumva zowawa monga mwa cifuniro ca Mulungu aike moyo wao ndi kucita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika. (1 Petro 4:19)**

#### **CHIFUNIRO CHAKE PA MOYO WATHU WAMUYAYA:**

**Atate, amene mwandipatsa Ine, ndifuna kuti, kumene ndiri Ine, iwonso akhale pamodzi ndi Ine; kuti ayang'anire ulemerero wanga, umene mwandipatsa Ine; 2 pakuti munandikonda Inelisanakhazildke dziko lapansi. (Yohane 17:24)**

#### **CHIFUNIRO CHAKE PA CHUMA CHAKUTHUPI:**

**Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. (Mateyu 6:33)**

**Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu; muyeso wabwino, wotsendereka, wokucumuka, wosefukira, anthu adzakupatsani m'manja mwanu. Pakuti 7 kudzayesedwa kwa inu ndi muyeso womwewo muyesa nao inu. (Luka 6:38 6)**

## CHAPUTALA 6

### KODI MULUNGU AMALAKHULA BWANJI NDI MUNTHU

#### ZOLINGA:

Pamapeto pa chaputala ichi muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kutchula njira zimene Mulungu amalakhulira ndi munthu.
- Kuzindikira kuti Mulungu alibe malire mukuthekera kwake polakhula ndi munthu

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani.  
(Aefeso 5:17)**

Monga mmene tinakambira pachiyambi cha phunziro limeneli, Baibulo ndi mbiri ya mmene Mulungu analakhulira ndi munthu komanso mmene munthu anachitira atamva kulankhula kwa Mulungu. Chaputala ichi chifukula Baibulo ndi cholinga choti tione njira zimene Mulungu anagwiritsa ntchito pofuna kulakhula ndi ndi munthu.

#### MAU A MULUNGU OLEMBEDWA

Tinaona kale muphunziro lina kuti Mulungu amalakhula ndi munthu kudzera mu Mau ake olembedwa. Kotero sikoyeneranso kuti Mulungu ayankhulenso pa zinthu zimenezi. Pamene Mulungu wagwiritsa ntchito njira zina pofuna kulankhula chifuniro chake, sipamakhala kutsutsana kwina kulikonse ndi Mau ake olembedwa.

#### PEMPHERO

Pali zitsanzo zambiri mu Baibulo zimene Mulungu analakhula chifukwa cha Pemphero ndi kusala kudya (kusadya chakudya pazifukwa zauzimu) zinapangitsa kuti Mulungu alankhule ndi Paulo ndi Banabasi.

**Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako. Pamenepo, m'mene adasala cakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke. (Macitidwe 13:2-3)**



Mumapemphero athu, tiyenera kupempha Mulungu kuti akwaniritse chifuniro chake padziko lapansi. Yesu Khristu anaphunzitsa ophunzira ake kupemphera.

**Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kucitidwe, monga Kumwamba comweco pansu pano. (Mateyu 6:10)**

Yesu asanasankha ophunzira ake, Iye anapemphera kufuna chitsogozo kuchokera kwa Mulungu.

**Ndipo kunali masiku awa, iye anaturuka nanka kuphiri kukapemphera; nacezera usiku wonse m'kupemphera kwa Mulungu. Ndipo kutaca, anaitana ophunzira ace; nasankha mwa iwo khumi ndi awiri, amene anawachanso dzina lao atumwi: (Luka 6:12-13)**

Imfa yake isanifike, Yesu apemphelera chifuniro cha Mulungu.

**Nati, Atate, mukafuna Inu, cotsani cikho ici pa Ine; koma si kufuna kwanga ai, komatu kwanu kucitike. (Luka 22:42)**

#### **APHUNGU**

Mulungu amathanso kuyankhula chifuniro chake kudzera mwa aphungu. Pali zotsanzo zambiri zoonetsera anthu akufuna upungu kuchokera kwa anthu a Mulungu.

**Popanda upo wanzeru anthu amagwa; Koma pocuruka aphungu pali cipulumutso. (Miyambi 11:14)**

#### **NYENGO ZAMOYO**

Mulungu amatha kuyankhula kudzera munyengo zathu. Chitsanzo chabwino kwambiri mu Baibulo ndi moyo wa Yesefe (Genesis 37:50)

Ngakhale kuti abale ake anamugulitsa iye kuukapolo ku Aigupto, iwo sanadziwe kuti ichi chinali chifuniro cha Mulungu:

**Tsopano musaphwetekwe mtima, musadzikwiwira inu nokha, kuti munandigulitsira ine kuno, pakuti Mulungu ananditumiza ine patsogolo panu kuti ndisunge moyo. (Genesis 45:5)**

Kudzera munyengo zimene Yosefe anakumana nazo, Palibe chimene iye anakachita, koma Mulungu anamugwiritsa tchito populumutsa miyandamiyanda ya anthu kuchilala.

Paulo analemba mau opatsa chidwi pa 1 Atesalonika 2:18. Iye anafotokoza akhristu aku Tesalonika kuti anakanika kuwayendera iwo chifukwa Satana anamutchinga iye. Chifukwa chakuti sanakhatha kuwayendera, iye analemba mpingo waku Tesalonika. Kulembedwa kwa buku limeneli kunali zotsatira zakutchinga kwa Satana. Komabe izi zinabweretsa zotsatira zazikulu zimene mwina sizikanatha kubwera anakakhala kuti iye anawayendera anthu amenewa. Ndipo uthenga umeneu waperekedwanso kumibadyo yosiyanasiyana kuti okhulupirira akapindule.

Palibe chinthu chimene chimachitika Mulungu osadziwa. Ngakhale nyengo zotchinga chifuniro cha Mulungu, Mulungu amakhala kuti akulamulirabe. Mulungu akhoza kugwiritsa ntchito nyengo ina iliyonse kaya yochokera kwa Satana ndi kuyingwiritsa ntchito pofuna kukwaniliritsa chifuniro chake. Pali lonjezo la Mulungu lodabwitsa lokhudza nyengo zathu:

**Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace. (Aroma 8:28)**

Tiyenera kusamlitsa pogwiritsa ntchito nyengo zathu ngati njira yodziwira chifuniro cha Mulungu. Mwachitsanzo, Mulungu anauza mneneri otchedwa Yona kuti akalalike ku mzinda wa Nenevi. Koma iye atafika kudoko, anasankha zopita dera lina chifukwa ngalawa imene anapeza inali yopita ku Talisi ndipo iye anaona ichi ngati chifuniro.

Nyengo zathu zamoyo zinayenera kulumikazana ndi njira zina zimene Mulungu amagwiritsa ntchito. Mulungu anali atayankhula kale ndi Yona, koma Yona anasinthana Nyengo zake kuti zigwirizane ndi zofuna zake.

## **ZITSEKO ZOTSEKUKA NDI ZOTSEKEKA**

Zotsatira za nyengo za moyo zimatchedwa zitseko “zotseguka ndi zotsekeka” Paulo anafotokoza mu buku la Akorinto:

**Koma ndidzakhala ku Efeso kufikira Penteskoste, Pakuti panditsegukira pa khomo lalikuru ndi locititsa, ndipo oletsana nafe ndi ambiri. (1 Akorinto 16:8-9)**

Khomo lotsekeka silimanthauza kuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Sizimanthauzo kuti sichifuniro cha Mulungu kuti Iye achitepo kanthu. Koma mukupita kwa nthawi, Paulo anakwanitsa Kufalitsa Uthenga Wabwino. Mulungu amakhala akukutsogolerani pamene khomo latsekeka. Iye amakhala kuti akutsogolerabe pamene khomo latsekuka ndi kutsekeka. Nthawi zina khomo limatsekeka chifukwa sinthawi yake Yoyenera mu dongosolo la Mulungu. Mukupita kwanthawi, Khomo lotsekeka lija limatsekuka.

## ANGELO

Loti anapatsidwa chitsogozo ndi Angelo amene anamuonekera kunyumba kwake ku Sodomu. Iye anauzidwa kuti asamuke munzinda wa Sodomu chifukwa Mulungu amafuna kuononga mzida umeneu (Genesis 19) Mngelo wa Mulunngu analakhula ndi Filipino ndikumuuza kuti apite ku Samariya (Machitidwe8:26). Kubadwa kwa Yohane M'batizi ndi Yesu Khristu kunalengezedwa ndi angelo (Luka1)

Pali zitsanzo zambirimbiri mu Baibulo zimene angelo akupereka chifuniro cha Mulungu kwa munthu. Mwainu nokha mukhoza kupeza zitsanzo zina mu Baibulo.

## ZOZIZWITSA

Chozizwa ndi chinthu chodabwitsa chazimu chimene munthu sangathe kukwanitsa kuchita.

Pa 1 Mafumu Chaputala cha 1 Mulungu anagwiritsa ntchito zozizwa kuti alakhule chifuniro chake. Mneneri Eliya anauzidwa kuti akonze gome pamaso pa Mulungu ndipo iye anakonza gome anafuula:

**Ndipo kunali, nthawi ya kupereka nsembe yamadzulo, Eliya mneneri anasendera, nati, Yehova Mulungu wa Abrahamu ndi Isake ndi Israyeli, lero kudziwike kuti Inu ndinu Mulungu wa Israyeli, ndi ine mtumiki wanu, kuti mwa mau anu ndacita zonsezi. Ndimvereni Yehova, ndimvereni, kuti anthu awa adziwe kuti Inu Yehova ndinu Mulungu, ndi kuti Inu mwabwezanso mitima yao. Pamenepo moto wa Yehova unagwa, nutentha nsembe yopsereza, ndi nkhuni, ndi miyala, ndi pfumbi, numwereretsa madzi anali mumcera. Ndipo anthu onse anaona, nagwa nkhope zao pansu, nati, Yehova ndiye Mulungu, Yehova ndiye Mulungu. (1 Mafumu 18:36-39)**

Mulungu anagwiritsa ntchito chodabwitsa ndi cholinga choti alankhule kwa anthu amene amapembedza mafano komanso ndikudzionetsera yekha ngati Mulungu yekhayo weniweni.

Mulungu anaonetseranso chifuniro chake kudzera mu zodabwitsa pachilengedwe. Moto ndi mtambo umapereka chitsogozo cha mmene ana a Israeli amayenera kuyendera usana ndi usiku pamene anali kuyenda muchipulu.

**Ndipo Yehova anawatsogolera usana ndi mtambo njo kuwatsogolera m'njira; ndi usiku ndi moto njo, wakuwawalitsira; kuti ayende usana ndi usiku; sanacotsa mtambo usana, kapena mtambo wamoto usiku, pamaso pa anthu. (Eksodo 13:21-22)**

**Mukhoza kupeza zitsanzo zina mu Baibulo zimene Mulungu analankhula chifuniro chake kudzera muzozizwa. Yang'anirani izi pamene muwerenga Baibulo.**

### **MALOTO**

Mulungu amafunitsitsa kuti adzilankhula nafe ngakhale titagona, Iye amalankhula nafe. Mulungu amalankhula kudzera m'maloto. Pali maloto ena apadera amene siwina aliyense amene angalote. Awa ndi maloto amene amachokera kwa Mulungu ndipo amakhala achindunji ndipo amaulula chifuniro cha Mulungu.

Zina mwazitsanzo zopezeka mu Baibulo ndi izi:

- Mulungu anamuchenjeza Abimaleki kudzera mumaloto pa tchimo lake lotenga mkazi wa Abrahamu, Sara (Genesis 20:3)
- Mngelo wa Mulungu anamukumbutsa Yakobo za pangano limene anapanga ndi Mulungu kudzera mumaloto. (Genesis 31:11-13)
- Mulungu anagwiritsa ntchito maloto pofuna kuonetsera chifuniro chake kwa Yosefe (Genesis 37).
- Mulungu anonekera kwa Solomoni kudzera kumaloto ndipo anampatsa mwayi oti apemphe chimene akukhumba. 1 Mafumu 3:5.
- Loto linaperekedwa kwa anzeru akum'mawa kuti adzere njira ina pobwelera kwao chifukwa cha upo la mfumu (Mateyu 2:12-13).

Izi ndi zitsanzo chabe dzochepa zoonetsera mmene Mulungu analankhulira kudzera kumaloto. Mukhoza kupeza zitsanzo zina zapadera powerenga nokha Baibulo.

### **Masomphenya**

Masomphenya ndi ofanana ndi maloto koma kusiyana kwake ndi kwakuti masomphenya ali ngati kukhala ndi maloto koma ukadali mmanso. Masomphenya akhoza kuonedwa ndi maso akuthupi kapena maso auzimu. Izi zikutanthauza kuti mukhoza kusaona zinthu ndi maso athu, koma Mulungu amapereka chithunzithunzi mkati mwa mzimu wanu.

Zina mwazitsanzo zoonetsera mmene Mulungu analankhulira pogwiritsa ntchito masomphenya ndi izi:

- Mulungu analakhula kwa Abrahamu kudzera mumaloto ndipo anampatsa malonjezano akulu. Genesis 15.

- Buku la Danieli ladzala ndi masomphenya komanso maloto. Mulungu anagwiritsa ntchito izi pofuna kuonetsera zinthu zambiri zamtsolo. Ndipo Iye analakhula mwa aneneri ambiri a Chipangano chakale kudzera mumasomphenya.
- Mulungu anamuonetsera Peturo kufunika kolalika uthenga kwa anthu Amitundu pogwiritsa ntchito masomphenya. Machitidwe 10.
- Mulungu anamuitana Paulo ku Makedoniya kudzera mumasomphenya. Machitidwe 16:9.
- Mulungu anamulakhula Paulo usiku kudzera mumasomphenya. Machitidwe 18:9-10.
- Buku lomaliza la M'baibulo ndi masomphenya amene Mtumwi Yohane anaona.

### **MAU OMVEKA**

Mulungu analankhula ndi mau omveka ndi Paulo panjira ya Kudamasiko. Mukhoza kuwerenga nkhani imeneyo pa Machitidwe 9.

**Ndipo anagwa pansu, namva mau akunena naye, Saulo, Saulo, Undilondalonderanji? Koma anati, Ndiouyani Mbuye? Ndipo anati, Ndine Yesu amene umlondalonda; (Machitidwe 9:4-5)**

Mulungu analankhulanso kwa Saulo ndi mau omveka:

**Ndipo Yehova anabwera, naimapo, namuitana monga momwemo, Samueli, Samueli. Pompo Samueli anayankha, Nenani, popeza mnyamata wanu akumva. (1 Samueli 3:10)**

Baibulo lili ndi mau ambiri onena kuti “ndipo Mulungu anati” ndipo nthawi zina limafotokoza kuti “Mulungu analakhula” kapena “kulamula.” Zonsezi zikungoonetsera kuti Mulungu amalankhula kugwiritsa ntchito mau omveka. Koma pali mau ena amene Mulungu anagwiritsa ntchito:

### **KULANKHULA KWA MZIMU WOYERA MKATI MWA MUNTHU.**

Nthawi zambiri, Mulungu amagwiritsan ntchito kulankhula kwa Mzimu Woyera mkati mwa anthu. Ndipo izi zimatchedwa kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

**Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu, (Aroma 8:14)**

Kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera kumatanthauza kuti otsegozedwao ayenera kukhala moyo wauzimu. Moyo wakufa muuchimo komanso opanda moyo wauzimu sungatsogozedwe ndi Mzimu Woyera. Kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera kumatanthauza kuti simungathe kuyenda panonkha m'moyo wanu ngati mmene tinaonera mu chaputa chapitachi.

Pamene mwapadwa mwatsopano, Mulungu amakupatsani mzimu wake umene Umakhala okonzeka kulandira zimene Iye akulakhula.

**Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga m'kati mwanu mzimu watsopano; ndipo ndidzacotsa mtima wamwala m'thupi, ndi kukupatsani mtima wamnofu. Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwanu, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwacita. (Ezekieli 36:26-27)**

Pamene mutsogozedwa ndi Mzimu Woyera, chifuniro cha Mulungu chimavumbulutsidwa ndi Mzimu Woyera mkati mwa mzimu wanu. Umodzi mwa mautumiki a Mzimu Woyenera ndi chitsogozo ngati mmene ndime iyi ikufotokzera:

**Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse; pakuti sadzalankhula za iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani. (Yohane 16:13)**

Mzimu wa munthu ndi “munthu obisika mumtima” amene akutchulidwa pa (1 Peturo 3:4) Pamene Mulungu akulankhula ndi munthu wamkati, Iye amakhala kuti akulankhula ndi Mzimu wanu. Olemmba buku la Miyambo akufotokoza kuti mzimu wa munthu ndiwo nyali ya Yehova.

**Mzimu wa munthu ndiwo nyali ya Yehova; Usanthula m'kati monse mwa mimba. (Miyambi 20:27)**

Nthawi ina Paulo ali pa Ulendo wapangalawa, iye anachenjeza Kenturiyo wangalawayo nati:

**Nanena nao, Amuna inu, ndiona ine kuti ulendo udzatitengera kuonongeka ndi kutayika kwambiri, si kwa akatundu okha kapena ngalawa yokha, komatunso kwa moyo wathu. (Macitidwe 27:10)**

Sikuti Paulo ananena kuti ndamva mau. Iye sananene kuti “ndaona masomphenya” kapena kulota maloto. Koma mzimu wake umachitira umboni mzimu wa Mulungu ndipo umboni umeneu unali olondola.

Muyenera kuphunzitsa mtima wanu kuti uyenera kukhala watchelu ndi Mulungu. Nthawi yambiri imaperekedwa kuchita masewera olimbitsa thupi, kukozenkeretsa maganizo athu kudzera mumasewero. Koma, nthawi yochepa chabe imaperekedwa kuti tikuze moyo wathu wauzimu. Mzimu wanu ukhoza kuphunzitsidwa chimodzomodzi mmene maganizo anthu amaphunzilira. Mzimu wanu ukhoza kukula ndi mphamvu ngati mmene thupi lamuthu likulira kudzera kuchita zamasewera. Mukhoza kuphunzitsa mtima wanu pakulingalira Mau a Mulungu.

**Buku ili la cilamulo lisacoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kucita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. (Yoswa 1:8)**

Mulungu amathanso kugwiritsa ntchito mau olankhulidwa mkati mwathu ndi Mzimu Woyera pofuna kutipatsa ife chikumbumtima. Chikumbumtima ndi kuzindikira choipa ndi chabwino mkati mwathu chimene Mulungu anatipatsa.

*Mnene munthu amamvera* ndi mau amene thupi limalakhula. Mulungu samagwiritsa ntchito mmene tikumvera pofuna kutilankula. Izi zili chomwechi chifukwa thupi lathu ndi mdani wa Mzimu. Ndi zofuna zathupi kapena mmene thupi lathu likumvera zikhoza kutipusitsa.

*Kuganiza* ndi mau ochokera mmalingalirao athu. Njira za Mulungu ndi zosemphana ndi kuganiza kwa munthu.

Chikumbumtima ndi mau a mzimu wa munthu amene amatitsutsa ndi kutitsogoza kuti tichite chifuniro chagwiro cha Mulungu. Mzimu Woyenera amayankhula kwa mzimu wathu ndikutsutsana ndi chikumbumtima chathu. Izi zimatithandizira kuti tichite chifuniro cha Mulungu. Pamene Mzimu Woyera walankhula ndi mzimu wathu, chikumbumtima chathu chimatsutsika. Koma ngati mungapitirize kunyalanyaza zimene chikumbumtima chathu, mtima wathu umaumitsidwa kapena kuti chikumbumtima chathu chamakhala chosamvaso kutsutsika ndi Mzimu Woyera.

**Oloedwa m'cikumbu mtima mwao monga ndi citsulo camoto; (1 Timoteo 4:2)**

Buku la Miyambo lili ndi ma vesi ambiri amene amaonetsera kuti Mulungu ndiye adziwa mtima ndi chikumbumtima cha munthu.

**Malongosoledwe a mtima nga munthu; Koma mayankhidwe a lilime acokera kwa Yehova. (Miyambi 16:1)**

**Mtima wa munthu ulingalira njira yace; Koma Yehova ayendetsa mapazi ace. (Miyambi 16:9)**

**Mtima wa mfumu uli m'dzanja la Yehova ngati mitsinje ya madzi; Aulozetsa komwe afuna. (Miyambi 21:1)**

### **MPHATSO ZA MZIMU WOYERA**

Mphatso za Mzimu Woyenera zimagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu pofuna kulankhula ndi munthu ndipo mphatso zimenezi ndikuthekera kwapaderadera kumene kumaperekedwa ndi Mzimu Woyera. Zambiri mwa mphatso zimenezi zimathandiza muthu kuti alumikizane ndi Mulungu.

Mphatso ya malilime imagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu pofuna kulankhula ndi munthu mu chilankhulo chimene iye samachidziwa. Izi zimatengera kutanthauzira malilime kucholera kwa Mulungu mwini. Chinenero cha pemphero la Mzimu Woyenera chimagwira ntchito yothandizira kuchita chifuniro cha Mulungu. Ngati simukudziwa mmene mungapempherere kuti muzindikire chifuniro cha Mulungu, ingopempherani mu Malilime.

**Ndipo iye amene asanthula m'mitima adziwa cimene acisamalira Mzimu, cifukwa apempherera oyera mtima monga mwa cifuno ca Mulungu. (Aroma 8:27 )**

Palonso mphatso ya Uneneli imene ndi chotengera cha uthenga ochokera kwa Mulungu kupita kwa anthu ake. Mphatso ina ndi yachidziwitso imene mulungu amayingwiritsa ntchito pofuna kuonetsera mzimu umene ukugwira ntchito mwa anthu ena. Mulungu amathanso kuyankhula pogwiritsa ntchito mzimu, luntha ndi chidziwitso. Mphatso zimenezi zimepereka chidziwitso chazimu chimene sitingachizindikire ndi maganizo athu akuthupi.

### **NJIRA ZINA NDI ZINA**

Njira ziwiri zina zodziwira chifuniro cha Mulungu ndi kuchita meyere kapena kugwiritsa ntchito chikopa. Taona kale njira zimenezi phunziro la mbuyomu kuti njira yochita mayera inagwiritsidwa ntchito Mzimu Woyera asanaperekedwe. Koma Mzimu Woyera atangoperekedwa, simaonetseredwanso kuti imagwira ntchito. Izi zili chimwechi chifukwa ndi utumiki wa Mzimu Woyera kupereka chitsogozo. Chikopa chinangotchulidwa kamodzi kokha mu Baibulo ndi Gideon. Ichi chinali chizindikiro cha chozizwitsa chimene chinagwiritsidwa ntchito pofuna kupereka chitsikimizo osati chitsogozo.



## MULUNGU ALIBE MALIRE

Mulungu samagwiritsa njira zomwe zomwezo pofuna kulankhula. Chifukwa cha ichi, timamuikira Mulungu malire ngati tingaike njira zokhazikika zimene iye amagwiritsa ntchito pofuna kuyankhula chifuniro chake. Mulungu wakhala akulankhula ndi munthu pogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana. Iye alibe malire pa njira zimene amagwiritsa ntchito pofuna kuyankhula chifuniro chake. Wonani zitsanzo ziri munsimuzi.

### **Mose:**

Munthawi imene Mose anali kutsogolera ana a Isreali muchipulu kupita kudziko lamalonjezano, Mulungu anawalonjeza iwo madzi. Nthawi ina Mulungu anamuuza Mose kuti amenye thanthwe ndi ndodo yake ndipo atachita izi, madzi anatuluka. Nthawi zina Mulungu anauza mose kuti alakhule kwa thanthwe. Koma iye anamenya thanthwe ngati mmene anachitira pachiyambi. Izi sizinamukondweretse Mulungu ndipo chilango chinaperekedwa kwa Mose. Nkhani imeneyi ikutsindikira kufunika kodikira kumva chitsogozo kuchokera kwa Mulungu ngakhale tikukumana ndi nyengo yachizolowezi. Mulungu samagwira ntchito mwachizolowezi cha mmene wakhala akuchira mbuyo.

Mwina mukhoza kuona ngati kuti Mulungu sanachite chilungamo pomulanga Mose chifukwa cha chinthu chaching'ono chimene anachita. Mwala umene amayenere kuulankhula unali ndi tanthuazo lapadera. Umayimira Ambuye wathu Yesu Khristu ngati madzi amoyo amene aneperekedw chifukwa cha imfa yake. Yesu anaphedwa kamodzi chifukwa cha onse. Chotere panalibenso chifukwa choti amenyedwenso (kumphedwa) kachiwiri. Tanthauzo lobisika la kumenya tanthwe ndi limene linapangitsa kuti kulakwitsa kwa Mose kukhale kwakukulu.

### **ELIYA:**

Mulungu anagwiritsa ntchito njira zambiri zodabwitsa pofuna kulankhula ndi mneneri Eliya. Nthawi ina Mulungu anauza Eliya kuti akayime pamphiri ndikudikira kuti Mulungu amulankhule. Izi ndi zimene zinachitika:

**Ndipo iye anati, Turuka, nuime pa phiri tino pamaso pa Yehova. Ndipo taonani, Yehova anapitapo, ndi mphepo yaikuru ndi yamphamvu inang'amba mapiri, niphwanya matanthwe pamaso pa Yehova; koma Yehova sanakhala m'mpheapomo. Itapita mphepoyo kunali cibvomezi; komanso Yehova sanali m'cibvomezico. Citaleka cibvomezi panali moto; koma Yehova sanali m'motomo, Utaleka mota panali bata la kamphepo kayaziyazi. (1 Mafumu 19:11-12)**

Pali zinthu zingapo zodabwitsa zauzimuz zimene zikutchulidwa munkhani iyi. Panali zinthu zingapo mphepo, moto ndi chivomerezi. Izi zinali zinthu zimene Mulungu anagwiritsa ntchito mbuyomo pofuna kulankhula ndi Eliya. Koma nthawi imeneyi, Mulungu analankhala mkati mwa mzimu wake ndi mau ang'ono amene mwina anali omveka ndi makutu kapena ayi.

### **PAULO:**

Pali njira zambiri zimene Mulungu anagwiritsa ntchito pofuna kupereka chitsogozo pa utumiki wa Paulo:

- Pa njira ya Damasiko, Mulungu anagwiritsa ntchito kuwala kwakukulu ndi mau pofuna kulankhula ndi Paulo. Machitidwe 9:1-8.
- Pamene chiwembu chinakonzedwa kuti iye aphedwe, iye anachenjezedwa ndi okhulupirira amene Mulungu anawagwiritsa ntchito kumuthandizira kuthawa. Machitidwe 9:20-25.
- Banaba agwiritsidwa ntchito ndi Mulungu pokhazikitsa ubale pakati pa iye ndi atumwi ena. Machitidwe 9:20-28.
- Okhulupirira anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kuti apulumutse Paulo kwa Ahelene okwiya. Machitidwe 9:29-30.
- Paulo atakumana ndi wanyanga, Mulungu anampatsa iye chitsogozo kuti wanyangayo akamasulidwe. Machitidwe 13:2-4.
- Pemphero ndi Mzimu Woyera zinamutsogolera Paulo kuchita utumiki ofalitsa Uthenga Wabwino. Machitidwe 13:2-4.
- Uneneri ochokera kwa mneneri unamuchenjeza Paulo zachizuzo chimene Paulo adzakumane nacho Ku Yerusalemu. Machitidwe. 21:10-14.
- Mulungu analankhula ndi Paulo kudzela kumaloto ndi masomphenya. Machitidwe 26:19; 27:23-24
- Khomo lalikulu la utumiki litatseguka, Paulo anasintha maganizo ake a Utumiki. I Akorinto 16:8-10.

### **FILIPO:**

**Koma mngelo wa Ambuye analankhula ndi Filipo, nanena, Nyamuka, nupite mbali ya kumwela, kutsata njira yotsika kucokera ku Yerusalemu kunka ku Gaza; ndiyo ya cipululu. Ndipo ananyamuka napita; ndipo taona munthu wa ku Aitiopiya, mdindo wamphamvu wa Kandake, mfumu yaikazi ya Aaitiopiya, ndiye wakusunga cuma cace conse, amene anadza ku Yerusalemu kudzapemphera; ndipo analinkubwerera,**

**nalikukhala pa gareta wace, nawerenga mneneri Yesaya. Ndipo Mzimu anati kwa Filipino, Yandikira, nudziphatike ku gareta uyu. (Macitidwe 8:26-29)**

Kunthawi yoyamba, Mulungu analankhula ndi Filipino kudzera kwa mngelo. Kachiwiri analakhula naye kudzera mwa Mzimu Woyera ndipo Filipino sanazengeleze koma kuchitapo kanthu. Iye sanadikirensa chitsikimikizo kuchokera kwa mngelo potengera kuti pachiyambi ndi amene analakhula naye.

**DAVIDE:**

Pamene Mfumu Davide anali wachichepere analimbana ndi mdani wa anthu a Mulungu otchedwa Goliyati. Goliyati anali chiphona komanso anali ndi zida zachikwanekwane, koma Mulungu anauza Davite kuti asagwiritse ntchito zida zimene anthu amagwiritsatsa ntchito pomenya nkhondo. Koma mmalo mwake, Davide anagwiritsa ntchito legeni ndi mwala. Ndi mwala umodzi okha, Davide agwetsa mdani wa anthu a Mulungu. Koma mukupita kwa nthawi, Davide akanaphwedwa ndi chiphona china, koma iye anapulumutsidwa ndi munthu otchedwa Abishayi. Kodi tikhoza kunena kuti Mulungu anali ndi mfumu Davite pamene iye anagonjetsa Goliyati ndipo kuti Mulungu sanali ndi iye pamene amafuna kumphedwa ndi chimphonachi? Ayi sichonchi, koma kuti Mulungu anagwiritsa ntchito njira zosiyana. Nthahwi yoyamba ija, Mulungu anagwiritsa ntchito ukadaulo wa Davite ogwiritsa ntchito legeni ndipo kachiwiri Mulungu anagwiritsa ntchito ukadaulo wankhondo wa Abisha.

Pamene Mulungu wasankha kuti asalankhule nanu ngati mmene amachitira kale, simuyenera kukhula okhumudwa. Ngati chifuniro chake munyengo imene mukudutsamo sichikufanana ndi zimene munakumana nazo, simukuyenera kukhala osokonekera. Izi zili chimwechi chifukwa Mulungu samagwiritsa ntchito njira zokhazikika pofuna kulankhula. Mulungu wamkuluyo njira zake zolumikizirana ndi Munthu m'chifuniro Chake ndi zopanda Malire.

**MAYESO ODZIYESA NOKHA.**

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

---

---

2. Perekani chitsanzo chimodzi chimene chagwiritsidwa ntchito mu muphuziro ili choometsera kuti mulungu alibe malire anjira zimene amagwiritsa ntchito polankhula.

---

---

3. Tchulani njira khumi ndi ziwiri zimene zakambidwa mu chaputala ichi zomwe Mulungu amagwiritsa ntchito kulankhula ndi munthu.

---

---

---

---

---

---

4. Werengani chiganizo ichi. Lembani T kutsogolo kwachiganizo ngati chiganizocho m'choona. Ngati chiganizocho chili chosalondola, lembani F Kutsogolo kwachiganizo.
- a. \_\_\_\_\_ Ngati mwakumana ndi chitseko chotsekeka, zimatanthaua kuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu.
  - b. \_\_\_\_\_ Yesu sanapempherere chifuniro chaambuye chifukwa amachidziwa kale.
  - c. \_\_\_\_\_ Yosefe anaona ngati nyengo zake sizinali zabwino ndipo analimbana nazo.
  - d. Nyengo zathu ndiye njira yabwino yozindikira chifuniro cha Mulungu.
  - e. \_\_\_\_\_ Yona anasintha nyengo zake ndi cholinga chofuna kukwanilitsa zolinga zake osati za Mulungu.
  - f. \_\_\_\_\_ Njira zina za Mulungu zolakhulira chifuniro chake sizimasemphana ndi Mau ake olembedwa.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku illi)

## ZOONJERA POPHUNZIRA

1. Werengani mapemphero awa ngati chitsogozo.

Salimo 25:4

Akolose 1:9

Salimo 86:11

Akolose 4:12

Aefeso 6:18-20

2. Mulungu amalankhula chifuniro chake koma munthu amathamangira kupanga ziganizo. Werengani zitsanzo za anthu amene anachita zinthu mwachangu posamulola Mulungu kuti alankhule chifuniro chake kwa iwo.

Kupha mu Igupto kwa Mose: Eksodo 2.

Gwirizano wa Yoswa ndi a Gibeoni Yoswa 9

Abarhamu ndi Ishimaeli: Abrahamu sanadikilire mwana olonjezedwa: Genesis 16.

3. Werengani Buku la Machitidwe ndipo tchulani njira zimene Mulungu anagwiritsa ntchito pofuna kulankhula chifunira chake kwa anthu mu mpingo oyambilira.

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

## CHAPUTALA 7

### CHITSAMBA CHOYAKA MOTO CHOSANYEKA

ZOLINGA:

Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi.

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kutchula njira zopezera chifuniro cha Mulungu.
- Kufotokoza mmene mungakhalire ndi chitsikimizo cha chifuniro cha Mulungu.
- Kupeza msanamira zitatu kuti mulandire chitsogozo kuchokera kwa Mulungu.

### VESI YOTSOGOLERA

**Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, Osacirikizika pa luntha lako;  
Umlemekeze m'njira zako zonse, Ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako.  
Miyambo 3:5-6**

### MAU OYAMBA

Mu chaputala chapitachi, tinasanthula umboni opezeka mu Baibulo umene ukuonetsera mmene Mulungu analankhulira ndi munthu kalero. Koma funso mkumati, kodi Mulungu akulakhalabe ndi anthu lero lino?

Mtumwi Paulo anafotokoza:

**KALE Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyana-siyana, koma pakutha pace pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe; (Ahebri 1:1-2)**

Mulungu analankhula ndi munthu kugwiritsa ntchito njira zambiri. Ndipo iye anapitilirabe kulankhula ndi anthu mu nthawi ya Paulo amene anafotokoza kuti uthenga waukulu ochekera kwa Mulungu ndiye ochokera kwa Mwana wake Yesu Khristu.

### NTHAWI YAKALE: CHITSAMBA CHOYAKA MOTO

Mulungu analankhula chifuniro chake pogwiritsa ntchito njira zambiri. Chimodzi mwazitsanzo zimenezi chikupezeka pa Eksodo chaputala 3:

**Koma Mose analikuweta gulu la Yetero mpongozi wace, wansembe wa ku Midyani; natsogolera gululo m'tsogolo mwa cipululu, nafika ku phiri la Mulungu, ku Horebe.**

**Ndipo mthenga wa Mulungu anamuonekera m'cirangali camoto coturuka m'kati mwa citsamba; ndipo anapenya, ndipo taonani, citsamba cirikuyaka moto, koma cosanyeka citsambaco. Ndipo Mose anati, Ndipatuketu, ndikaone cooneka cacikuruco, citsambaco sicinyeka bwanji, Pamene Yehova anaona kuti adapatuka kukapenya, Mulungu ali m'kati mwa citsamba, anamuitana, nati, Mose, Mose. Ndipo anati, Ndiri pano. (Eksodo 3:1-4)**

Kudzera muchitsamba choyaka moto koma osanyeka, Mulungu anamuitana Mose ndi cholinga choti akapululumutse ana a Israeli ku nsinga za ukapolo kwa Igupto. Indedi Mulungu analankhula kwa munthu nthawi yakale.

### **MASIKU A LERO: CHITSAMBA CHIKUYAKABE**

Kodi Mulungu akulankhulabe kugwiritsa ntchito zozizwitsa zimene anagwiritsa ntchito kalero? Kodi njira zimenezi zimagwira ntchito mu Chipangano Chakale chokha kulekeza munthawi imene Mzimu Woyera anaperekedwa?

Chitsamba chija chikuyakabe! Koma sikuti mukhoza kulandira chitsogozo kuchokera kwa Mulungu kudzera munjira yofanana ndi imene Mulungu analankhulira ndi Mose. Koma nkhani ndi yakuti Mulungu akulankhulabe ndi munthu kudzera muzozizwitsa ngati mmene anachitira mu Chipangano Chakale.

Pa Ahebri 1:1-2, Paulo akufotokoza kuti Mulungu akulankhulabe ndi dziko lonse kudzera mwa Khristu Yesu. Mulungu sakungolankhula kokha kudzera mu Mau olembedwa mu Baibulo, koma Yesu analonjeza:

**Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse; pakuti sadzalankhula za iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani. (Yohane 16:13)**

Mzimu Woyera akupitilirabe kulankhula uthenga wa Mulungu kudzera mwa Khristu Yesu.

Mzimu Woyera atatsika patsiku la Pentekoste pa Machitidwe 2, mavumbulutso apadera anapitilirabe kulankhulabe ngati mmene amachitira mu Chipangano Chakale. Anthu anali kulota maloto, kuona masomphenya, kulankhula ndi angelo ndi njira zina zambiri zodabwitsa zimene Mulungu anagwirita ntchito.

Kugwiritsa ntchito zozizwitsa sikunaima chifukwa cha kubwera kwa Mzimu Woyera. Koma Mzimu Woyera anagoonjezera gawo lina lachitsogozo. Ena mwa magawo anaonjezedwa ndi kulankhulidwa mkati mwa mzimu wathu, kupembedzera molingana ndi chifuniro cha Mulungu pogwiritsa ntchito pemphero la zinenero zina.

Buku lomaliza mu Baibulo, Chivumbulutso ndi masomphenya amene Mulungu anapereka kwa mtumwi Yohane.

Mulungu akupitilira kulankhulabe lero lino pogwiritsa ntchito njira zimenezi. Molingana ndi mbiri ya mpingo wa lero lino, pali maumboni odziwika bwino lomwe owonetsera kuti Mulungu akulankhulabe pogwiritsa ntchito zozizwitsa. Izi zili chomwechi chifukwa:

**Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse. (Ahebri 13:8)**

### **NANGA NGATI PALIBE CHITSAMBA?**

Nanga chingachitike ndi chiyani zitakhala kuti Mulungu sakukulankhulani kugwiritsa ntchito njira ya zozizwitsa? Kodi nanga zitakhala kuti iye sakulankhula nanu kudzera mumaloto, masomphenya, mau omveka, kapena kudzera mphatso yauzimu ya uneneri. Nanga zitakhala kuti palibe chitsamba chikuyaka moto?

Anthu ena amakhala akudikira kulandira mavumbulutso auzimu kuchokera kwa Mulungu. Anthu ambiri okhulupirira amaononga nthawi yawo yambiri osachitapo kanthu uku akudikirira uthenga odabwitsa ochokera kwa Mulungu.

Mpingo woyamba sunachite izi, iwo anali okondwera pamene Mulungu anali kuwatsogolera kugwiritsa ntchito zozizwitsa. Ziganizo zao zambiri zimene anapanga sikuti anadikira kuti alandire chitsogozo kudzera mumaloto, angelo ndi masomphenya. Koma iwo anayendabe ngati mphamvu yaikulu ya Mulungu.

Ndiye mungapange bwanji ngati palibe chitsamba choyaka? Izi ndi njira zisanu ndi ziwiri zimene mungawiritse ntchito kuti mudziwe chifuniro cha Mulungu.

#### **1. Pempherani:**

Muyenera kupempherera chitsogozo cha Mulungu pa moyo wanu. Yesu Khristu anaphunzitsa ophunzira ake chitsanzo chakapempheredwe chimene gawo lina linali loti apemphere kuti chifuniro cha Mulungu chichitike.



**Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kucitidwe, monga Kumwamba comweco pansipano. (Mateyu 6:10)**

Pamene mupemphera, pemphani Mulungu kuti akuonetsereni chifuniro chake ngati mmene anachitira mose:

**Ndipo tsopano, ngati ndapeza ufulu pamaso panu, mundidziwitsetu njira zanu, kuti ndikudziweni, ndi kuti ndipeze ufulu pamaso panu; ndipo penyani kuti mtundu uwu ndi anthu anu. (Eksodo 33:13)**

Davite naye anapemphera:

**Mundidziwitse njira zanu, Yehova; Mundiphunzitse mayendedwe anu. (Masalmo 25:4)**

Pemphani nzeru kuti mupange ziganizo zoyenera:

**Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye, Koma apemphe ndi cikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo. Pakuti asayese munthu uyu kuti adzalandira kanthu kwa Ambuye (Yakobo 1:5-7)**

Muyenera kupempha mapemphero kwa abale ena. Nthawi zambiri Mulungu amaonetsera chifuniro chake pogwiritsa ntchito mphatso zauzimu zopezeka mumikumano yamapemphero. Paulo ndi Banaba analandira chitsikimizo chamaitandiwe ao kuutumiki kudzera mumikumano waokhulupirira.

## **2. SANTHULANI MALEMBA:**

Santhulani Mau a Mulungu olembedwa kuti muone ngati pali mau amene akulankhula kunyengo yanu. Yang'anitsitsani ngati pali mfundo kapena chitsanzo cha munthu wina chimene chikugwirizana ndi nyengo imene mukukumana nayo.

Kusanthula malemba sikumatanthauza kuti kungotsegula Babulo lanu ndikuyamba kuwerenga tsamba limene mwapezalo. Kusanthula malemba ndi kuwerenga mozama mau a Mulungu ndikugwiritsa ntchito mfundo zake popanga ziganizo. Chitseko chotsekuka komanso mwayi ulionse umene mukuona ngati ukuchokera kwa Mulungu uyenera kuyesedwa ndi Mau a Mulungu. Yesu Khristu anagwiritsa ntchito mfundo yomweyi pamene anayesedwa ndi Satana kuti achite mosemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Iye anayankha

“kwalembedwa.” Izi zikuonetsa kuti iye anaunikira zinthu molingana ndi Mau a Mulungu (Mateyu 4).

Pamene mukusanthula Baibulo, onenetsani kuti mwarenganso malonjezano ambiri kuti akakhale chitsogozo. Ena mwa malonjezano amenewa aperekedwa mu ndime ya zophunzira zoonjezera. Kuwerenga ndime zimenezi zikuthandizani kukuza chikhulupiriro chanu kuti Mulungu amayankhula ndipo inu mukhoza kuzindikira mau ake.

### **3. MVETSERANI KULANKHULA KWA MZIMU WOYERA MKATI MWANU:**

Pempherani ndi kuwerenga Mau a Mulungu, Mulungu amalankhula chifuniro chake mkati mwanu kudzera mukulankhula kwa Mzimu Woyera mkati mwanu. Izi taziona kale mwatsatanetsane mu Chaputala ichi. Mulungu amagwiritsa ntchito chiyankhulo cha pemphero cha Mzimu Woyera pofuna kulankhula nanu. Ngati mulibe kutsikimizika pa chifuniro cha Mulungu, pempherani mu chinenero cha Mzimu Woyera.

Mzimu Woyera amadziwa chifuniro cha Mulungu changwiwo ndipo iye amathandizira inu kuti mupemphere molingana ndi chifuniro chimenechi.

**Ndipo iye amene asanthula m'mitima adziwa cimene acisamalira Mzimu, cifukwa apempherera oyera mtima monga mwa cifuno ca Mulungu. (Aroma 8:27)**

Kumbukirani kuti Yesu anafotokoza kuti Mzimu Woyera adzationetsa zinthu zonse zimene zikutanthaza kuti adzawulula chikonzero cha Mulungu kwa ife. Iye amatsogolera molingana ndi chifuniro cha Mulungu.

### **4. FUNANI UPHUNGU WACHIKHRISTU**

Ngati mmene tinakambira kale, Mulungu amagwiritsa ntchito aphungu achikhristu kuti akathandizire aphungu popanga ziganizo; Baibulo limafotokoza kuti:

**(Miyambi 12:15) Njira ya citsiru ndiyolungama pamaso pace pace; Koma wanzeru amamvera uphungu.**

Ndi zofunikwa kwambiri kuti mufune uphungu kwa akhristu okhwima osati kwa akwatswiri a maganizidwe amunthu achikunja. Mukafunsira uphungu kwa anthu awa adzakupatsani uphungu wachikunja ndi iwo ali ngati atsogoleri akhungu otsogolera anthu osapenya.

**WODALA munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipa, Kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa, Kapena wosakhala pansu pa bwalo la onyoza. (Masalmo 1:1)**

Simukuyeneranso kufunsira uphungu kwa akhristu oti angobadwa mwatsopano kumene. Iwo amakhala kuti alibe chidziwitso chambiri komanso nthawi zambiri amakhala sanakhwime muuzimu.

Athu ena amapita kwa aphungu ndi cholinga choti phunguyo agwirizane ndi maganizo awo. Ngati maonedwe anu azinthu ali amenewa, palibe chimene mungapindule. Akhristu ena amafuna uphungu ochokera kwa aphungu angapo nd cholinga choti afananitse uphungu umene alandirewo. Izi zimakhala ngati kuchita mavoti kuti aone amene akugwirizana ndi mfundo kapena maganizo ao. Ichi sicholinga cha uphungu chifukwa muyenera kuzindikira kuti uphungu onse uyenera kugwirizana ndi mau a Mulungu olembedwa.

**5. UNIKIRANI NYENGO ZANU**

Muyenera kuunikira nyengo zimene zikugwirizana ndi chiganizo chimene mukufuna kupangacho. Ndipo izi zikuyenera kuchitika mogwirizana ndi chitsogozo chimene chimadza mumpemphero, kuwerenga Mau a Mulungu, uphungu ndi kulankhula kwa Mzimu Woyera mkati mwanu.

Nyengo zathu pazokha sizikuyenera kugwiritsidwa ntchito pofunafuna chifuniro cha Mulungu. nthawi zina nyengo zathu zimapereka mwayi ochepa wamayankho athu pamene tikufunafuna chifuniro cha Mulungu.

**6. KUGWIRITSA NTCHITO ZIFUNGULO ZA BAIBULO KUTI MUPEZE CHITSOGOZO CHATSOPANO**

Kudziko lakuthupi, timagwiritsa ntchito zifunguro (makiyi) pofuna kutsegula zitseko. Chimodzimodzi kudziko lauzimu, Mulungu wapereka zifungulo zotsekulira zitseko zachifuniro chake. Zifungulo zimenezi zikupezeka mu Buku la Miyambo:

**Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, Osacirikizika pa luntha lako; Umlemekeze m'njira zako zonse, Ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako. (Miyambi 3:5-6)**

**Chifunguro Chayomba: Kukhulupirira.**

Simukuyenera kuopa chimene Mulungu akukupemphani kuti muchite. Muyenera kudziwa chikonzero chake kuti ndi chabwino. Ndithu munthu ayenera kukhulupirira amene anapereka

mwana wake yekhayo kuti akafere ife. Chikhulupiliro chanu chikuyenera kukhala mwa Mulungu osati munthu.

**Atero Yehova: Wotembereredwa munthu amene akhulupirira munthu, natama mkono wanyama, nucoka kwa Yehova mtima wace. (Yeremiya 17:5)**

### **Chifungulo Chachiwiri: Kusadalira Mzeru Zanu.**

Simukuyenera kudalira maganizo anu. Koma izi sizikutanthauza kuti kuganiza kulibe ntchito. Buku la Miyambo ladzala ndi zitsanzo za malamulo oti tigwiritse ntchito nzeru kapena kumvetsetsa kwathu ngati anthu. Nkhani yayikulu apa ndi yakuti sitingadalire nzeru zokha kapena kaganizidwe kathu pamene tikufuna chifuniro cha Mulungu.

Mfumu Davide sinapemphe chitsogozo cha Mulungu pamene imabwelera ndi likasa ku Yerusalemu. Iye anagwiritsa ntchito nzeru zake posuntha likasali. (1 Samueli 6:1-7)

Chifukwa chakuti ichi sichinali chikonzero cha Mulungu, chiweruzo chinangwera iye. Inde chinali chifuniro cha Mulungu kuti likasa libwelere ku Yerusalemu, koma chifuniro cha Davide chinali chosemphana ndi chifuniro cha Mulungu.

### **Chifungulo Chachitatu: Kuzindikira Mulungu Muzonse.**

Kuzindikira Mulungu muzonse ndi kupereka ulemu kwa Mulungu ndi maganizo, mau ndi zochita zathu zonse. Iye akuyenera kukhala oyamba mmoyo wanu:

**Amenenso anatifotokozerana cikondi canu mwa Mzimu. (Akolose 1:8)**

Yoswa analakwitsa kwambiri pamene sanafunse uphungu ochokera mkamwa mwa Mulungu. Iye anachita ubale ndi a Gidiyoni amene anali fuko losakhulupirira. Izi zinali zoletsedwa pamaso pa Mulungu.

Mfundo zitatu:

- Kukhulupirira Mulungu ndi mtima wako onse.
- Osakhulupirira kumvetsetsa kwanu kapena mzeru zanu.
- Kulemekeza kapena kuzindikira Iye muchilichonse.

## **7. SANKHANI NJIRA YA MZERU**

Pamene mukupanga ziganizo zimene ndizopezeka mu Baibulo, muyenera kupanga ziganizo zimenezi molingana ndi mau a Mulungu olembedwa. Ziganizo zina mukhoza kupanga pochita zinthu izi: kuwerenga mau a Mulungu, kupemphera, kufunsira uphungu, kuunguza nyengo zanu. Komanso mukhoza kugwiritsa ntchito nzeru zanu. Izi zili chomwechi chifukwa mulungu ndi amene amapereka mzeru.

Njira imene ikuoneka kuti ndi ya mzeru ndi imene muyenera kusankha chifukwa ndi imene imapereka mwayi waukulu oti mukhoza kukula muuzimu. Ndipo njira ya mzeru ndi imene ili yogwirizana ndi zimene Mulungu wavumbulutsa kudzera mu Baibulo, Pemphero, kulankhula kwa Mzimu Woyera ndi uphungu wachikhristu.

Kuthekera kozindikira njira ya mzeru kumakula pamene mukula muuzimu:

**Pakuti mungakhale mwayenera kukhala aphunzitsi cifukwa ca nyengoyi, muli nako kusowanso kuti wina aphunzitse inu zoyamba za ciyambidwe ca maneno a Mulungu; ndipo mukhala onga ofuna mkaka, osati cakudya cotafuna. Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda. (Ahebri 5:12-13)**

Kukula muuzimu kumabwera chifukwa cha Ubale ndi Mulungu, pemphero ndi kulingalira mau a Mulungu olembedwa (Baibulo).

**Ndipo mtendere wa Kristu ucite ufumu m'mitima yanu, kulingakonso munaitanidwa m'thupi limodzi; ndipo khalani akuyamika. (Akolose 3:15 )**

Oyimbira kapena owunikira masewera amaonetsetsa kuti masewerao akuseweredwa molinga ndi malamulo amasewerowo.

Mudziko lauzimu, mtendere wa Mulungu ndi umene umayendetsa chifuniro cha Mulungu. Zochita zathu komanso ziganizo zathu zimaunikiridwa ndipo ngati zili zogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu, izi zimabweretsa mtendere mkati mwanu. Ngati mukusowa mtendera, simukuyenera kuchita kena kalikonse. Muyenera kudikira mpaka mutapeza mtendere pachiganizo chimene mukufuna kupangacho. Kusowa mtendere ndi chizindikiro chochokera kwa oyimbira masewero kuti chinachake sichiri bwino:

**Pakuti Mulungu sali Mulungu wa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima. (1 Akorinto 14:33)**

**CHITHU CHIMODZI PAKAMODZI**

Mfundo yofunika kwambiri pa za chifuniro cha Mulungu ndi kuzindikira kuti Mulungu amaonetsera chikonzero chake pakamodzi. Izi zikutanthauza kuti samakuonetserani dongosolo lonse lamoyo wanu pakamodzi. Mulungu samangolankhula pakamodzi mmoyo wanu ayi. Izi zili chomwechi chifukwa ndi zosatheka kukhazikitsa ubale ndi muthu pongocheza naye kapena kulankhula naye kamodzi kokha. Ubale ndi chinthu chimene chimatenga nthawi yokambirana kapena kuchezerana mopitilira. Mulungu amakhala akulankhulabe ndipo ife timakhala tikukula mukuthekera kwathu kozindikira Mau ake.

Mulungu ali ndi chifukwa chovumbulutsira chifuniro chake pang'nopang'ono. Nthawi zambiri mumakhala kuti simunakonzekere kuti mudziwe dongosolo lonse lamoyo wanu. Izi zili chomwechi chifukwa zikhoza kubweretsa kumva kuperewera chifukwa cha ntchito imene ili patsogolo panu. Yesu anauza ophunzira ake nati:

**Ndiri nazo zambirinso zakunena kwa inu, koma simungathe kuzisenza tsopano lino.  
(Yohane 16:12)**

Simukuyenera kudandaula zamtsogolo. Chimene muyenera kuchita ndikupanga ziganizo zoyenera Molingana ndi nyengo imene mukudutsamo. Tsogolo ndi chinthu chimene chili mmanja mwa Mulungu. Koma izi sizikutanthauza kuti simukuyenera kukonzekera zamtsogolo ayi. Nkhani ndi yakuti simuyenera kudandaula zamtsogolo. Chimene chili chofunika ndikukhala moyo wanu molingana ndi chifuniro cha Mulungu cha nthawi imene muliyo. Muyenera kuphunzira kumva mau ake a moyo wanu wa tsiku ndi tsiku. Mapeto a izi ndi akuti moyo wanu onse mumayenda mu chifuniro cha Mulungu.

Mulungu samaonetsera chifuniro chake chonse kwa ife chifukwa akufuna kuti tikhale moyo wa chikhulupiriro. Zimakhala zophweka kuyamba ulendo ngati mukudziwa kumene mukathere. Koma sizophweka kuyamba ulendo wachikhulupiriro umene mathero ake ndi osadziwika.

Baibulo limaonetsera chikhulupiriro cha Abrahamu:

**Ndi cikhulupiriro Abrahamu, poitanidwa, anamvera kuturuka kunka ku malo  
amene adzalandira ngati colowa; ndipo anaturuka wosadziwa kumene akamukako.  
(Ahebri 11:8)**

Palibe chithu chimene chingakuze chikhulupiriro chanu kuposa kuchita chithu pakamodzi. Kuchita chithu pakamodzi pamene Mulungu akuonetsera chifuniro chake zimatanthauza kuti musachite zinthu mothamangira. Mose anachita zinthu mofulumira ndipo chifukwa chaichi, anapha munthu waku Igupto. Abrahamu anayenda nsanga kuposa chikonzero cha Mulungu pofuna kukhazikitsa Ishamaeli ngati mwana walonjezano.

Buku la Estere limatsindika kufunika kodikira pa Mulungu. Anthu a Mulungu anali pachiopsezo choonongedwa ndi chiwembu chokonzedwa ndi munthu oipa otchedwa Hamani. Iye anapempha amfumu kuti aononge Ayuda onse.

Mfumukazi Estere imadziwa zachikonzero ichi ndipo imazindikira kuti sichinali chikonzero cha Mulungu kuti anthu Achiyuda akaonongedwe, koma iye sanachite zinthu mothamanga. Iye anadikira kufikira nthawi imene Mulungu anamupatsa dongosolo loyenerera. Munthawi yakudikirira imeneyi, mfumu inazindikira kuti Modekayi amene anali Muyuda, anapulumutsa moyo kuchiwembu chimene chinakonzedwa kuti mfumu iphedwe.

Izi zitadziwika, Estere anaulula chiwembu cha Hamani chofuna kumpha Ayuda. Hamani analangidwa chifukwac cha chiwembu chake ndipo Ayuda onse anapulumutsidwa kuchiwembu chake. Zonsezi zinachitika chifuka chakuti Estere anadikira kwa masiku angapo asanachitepo kanthu.

### **CHITSAMBA CHIKUYAKABE**

Mulungu akutsogolerabe anthu ake ndipo amakhumba kulankhulabe ndi ife. Chifukwa cha ichi, muuzimu tikhoza kunena kuti chitsamba chija chikuyakabe.

**Undiitane Ine, ndipo Ine ndidzakuyankha iwe, ndipo ndidzakusonyeza iwe zazikuru, ndi zolakika, zimene suzidziwa. (Yeremiya 33:3)**

Mulungu akufuna kuvumbulutsa chifuniro chake komanso kuonetsera poyera chikonzero chake. Iye akupitilirabe kupereka chitsogozo. Iye ndi Mulungu amene amalakhula ngati inuyo mwakonzeka kumvetsera.

## MAFUNSO ODZIYESA NOKHA:

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

---

2. Kodi ndi chitsikimizo chiti chimene Mulungu amapereka kwa okhulupirira pamene akuyenda muchifuniro changwiro.

---

---

3. Tchulani zifungulo ziwiri zodziwira chifuniro cha Mulungu molingana ndi Miyambo 3:5-6.

---

4. Kodi kuzindikira Mulungu pa zonse ndi chiani?

---

---

5. Tchulani ndondomeko zisanu ndi ziwiri zopezera chifuniro cha Mulungu molingana ndi chaputala ichi.

---

---

---

---

6. Werengani ziganizo izi ndipo ngati chiganizo chili cholondora lembani T kutsogolo kwachiganizocho. Ngati chiganizo chili chosalondora, lembani F kutsogolo kwa chiganizocho.

a. \_\_\_\_ Njira yabwino yogwiritsa ntchito Baibulo pofuna kupeza chifuniro cha Mulungu ndi kutsegula Baibulo ndipo tsamba limene lakusangatsaniro ndiye chifuniro cha Mulungu.

b. \_\_\_\_ Mulungu nthawi zambiri amavumbulutsa dongosolo lonse la moyo wathu mwatsatanetsatane kudzera mu vumbulutso limodzi lozizwa.

c. \_\_\_\_ Mulungu anasiya kulankhula lero lino kudzera mumaloto, masomphenya ndi njira ya zozizwa.

(Mayankho amafunsowa ali kumapeto kwa bukuli)



## **ZOONJEZERA POPHUNZIRA**

1. Fananizani Miyambo 3:5-6 ndi Aroma 12:1-2. Mundime zimenezi pali zinthu zabwino ziwiri zoyenera kuzitsata ndi zinthu ziwiri zimene sitikuyenera kutsata. Tchulani mfundo zimene zili mundandanda uli munsu.

Miyambo 3:5-6

Aroma 12:1-2

Zoyenera kutsata:

Zosayenera kutsata:

Zoyenera kutsata:

2. M’busa Goerge anali mtsogoleri wauzimu wamphamvu amene anayambitsa ndikutsogolera nyumba zosungira ana amasiye ku England. Muzolemba zake, iye anafotokozera chinsisi chake chimene amagwiritsa ntchito pofuna kuzindikira chifuniro cha Mulungu”

“Choyamba ndimaonetsetsa kuti mtima wanga ulibe chifuniro chinachilichonse pa nkhani iliyonse”

Zovuta zambiri zimene timakumana nazo zimagonjetsedwa ngati pamene mtima wathu uli okonzekeza kuchita chifuniro cha Mulungu pa china chilichonse. Nkhani yaikulu ndi kuzindikira chifuniro cha Mulungu.

Ndikafika pamenepa, sindalola kuti mmene ndikumvera kapena ndikuonera zinthu kuti kundionetsere zotsatira zachiganizo changa. Chifukwa ngati ndingatere, kukhala kudziyenga ndekha chabe.

Ndimafunafuna chifuniro cha Mzimu wa Mulungu kudzera mu Mau a Mulungu. Mau ndi Mzimu wa Mulungu ziyenera kugwirizana kapena kulumikizana. Ngati ndingayang’anire pa Mzimu yekha opanda Mau a Mulungu, ndimakhala kuti ndapereka mwayi odziyenga dekha. Ngati Mzimu Woyera atitsogolera, timafunafuna chifuniro cha Mulungu molingana ndi Malemba ake.

Kenako, ndimaganzira nyengo zimene ndikudutsamo. Izi nthawi zambiri zimaonetsera chifuniro cha Mulungu mogwirizana ndi Mau ndi Mzimu. Kudzera mu mupemphero, ndimapempha Mulungu kuti andionetsere chifuniro chake. Ndipo kudzera muzinthu izi, Pemphero, kusanthula mau a Mulungu ndi kulingalira mozama, ndimapanga chiganizo chimene ndikuona kuti ndichabwino molingana ndi kuthekera kwanga komanso

chidziwitso changa. Koma ngati mtima wanga uli ndi mtendera ndipo izi zikapitilirabe kuchitika, ndimachitapo kathu moyenera.

Kaya ndi muzinthu zing'onozing'ono ndi zochitika zikuluzikulu, njira imeneyi yakhala yothandiza nthawi zonse.

3. Mulungu anapereka malonjezano ake kudzera mumalemba okudza chitsogozo.  
Werengani

Salimo: 3:8; 5:8; 25:5,9:12; 27:11; 31:3; 32:8; 37:23; 48:14; 61:2; 73:24; 78:52,72; 85:8, 13; 107:7; 139:10,24; 142:3; 143:10

Miyambo: 3:6; 4:11; 8:20; 11:3,15; 16:9; 21:29; 23:19

Mlaliki 10:10

Yesaya: 45:13; 58:11; 61:8

Yohane 10:3; 16:13

Aefeso: 5:17

Akolose 1:9; 4:12

4. Chimodzi mwachitsanzo chopambana cha chitsogozo ndi chitsogozo cha Mulungu pa ana a Israeli kuchoka ku Igupto kupita kudziko lamalonjezano. Mukhoza kuwerenga ndime zili munsimu.

Eksodo 13:17, 18, 21: 15:13

Deteromome 8:2, 15; 29:5; 32:10;

I Mbiri 11:2

II Mbiri 25:11

II Samueli 5:2

Nehemiya 9:12

Salimo 77:20; 78:14, 53; 80:1; 106:9; 107:7; 136:16

Yesaya 48:21; 63:12-14

Yeremiaha 2:6, 17

Ahebri 8:9

5. Ichi ndi chitsanzo chophwekerapo chimene mukhoza kutsata popanga chiganizo

- Kutsutsana: onetsetsani kuti chiganizo chisapangidwe motsutsana ndi mau a Mulungu.
- Kudziletsa: Simukuyenera kupanga chiganizo muli ndi mkhwiyo, mantha, kukhumudwa ndi zina zambiri.
- Uphungu: funani uphungu wachikhristu pachiganizo chanucho.
- Nyengo: unikirani nyengo zabwino ndi zoipa zogwirizana ndi chiganizo chimene mukufuna kupangacho. Mulungu nthawi zina amagwiritsa ntchito nyengo zathu pofuna kutsogolera moyo wathu.
- Chapamtima: unikirani chinthu chimene chili pamtima panu. Nthawi zina Mulungu amapereka chithu chapamtima ndi cholinga chakuti atsogorere ife kuchifuniro chake. Ndipo ngati chili chochokera kwa Mulungu, chimakhala chogwirizana ndi mau a Mulungu nthawi zonse.
- Chikumbu mtima: chikumbumtima chathu chimene chili chenjezo lochokera kwa Mulungu chimakudziwitsani ngati mwatenga njira yolondola.
- Kukhutitsidwa: onetsetsani kuti muli ndi mtendere wa Mzimu Woyera umene umabwera pamene mwapanga chiganizo choyenera.

## **CHAPUTALA 8**

### **MTCHITIDWE OKAIKITSA**

#### **ZOLINGA:**

Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la ntchitidwe okaikitsa.
- Perekani ndondomeko zakapangidwe kaziganizo zokhudza mtchitidwe okaikitsa.
- Kusiyanitsa pakati pa “m’bale ofooka ndi “m’bale olimba”
- Perekani ndondomeko za Baibulo zothandizira m’bale ofooka.
- Kupereka ndondomeko zothanirana ndi kusagwirizana pakati pa anthu okhulupirira.
- Kupereka ndondomeko zothana ndikusamvana pakati pa abale awiri.

#### **VESI YOTSOGOLERA.**

**Cifukwa cace mungakhale mudyu, mungakhale mumwa, mungakhale mucita  
kanthu kena, citani zonse ku ulemerero wa Mulungu. (1 Akorinto 10:31 )**

Chaputala ichi chifotokozerera kapangidwe kaziganizo pa mtchitidwe okaikitsa. Tanthauzo la mau amenewa lifotokozeredwa, komanso ndondomeko zothanirana ndi mchitidwe okaikitsa zikambidwanso. Kuonjezera apo, tikambaso za mmene tingachitire ndi m’bale ofooka, kuthana ndi kusamvana pakati pa okhulupirira ndi kuweruza zolakwirana pakati abale okhulupirira.

### **MTCHITIDWE OKAIKITSA**

Chikhalidwe china chilichonse chimakhala mtchitidwe okaikitsa. Uwu ndi mtchitidwe umene sumatchulidwa ndi Baibulo ngati uli olakwika kapena oyenera pakati pa anthu otsata Yesu. Khristu.

Mukhoza kuganizira zitsanzo zamtchitidwe okaikitsa muchikhalidwe chanu. Mwachitsanzo, izi zikhoza kukhala zinthu zachikondwerero. Zikhoza kukhalanso mabungwe amene munthu akhoza kukhala modzi mwa membala. Mtchitidwe umeneu ukhozanso kukhala zizolowezi ndi ziganizo zimene timapanga zokhudza chakudya choti tidye kapena chakumwa chimene. Pakhoza kukhalanso mafunso okhudza masiko opembedza.

Ndiye tingadziwe bwanji chifuniro cha Mulungu pa mtchitidwe okaikitsa umene chitsogozo chake sichinalembedwe mu Baibulo. Muyenera kudzifunsa mafunsa awa:

## **KODI ZIMALEMEKEZA MULUNGU?**

Baibulo limafotokoza kuti zonse timachita ziyenera kulemekeza Mulungu:

**Cifukwa cace mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale mucita kanthu kena, citani zonse ku ulemerero wa Mulungu. (1 Akorinto 10:31)**

**ciri conse mukacicita, gwirani nchito mocokera mumtima, monga kwa Ambuye, osati kwa anthu ai; podziwa kuti mudzalandira kwa Ambuye mphotho ya colowa; mutumikira Ambuye Kristu mwaukapolo. (Akolose 3:23-24)**

## **KODI CHOLINGA CHANU NDI CHANI?**

Kodi ndi chifukwa chiani mukufuna kuchita zimene mukufuna kuchitazo? Izi zili chomwechi chifukwa ngakhale chinthu chabwino chikhoza kuchitika pazifukwa zosayenera. Mwachitsanzo, Yokobo akupereka cholinga cholakwika chapemphero.

**Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukacimwaze pocita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)**

Kupemphera sikolakwika koma cholinga cha pemphero chikhoza kukhala cholakwika. Cholinga chomwe chaperekedwa mu vesi iyi ndi chofuna kukwaniritsa zilakolako zonyasa.

## **KODI NDI CHOFUNIKA?**

Paulo akufotokoza kuti ngakhale zinthu zina zili zololedwa (zosasemphana ndi Mau a Mulungu), muyenera kuganizirabe ngati zili zofunika kuchita. Iye akufotokoza:

**Zinthu zonse ziloledwa kwa ine; koma si zonse zipindula, Zinthu zonse ziloledwa kwa ine, koma sindidzalamulidwa naco cimodzi. (1 Akorinto 6:12)**

## **KODI ZIBWERETSA KUKULA MUUZIMU:**

Zochitika zambiri zikhoza kukhala chotchinga kuti tikule mumzimu. Zinthu zina zokhoza kutitengera nthawi yathu yambiri kotere kuti izi zikhoza kulepheleretsa ife kuti tikule mumzimu.

**Ndipo ena ndiwo akufesedwa kuminga; iwo ndiwo amene adamva mau, ndipo malabadiro a dziko lapansi, ndi cinyengo ca cuma, ndi kulakalaka kwa zinthu zina, zilowamo, zitsamwitsa mau, ndipo akhala opanda cipatso. (Marko 4:18-19)**

**Ndipo zija zinagwa ku mingazi, ndiwo amene adamva, ndipo m'kupita kwao atsamwitsidwa ndi nkhawa, ndi cuma, ndi zokondweretsa za moyo, ndipo sakhwimitsa zipatso zamphumphu. (Luka 8:14)**

Muyenera kudzifunsa funso ili “kodi mtchitidwe uwu undithandiza kuti ndikule mumzimu kapena ayi?”

Mtchitidwe olepheleretsa kuti tikule munzimu uli ngati kunyamula zolemera zolemphelelersa kuthamanga paliwiro limene Mulungu waikiza kuti tithamange.

**Cifukwa cace ifenso, popeza tizingidwa nao mtambo waukuru wotere wa mboni, titaye colemetsa ciri conse, ndi cimoli Iimangotizinga, ndipo tithamange mwacipiriro makaniwo adatiikira, ndi kupenyenera woyambira ndi womariza wa cikhulupiriro cathu, (Ahebri 12:1)**

### **KODI NDI CHIZOLOWEZI CHOTIPANGA IFE KUKHALA KAPOLO:**

Mtchitidwe wina uli onse umene umatipanga ife kukhala kapolo, kaya ndi kuthupi, muuzimu, maganizo komanso umene umafuna nthawi yathu yambiri uyenera kupewedwa.

### **KODI NDI KULEKELERA?**

Mtumwi Paulo akufunsa fuso pa II Akorinto 6:24 “kodi pali ubale wanji pakati pa mdima ndi kuwala?”

Kodi mtchitidwe okaikitsa umene mukufuna kuchitao ndi osemphana ndi mau a Mulungu? Kodi mukhala mukuchita molingana ndi chifaniziro cha dziko lapansi? Baibulo limafotokoza kuti:

**Cifukwa cace, Turukani pakati Pao, ndipo patukani, ati Ambuye, Ndipo musakhudza kanthu kosakonzeka; Ndipo Ine ndidzalandira inu, (2 Akorinto 6:17)**

### **KODI ZIBWERETSA MAYESERO:**

Yesu anatiphunzitsa kupemphera kuti tingalowe mkuyesedwa. Ndi zopanda pake kupemphera pemphero limene loti tisayesedwe koma mapeto ake ndikudziika dala malo oti tikhoza kuyesedwa. Baibulo likuchenjeza:

**Munthu poyesedwa, asanena, Ndiyisedwa ndi Mulungu; pakuti Mulungu sakhoza kuyesedwa ndi zoipa, ndipo iye mwini sayesa munthu: koma munthu ali yense ayisedwa pamene cilakolako cace ca iye mwini cimkokera, nicimnyenga. Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa. (Yakobo 1:13-15)**

Kuyesedwa ndi kosiyana ndi chiyeso cha chikhulupiriro chathu. Chiyeso chachikhulupiriro chathu chimachitika pamane okhulupirira akumana ndi nyengo zovuta osati chifukwa choti walakwitsa. Nyengo zimenezi zimayesa chikhulupiriro chathu mwa Mulungu. Koma Mulungu amalola izi zichitike ndi cholinga cholimbisa chikhulupiriro chathu ndi kuti tikakule moyo wathu wauzimu.

Koma Mulungu sayesa munthu chifukwa mayesero ndi chikhumbitso chopanga choipa. Mayesero amabwera ngati simuyang'anira maganizo ndi zochita zanu bwino lomwe kapena ndi pamene Satana wakukopani kuti muchite choipa. Mchitidwe wina okaikitsa umatha kukuikani inu mumayesero. Ndipo ngati inu mugonjera kuchiyesocho, chilakolako chimabala tchimo. Mapeto a tchimo ndi imfa ya moyo wathu wauzimu.

### **KODI PALI MAONEKEDWE A CHOIPA**

Kodi mtchitidwe umene mukufuna kuchitao uli ndi maonekedwe a choipa kwa anthu ena? Baibulo limafotokoza kuti:

**Mupewe maonekedwe onse a coipa. (1 Atesalonika 5:22)**

### **KODI NDI CHOTSUTSANA NDI CHIKUMBUMTIMA CHANU:**

Pamene mukupanga chiganizo chokhudza mtchitidwe okaikitsa, muyenera kukhala kuti mwatsikimizika mkati mwanu kuti chiganizo mukufuna kupangacho ndi cholondora. Mu nthawi ya Chingano Chatsopano panali kusamvana pakati pa okhulupirira ngati kunali koyenera kudya nyama yoperekedwa ku msembe. Nsembe zimenezi zimaperekedwa mu nthawi ya Chipangano chakale ngati chotetezera tchimo. Nthawi imeneyi inali Yesu asanabwere kudzapereka moyo wake ngati nsembe yomaliza. Paulo anayankha motere funso limeneri:

**Koma iye amene akayika-kayika pakudya, atsutsika, cifukwa akudya wopanda cikhulupiriro; ndipo cinthu ciri conse cosaturuka m'cikhulupiriro, ndico ucimo. (Aroma 14:23)**

Nkhani ndi yakuti muyenera kutsikimizika mkati mwanu kuti chimene mukupangacho ndi choyenera. Ngati muli ndi kukaika, chimene mukupangacho chimakhala tchimo.

### **KODI ZIMAKHUDZA BWANJI ANTHU ENA:**

Ndondomeko yomaliza pa mtchitidwe okaikitsa ndi kufunsa ngati mtchitidwewo ukhudze anthu ena. Kodi zithandiza anthu ena? Kapena kuti kumangilira moyo wauzimu wa anthu ena. Baibulo limafotokoza kuti:

**(Aroma 14:19) Cifukwa cace tilondole zinthu za mtendere, ndi zinthu zakulimbikitsana wina ndi mnzace.**

Tiyenera kufunsa: kodi mtchitidwe umeneu uthandiza kuti anthu ena akakule moyo wauzimu. Paulo akufotokoza:

**Zinthu zonse ziloleka; koma sizipindula zonse. Zinthu zonse ziloleka; koma sizimanga zonse. (1 Akorinto 10:23)**

Mtchitidwe wina umene timachita ukhoza kubwenza mbuyo okhulupirira ena moyo wao wauzimu. Mwachitsanzo, Paulo pankhani yakudya nyana anafotokoza:

**Cifukwa cace, ngati cakudya cikhumudwitsa mbale wanga, sindidzadya nyama ku nthawi yonse, kuti ndingakhumudwitse mbale wanga. (1 Akorinto 8:13)**

Malingana ndi Paulo, kudya nyama sitchimo ayi. Koma iye sangadye ngati ichi chikhale chotchinga kwa m'bale ofooka mwa Ambuye. M'bale ofooka ndi okhulupirira amene chifukwa cha chikhulupiriro, chidziwitso komanso chikumbumtima chochepa, atha kukhudzidwa ndi m'bale olimba chikhulupiriro. Iye akhoza kupangitsidwa kuti achimwe motsutsana ndi chikumbumtima chake. Chifukwa cha ichi, kakulidwe ka moyo wake wauzimu kakhoza kusokonekera.

M'bale olimba chikhulupiriro ndi amene kumvetsetsa kwake kwa ufulu magawo ena komanso mphamvu yake ya chikumbumtima imamuthandiza kugwiritsa ntchito ufulu wake ndi chikumbumtima chabwino. Iye samasunthika ndi maganizo osiyanasiyana a anthu ena.

Mtchitidwe wina ulionse wa m'bale olimba mchikhulupiriro umene ndi oloedwa umakhala olakwika ngati ungapangitse kuti m'bale ofooka kuti achimwire chikumbumtima chake kapema kumulepheretsa kukula moyo wake wauzimu. Paulo analemba:

**Kuli kwabwino kusadya nyama, kapena kusamwa vinyo, kapena kusacita cinthu ciri conse cakukhumudwitsa mbale wako. (Aroma 14:21)**

## **KUFOTOKOZA MWACHIDULE KUPANGA CHIGANIZO PA MCHITIDWE OKAIKITSA**

Chithunzi chili pansichi chikufotokozera mwachidule ndodndomeko zakapangidwe kachiganizo pa mtchitidwe okaikitsa



<b>Kudzifunsa nokha. . .</b>	<b>Umboni wa m’Baibulo</b>
Kodi ziperekeka ulemelero kwa Mulungu?	I Akorinto 10:31; Akolose 3:17,23
Kodi cholinga chake ndi chiani?	Yakobo 4:3
Kodi ndi zofunika?	I Akorinto 6:12
Kodi zibweretsa kukula munzimu?	Marko 4:18,19; Luke 8:14; Ahebri 12:1
Kodi zibweretsa chizolowezi chaukapolo?	I Akorinto 6:12
Kodi ndi kulekelera?	II Akorinto 6:17
Kodi zibweretsa mayesero?	Yakobo 1:13-15
Kodi pali maonekedwe a choipa?	I Atesalonika 5:22
Kodi ndi zosemphana ndi chikumbumtina changa?	Aroma 14:23
Kodi zikhudza anthu ena?	Aroma 14:19,21; I Akorinto 8:13; 10:23

## **PAMENE OKHULUPIRIRA ASEMPHANA**

Werengani Aroma 14:1 ndi 15:2. Ma vesi amenewa akuonetsa kuti nthawi zina pamakhala kusiyana maganizo pakati pa opkhulupirira. Kusemphana maganizo kumeneku kumabwera chifukwa cha mtchitidwe okaikitsa umene sunakambidwe kuti ndi olondora kapena olakwika molingana ndi Baibulo.

Ndime zimenezi zikufotokoza kuti kusiyana maganizo kumeneku sikungabweretse choipa ngati tipitilira kukondana wina ndi mzake komanso kusanthulabe malemba. Aroma 14 akupereka ndondomeko zothanirana ndi kusemphana maganizo pakati pa okhulupirira mu zinthu zimene sizinakambidwe mu Baibulo.

## **KUSIYANITSA MCHITIDWE WA CHILAMULO NDI UFULU:**

Pa Aroma 14:14, amafotokoza kuti ndi kofunika kusiyanitsa pakati pa mtchitidwe wa ufulu ndi wachilamulo pamene okhulupirira asemphana. Pa nkhani zimene sizinalembedwe mu mau a Mulungu, Paulo akufotokoza:

**Ndidziwa, ndipo ndakhazikika mtima mwa Ambuye Yesu, kuti palibe cinthu conyansa pa cokha; koma kwa ameneyo aciyesa conyansa, kwa iye cikhala conyansa. (Aroma 14:14)**

## **KUKHAZIKITSA CHIKUMBUMTIMA CHANU:**

Muyenera kukhazikitsa chikumbumtima chanu mu mtchitidwe okaikitsa. Mwachitsanzo, pa nkhani ya masiku oyeretsedwa Paulo akufotokoza:

**Munthu wina aganizira kuti tsiku lina liposa linzace; wina aganizira kuti masiku onse alingana. Munthu ali yense akhazikike konse mumtima mwace. (Aroma 14:5)**

Gwiritsani ndondomeko zimene zaperekedwa kale muchaputala chimenechi kuti mukhazikitse chikumbumtima chanu pa mtchitidwe okaikitsa.

## **PEREKANI UFULU KWA ANTHU ENA KUTI AKHAZIKITSE CHIKUMBUMTIMA CHAO:**

Ngakhale kuti anthu ena ali ndi maganizo osiyana ndi anu, muyenera kulemekeza ufulu wao kuti akhazikitse chikumbumtima chao pa mtchitidwe okaikitsa.

**Koma iwe uweruziranji mbale wako? kapena iwenso upeputsiranji mbale wako? pakuti ife tonse tidzaimirira ku mpando wakuweruza wa Mulungu. (Aroma 14:10)**

**Cifukwa cace risaweruzanenso wina mnzace; koma weruzani ici makamaka, kuti munthu asaike cokhumudwitsa pa njira ya mbale wace, kapena compunthwitsa. (Aroma 14:13)**

## **UFULU WANU UKHALE NDI MALIRE CHIFUKWA CHACHIKONDI:**

Mfundo yaikulu pa Aroma 14:13-15:2 ndi yakuti ufulu wathu pachikhristu uli ndi malire chifukwa chachikondi.

**Yense wa ife akondweretse mnzace, kumcitira zabwino, zakumlimbikitsa. (Aroma 15:2)**

Tiyenera kukhala okhudzika ndi okhulupirira ena pokhala ndi malire azimene tikhoza kuchita. Izi tiyenera kuchita chifukwa chachikondi. Mfundo yaikulu ndi yakuti chifukwa chachikondi, sitienera kuchita kalikonse kamene kakhoza kuti abwelere mbuyo moyo wao wauzimu.

**Cifukwa cace risaweruzanenso wina mnzace; koma weruzani ici makamaka, kuti munthu asaike cokhumudwitsa pa njira ya mbale wace, kapena compunthwitsa. (Aroma 14:13)**

## **KUKONZA ZOLAKWIRANA:**

Ngati okhulupirira walakwira m'bale wina, Mateyu 18:15-17 akupereka ndondomeko zokonzakusemphana pakati pa abale awiriwa:

**Ndipo ngati mbale wako akucimwira iwe, pita, numlangize pa nokha iwe ndi iye; ngati akumvera iwe, wambweza mbale wako. Koma ngati samvera, onjeza kutenga ndi iwe wina mmodzi kapena awiri, kuti atsimikizidwe mau onse pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu. Ndipo ngati iye samvera iwo, uuze Mpingo; ndipo ngati iye samveranso Mpingowo, akhale kwa iwe monga wakunja ndi wamsonkho. (Mateyu 18:15-17)**

Ndondomeko zoyenera kutsatidwa pamene m'bale wakulakwira ndi izi:

1. Pitani pa awiri kuti mukonze kusemphana kwanu: simukuyenera kukamba zimene wakulakwirani kwa anthu ena. Muyenera kukumana ndi amene wakulakwiraniyo. Pepherani ndi kusanthula malemba limodzi amene wakulakwiraniyo.
2. Ngati iye samvera inu, tengani mboni ziwiri kuti zikambe naye. Muyenera kusankha okhulupirira osakondera. Atsogoleri a Mumpingo chikhoza kukhala chisankho chabwino. Inu ndi mboni zimenezi pamodzi ndi m'bale wakulakwiraniyo muyenera kuwerenga malemba limodzi komanso kupemphera.
3. Ngati m'baleyu safuna kuyanjanitsidwa, nkhani iyenera kutengeredwa kumpingo onse. Koma zikuyenera kuchitika nthawi yabwino osati nthawi imene anthu akupembedza. Ngati m'bale safuna kuyanjanitsidwa pamaso pampingo onse, iye ayenera kutengedwa ngati wachikunja.

#### **KUFOTOKOZERA MWACHIDULE PAMENE OKHULUPIRA ASEMPHANA:**

Chithunzi chili pansichi chikufotokozera ndondomeko zimene ziyenera kutsatidwa pamene okhulupirira asemphana pa mtchitidwe okaikitsa.

**Pameme okhulupirira asemphana**

Aroma 14-15:2 and Mateyu 18:15-17

Kusiyanitsa pakati pa chilamulo ndi Ufulu.

Kukhazikitsa chikumbumtima chanu

Perekani ufulu kwa ena kuti akhazikitse chikumbumtima chao

Ufulu wanu uyenera kukhala ndi malire chifukwa chachikondi.

Muyera kukonza zonse zolakwirana

## MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera:

---

---

2. Kodi mau oti mtchitidwe okaikitsa amanthauza chiani?

---

---

3. Tchulani ndondomeko khumi zimene mutha kugwiritsa ntchito pa mtchitidwe okaikitsa.

---

---

---

---

4. Kodi mau oti “M’bale ofooka amanthauza chiani?

---

---

5. Kodi mau oti “m’bale olimba mchikhulupiriro amanthauza chiani?

---

---

6. Tchulani ndondomeko zisanu zothana ndi kusamvana pakati pa abale awiri okhulupilira.

---

---

7. Kodi ndi njira ziti zitatu zimene munthu ayenera kuchita pamene walakwiridwa ndi m’bale wina okhulupirira.

---

---

---

(Mayanko amafunso awa ali kumapeto kwa Buku ili)

## **ZOONJEZERA POPHUNZIRA**

Mwapemphero unikirani moyo wanu ndipo tchulani mndandanda wa mtchitidwe okaikitsa umene mumachita pakadali pano kapena mukulingalira mutachita.

Unikilani mtchitidwe wina ulionse paokhapaokha pogwiritsa ntchito mfundo zimeme zaperekedwa m'musizi:

<b>Kudzifunsa nokha. . .</b>	<b>Umboni wa m'Baibulo</b>
Kodi ziperekeka ulemelero kwa Mulungu?	I Akorinto 10:31; Akolose 3:17,23
Kodi cholinga chake ndi chiani?	Yakobo 4:3
Kodi ndi zofunika?	I Akorinto 6:12
Kodi zibweretsa kukula munzimu?	Marko 4:18,19; Luka 8:14; Ahebri 12:1
Kodi zibweretsa chizolowezi chaukapolo?	I Akorinto 6:12
Kodi ndi kulekerera?	II Akorinto 6:17
Kodi zibweretsa mayesero?	Yakobo 1:13-15
Kodi pali maonekedwe a choipa?	I Atesalonika 5:22
Kodi ndi zosemphana ndi chikumbumtima changa?	Aroma 14:23
Kodi zikhudza anthu ena?	Aroma 14:19,21; I Akorinto 8:13; 10:23

## CHAPUTALA 9

### CHIFANIZIRO CHA BAIBULO CHAKAPANGIDWE KA CHIGANIZO

#### ZOLINGA:

#### Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza cholinga cha chifaniziro.
- Kufotokoza kufunika kwa chifaniziro popanga chiganizo.
- Kugwiritsa ntchito chifaniziro cha Baibulo kuti mupange ziganizo zoyenera.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Mtima wa munthu ulingalira njira yace; Koma Yehova ayendetsa mapazi ace.  
(Miyambi 16:9)**

#### MAU OYAMBA

Chaputala ichi chifotokozera chifaniziro cha Baibulo chakapangidwe ka chiganizo. Chifaniziro ndi chitsanzo cha chinthu ndipo cholinga chake ndi kupereka chitsanzo choti chitsatidwe. Chiganizo ndi chisankho chimene munthu amapanga. Muyenera kupeza yankho panyengo zanu zamoyo ndi kusankha zimene muchite. Ndongomeko yonseyi imatchedwa kupanga chiganizo. Chifaniziro chakapangidwe ka chiganizo chimapereka chitsanzo choti ife tikhoza kutsata pamene tikupanga ziganizo. Moyo wathu wakhazikika pakupanga ziganizo ndipo kupanga chiganizo ndi udindo. Kukana kupanga chiganizo ndi chiganizo chimene.

Chifaniziro cha Baibulo muchaputala chimenechi chikuthandizani kuti mupange ziganizo za mzeru zogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu.

**Mtima wa munthu ulingalira njira yace; Koma Yehova ayendetsa mapazi ace.  
(Miyambi 16:9)**


#### CHIFANIZIRO

Unikirani chifaniziro cha kapangidwe kachiganizo mu chithunzi chili minsichi. Chithinzichi chikungoonetsera zimene mwaphunzira kale mumachaputala ambuyomu.

### CHIFANIZIRO CHA BAIBULO CHAKAPANGIDWE KA CHIGANIZO

Muyera kupeza vuto, funso kapena nyengo imene ikufunika chitsogozo.

Kodi yankho la vuto lathu likupezeka mu Baibulo kapena pali mfundo yaikulu imene ikhoza kugwira ntchito?



Mndandanda 1

mndandanda 2

mndandanda 3

Kupanga chiganizo

kodi ndi mchitidwe okaikitsa?

Kodi ndi nyengo yeniyeni yamoyo

Molingana ndi mfundo

pangani chiganizo pogwiritsa ntchito

gwiritsani ntchito njira izi:

Kapena chitsanzo cha

mafunso ali munsiwa

pempherani

Baibulo

mumvetse chitsogozo

Chochokera kwa Mzimu Woyera

Funani uphungu wachikhristu

Unguzani nyengo zanu

Gwiritsani ntchito

Kodi ziperekeka ulemelero kwa Mulungu?

Zifungulo za Baibulo kuti

mupange chiganizo

Kodi cholinga chake ndi chiani?

Kodi ndi zofunika?

**Yang'anira ngati muli ndi  
mtendere mkati mwanu**

Kodi zibweretsa kukula mu uzimu?



Kodi zibweretsa chizolowezi chaukapolo?

Kodi ndi kulekelera?

Kodi zibweretsa mayesero?

Kodi pali maonekedwe a choipa?

Kodi ndi zosemphana ndi chikumbumtima changa?

Kodi zikhudza anthu ena?

**Yang'anirani ngati muli ndi mtendere mkati mwanu**

Ngati mulibe mtendere mkati mwanu, pitiliranibe kufunafuna ambuye pogwiritsa ntchito chifaniro ichi

## **KUGWIRITSA NTCHITO CHIFANIZIRO**

Molingana ndi chifaniziro chatu, njira yoyamba pamene tikupanga chiganizo ndi kupeza vuto, funso kapena nyengo imene ikufunika yankho. Chachiwiri ndi kusanthula malemba kuti tione ngati yankho la vuto lathu kapena nyengo yathu yaperekedwa mu Baibulo. (Mndandanda 1). Onetsetsani kuti chiganizo chanu ndi chogwirizana ndi Malemba.

## **INDE**

Ngati yankho lanu liri inde, ndiye kuti vuto lanulo yankho lake likupezeka mu Baibulo. Chimene mukuyenera kuchita ndi kupanga chiganizo molingana ndi mau a Mulungu (yang'anani mdandanda 2) Onetsetsani kuti chiganizo chanu ndi chogwirizana ndi Mau a Mulungu. **a**

## **AYI**

Ngati yankho lanu liri “ayi” gwiritsani ntchito mfundo za mndandanda 1 ndi 2.

Apa mupeza mayankho awiri a nyengo zimene sizinakambidwe mu Baibulo. Muyenera kuzindikira ngati chiganizo choti chipangidwe chikukhudza ntchitidwe okaikitsa kapena nyengo yeniyeni yamoyo.

## **MTCHITIDWE OKAIKITSA**

Mtchitidwe okaikitsa ndi chinthu chimene sichinakambidwe mumalemba. Izi zikhoza kukhala zoyenera kapena zosayenera. Chitsanzo cha izi chikhoza kukhala zinthu zachisangalalo, zizolowezi, dzakudya zimene tikhoza kudya kapena chakumwa chimene, mavalide ndi tsiku lopembedza.

Ngati chiganizo chimene mukufuna kupangacho ndi chokaikikitsa, muyenera kudzifunsa mafunso amene atchulidwa mu mndandanda. Mfundo za Baibulo zotsogolera popanga chiganizo pa mtchitidwe okaikitsa zafotokozeredwa kale mu chaputala 8. Muyenera kuyankha mafunso onsewa ndi kupemphera. Pomaliza, pangani chiganizo molingana ndi ndi mayankho amafunso opezeka pa chifaniziro.

## **NYENGO ZA MOYO WA TSIKUNDITSIKU:**

Nyengo za moyo zikhoza kukhala zinthu ngati, ziganizo zokhudza ukwati, utumiki, ntchito, malo oti tikhalepo ndi chisankho cha mpingo umene tikufuna kumaphepha. Izi ndi zisankho zimene zimakhudza moyo wathu kwambiri mukupita kwa nthawi.

Kuti mupange ziganizo zokudza moyo wa tsikunditsiku, yang'anani mndandana 3 kumanja kwa chifaniziro chakapangidwe kachiganizo. Choyamba muyenera kupempherera chiganizo chanucho. Pemphani Mulungu kuti akwaniritse chifuniro chake pa moyo wanu. Pemphani nzeru pamoyo wanu kuti mupange ziganizo zoyenera. Mtamandeni Mulungu chifukwa cha chitsogozo popanga chiganizo choyenera. Pemphani anthu ena kuti apemphere nanu. Werengani mau a Mulungu ndipo pamene mukuwerenga lengezani chitsogozo chochokera mu Mau a Mulungu.

Mvetserani kulankhula kwa mzimu Woyera pamene akukulankhulani za chifuniro cha Mulungu pamoyo wanu. Muyenera kuzindikira mavumbulutso a chozizwitsa ngati mungawalandire kuchokera kwa Mulungu. Mavumbulutso amenewa akhoza kukhala zinthu ngati: Masomphenya, maloto, angelo, mau omveka ochokera kwa Mulungu ndi chitsogozo chinachilichonse chogwirizana ndi Mau a Mulungu.

Muyenera kufuna uphungu wachikhristu. Unguzani nyengo zimene zazungulira chiganizo chanu. Gwiritsani ntchito zifungulo za Baibulo zimene mwaphunzira mu chaputala ichi. (Izi zikupezeka pa Miyambo 3:5-6). Molingana ndi mfundo zimenezi pangani chiganizo chogwirizana ndi mfundozi.

### **OYIMBIRA MASEWERA WA MTENDERE**

Popanga ziganizo zimene sizinakambidwe mu Baibulo, oyang'anira masewera wamtendere akhale chitsogozo chanu. Ngati mwapanga chiganizo chokhudza mtchitidwe okaikitsa ndipo mulibe mtendere mkati mwanu, pitiliranibe kufunafuna ambuye pogwiritsa ntchito njira za chifaniziro chimene chaperekedwa. Musapange chiganizo chomaliza pokhapokha ngati muli ndi mtendere mkati mwanu.

Simukuyera kuthamangira:

**Yembekeza Yehova: Limbika, ndipo Iye adzalimbitsa mtima wako; Inde, yembekeza Yehova. (Masalmo 27:14)**

**Moyo wanga, ukhalire cete Mulungu yekha; Pakuti ciyembekezo canga cifuma kwa Iye, (Masalmo 62:5)**

**Khala cete mwa Yehova, numlindirire Iye: Usabvutike mtima cifukwa ca iye wolemerera m'njira yace, Cifukwa ca munthu wakucita ciwembu. (Masalmo 37:7)**

**koma iwo amene alindira Yehova adzatenganso mphamvu; adzauluka pamwamba ndi mapiko monga ziombankhanga; adzathamanga kuma osalema; adzayenda koma osalefuka. (Yesaya 40:31)**

Chifukwa chakuthamangira, mfumu Saulo inlandidwa ufumu wake. Mukhoza kuwerenga nkhani imeneyi pa 1 Samuel 13. Nehemiya anadikira chitsogozo chochokera kwa Mulungu komanso nthawi yake yoikika. Mukhoza kuwerenga nkhani imeneyi mu Buku la Nehemiya.

## MAFUNSO ODZIYANKA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osanera.

---

---

2. Kodi cholinga cha chifaniziro ndi chiani?

---

---

---

3. Kodi chifaniziro chakapangidwe kachiganizo ndi chiani?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

## ZOWONJEZERA POPHUNZIRA

Gwiritsani ntchito chifaniziro cha Baibulo chimene chaperekedwa mu chaputala ichi kuti chikuthandizeni pa funso, nyengo ya moyo imene ikufunika kuti mupange chiganizo

## CHAPUTALA 10

### MWAYESA NDI KULEPHERA KODI?

#### ZOLINGA

Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kupeza zitsanzo za anthu mu Baibulo amene angonjetsa kulempha ndikubwelera kuchifuniro cha Mulungu changwiro.
- Kupeza zitsanzo za anthu mu Baibulo amene anasemphana ndi chifuniro cha Mulungu ndipo mathero awo anali olephera.
- Kutchula ndondomeko zobweleranso kuchifuniro cha Mulungu pamene mwalempera.

#### VESI YOTSOGOLERA:

**Ha! Akadandimvera anthu anga, Akadayenda m'njira zanga Israyeli! (Masalmo 81:13)**

#### MAU OYAMBA

Mu phunziro limeneri, mwaphunzira mmene Mulungu amalankhulira chifuniro chake kwa munthu. Koma chingachitike ndi chiani pamene mwalempera kuzindikira chifuniro cha Mulungu? Mwina mkutheka kuti mwadaladala simunamvere chifuniro chake. Mwina munasemphana ndi chitsogozo chake chifukwa chakulakwitsa kapena simunamvetse mfundo za Baibulo. Mkutheka kuti mwina mwachita zinthu mothamanga popanda chitsogozo cha Mulungu. Ndiye tipange bwanji pamene taya koma talephera.

#### ANTHU OLEPHERA AMENE ANACHITA BWINO

Baibulo liri ndi zitsanzo za atsogoleri amphamvu amene panthawi ina yamoyo wao analephera kuchita chifuniro cha Mulungu kapena kusemphana kumene ndi chifuniro cha Mulungu. komabe, posatengera izi anthu amenewa anachita bwino kwambiri.

Abrahamu: chifukwa cha mantha oti akhoza kuphedwa komanso mkazi wake kutengedwa, iye ananama kuti Sara simkazi wake. Koma iye anatchedwabwe bwenzi la Mulungu komanso munthu wachikhulupiriro.

**Mose:** Mmaloti alankhule ndi thanthwe malingana ndi mmene Mulungu anamuuzira, iye analimenya kuti madzi atuluke. Posatengera izi, Baibulo limafotokoza kuti palibenso mneneri wamphamvu ngati Mose.

**Davide:** Iye anachita chigololo ndi mkazi wamunthu wina ndipo kuonjezera apo, iye anapha mwamuna wamkaziyo pofuna kubisa ntchimo lake. Posatengera izi, iye anali mfumu wamphamvu ndipo anatchedwa wapamtima wa Mulungu.

**Yona:** Iye anapita malo osemphana ndi amene Mulungu anamuza kuti akalalike. Koma pakudutsa kwanthawi, iye analakira uthenga wamphamvu wachitsitsumutso mu mbiri. Chifukwa cha uthenga wake, mzinda onse wa Nenevi unalapa.

**Petro:** Iye anamukana Yesu Khristu, koma patadutsa nthawi anakhala mtsogoleri mwamphamvu wamphamvu.

### **ANTHU OLEMPHERA AMENE ANALEPHERA**

Baibulo liri ndi zitsanzo za anthu amene anasemphana ndi chifuniro cha Mulungu komanso mathero amoyo wao anali olephera komanso ogonjetsedwa.

**Samosoni:** iye anali oweruza ofunikira wa Isreali amene anapatsidwa mphamvu zambiri zakuthupi ndi Mulungu. Iye anayamba ndi kulanditsa ana a Israeli mmnja mwa adani ao Afilisiti. Koma chifukwa cha ubale wake ndi azimayi achikunja, iye anagwida ndipo anafa ngati wandende mmanja mwa adani a Israeli.

**Uziya:** Pachyambi mfumuyi inachita bwino pamaso pa Mulungu ndipo Mulungu anamupambanitsa iye. Koma iye anachimwa pamene analowa mukachisi ndikuchita zimene zimayenera kuchitidwa ndi ansembe okha. Chifukwa cha ichi, anagwidwa ndi khate ndipo anafa.

**Saulo:** Iye ngati mfumu yoyamba ya Israeli anakonedwa ndi anthu ake ndipo mzimu wa ambuye unakhala pa iye. Chifukwa chakusamvera, Saulo anakanidwa ngati mfumu ndipo mfumu ina inasankhidwa kuti ikamalizitse ntchito yake. Mathero a moyo wa Saulo anali olephera, ochititsa manyazi kenako angodzipha yekha.

**Eli:** Pachiyimbi, Iye anali wansembe wamphamvu mu nyumba ya Ambuye. Eli ndi ana ake anafa imfa yochitisa manyazi chifukwac chakusamvera.

**Yudasi:** Yudasi anali ophunzira wa Yesu Khristu munthawi ya utumiki wa Yesu pa dziko lapansi. Iye anaona zozizwa zimene Yesu anachita komanso anamva chiphunzitsa chake.

Posatengera izi, Yudasani anamupereka Yesu komanso nachotsa moyo wake omwe kapena kuti anadzipha.

### **KODI ZIKUSIYANA PATI**

Tatchula zitsanzo zingapo za Baibulo za anthu amene munyengo ina analempera kuzindikira chifuniro cha Mulungu. Koma ena mwa anthu amenewa, anakonzaso zinthu zao ndipo anakhala atumiki amphamvu a Mulungu. Koma ena sanakonzeso njira yao ndipo mathero awo anali olephera. Koma kodi zikusiyana pati pakati pamagulu awiriwa.

Kuti tiyankhe funso limeneli, tiyenera kuunikira moyo wa mafumu awiri a Israeli amene ndi mfumu Saulo ndi Davide. Poyamba werengani nkhani ya kuchoka pamaso pa Mulungu kwa Davide (II Samueli chaputala 11-12). Kenako werenganinso nkhani yakulephera kwa mfumu Saulo pa 1 Mafumu chaputala 15. Kulempera kwa mfumu Davide kumaonekera kwambiri kusiyana ndi kulempera kwa Saulo. Mulungu anauza Saulo kuti asakatenge chilichonse pamene akamenya nkondo, koma iye anatenga bulu ngati cholanda chakunkhondo.

Davide nachita chigololo ndi mkazi wamwini. Ndipo izi zitadziwika chifukwa chapakati, Iye anakonza chiwembu ndikupha mwamuna wamkaziyu. Saulo anakanidwa ngati mfumu ya Israeli, koma Davide anapitilirabe kukhala pampando waufumu kufikira kuti anatchedwa wapamtima wa Mulungu. Koma nanga ndi chifukwa chiyani ena moyo wao mathero ake anali kulephera pamene ena anapitilirabe kuchita bwino.

Mneneri Samueli anamfikira Saulo ndi kumuza kuti wachimwa, Saulo anati:

**Ndipo Sauli anati kwa Samueli, Ndinacimwa; pakuti ndinalumpha lamulo la Yehova, ndi mau anu omwe; cifukwa ndinaopa anthuwo, ndi kumvera mau ao. Pomwepo iye anati, Ndinacimwa, koma mundicitire ulemu tsopano pamaso pa akuru a anthu anga, ndi pamaso pa Israyeli, nimubwerere pamodzi ndi ine, kuti ndikalambire Yehova Mulungu wanu. (1 Samueli 15:24, 30)**

Saulo anagwidwa chifukwa chamachimo ake ndipo iye anawavomereza. Iye anaonetsa kuzindikira kulakwa kwake komanso anadzimvera chisoni. Koma iye anachita izi chifukwa chakuti anagwidwa. Kuonetsa kudzimvera chisoni kokha sikokwanira ayi koma chisoni chiyenera kubweretsa kulapa.

**Pakuti cisoni ca kwa Mulungu citembuzira mtima kuchipulumutso, cosamvetsanso cisoni; koma cisoni chadziko lapansi cicita imfa. (2 Akorinto 7:10)**

Saulo amavomeleza kuti anachimwa koma iye amakankhizira kuchimwa kwake pa anthu ena. Iye sanafune kuvomeleza udindo pazochita zake. Iye amafuna kuti apembedze Mulungu pamene Mulungu afuna kuti iye alape. Mfumu Saulo inali yokhudzika kwambiri ndi mmene anthu amamuonera osati mmene Mulungu amamuonera. Chifukwa cha ichi, Samueli anauza Saulo nati:

**Ndipo Samueli ananena naye, Yehova anang'amba ufumu wa Israyeli lero kuucotsa kwa inu, naupatsa kwa mnansi wanu wina wabwino woposa inu. (1 Samueli 15:28)**

Ufumu unalandidwa kwa Saulo ndikupatsidwa kwa Davide.

Pamene mneneri Natani anauza Davide kuti wachimwa, Iye anavomereza zatchimo lake:

**Ndipo Davide anati kwa Natani, Ndinacimwira Yehova. Natani nati kwa Davide, Ndiponso Yehova wacotsa chimo lanu, simudzafa. (Samueli 12:13)**

Iye sanafune kuloza zala anthu ena. Iye sanalozе chala Barthsheba koma anavomereza kulaka kwake ndikupempha chikhulukiro pamaso pa Mulungu.

**Cifukwa ndazindikira macimo anga; Ndipo coipa canga ciri pamaso panga cikhalire: Mundilengere mtima woyera, Mulungu; Mukonze mzimu wokhazikika m'kati mwanga. (Masalmo 51:3,10)**

Mfumu Davite ndi Saulo anapanga ziganizo zolakwika. Koma mfumu Davide itauzidwa kuti yalakwitsa, Iye analapa komanso ndikusintha kachitidwe kake. Izi ndi zosiyana ndi Saulo. Iye anasemphana ndi chifuniro cha Mulungu ndipo mathero amoyo wake anali olephera, ogonjetsedwa komanso anadzipha yekha.

## **MWAYESA NDIPO MWALEPHERA KODI?**

Pamene mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu, pali ndondomeko za Baibulo zimene zikhoza kukuthandizani kuti mubwerere kuchifuniro cha Mulungu. Pofuna kuonetsera ndondomeko zimenezi, tigwiritsa ntchito chitsanzo cha Yona. Musanapitirire ndi phunziro ili, werengani buku la Yona.

Yona anauzidwa ndi Ambuye kuti akalalikire mzinda ochimwa wa Nenevi. Mmalo moti amvere chifuniro cha Mulungu, iye anachita mosemphana ndi Mulungu. Yona anagwiritsa ntchito njira izi kuti abwerere kuchifuniro cha Mulungu ndipo izi ndi njira zimene muyenera kutenga pamene mwalemphera.



## **KUZINDIKIRA KULEPHERA KWANU:**

Zinatengera mafunde akulu panyanja kuti Yona azindikire kuti wasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. (Yona1:2) Muyenera kukhala ndi chitsikimikizo kuti Mulungu ali ndi njira zokudziwitsirani pamene mwasemphana ndi chifuniro chake.

Ngati simungazindikire kuti mwansemphana ndi chifuniro cha Mulungu, ndi zovuta kuti mubwerere ndikuchita chifuniro chake. Musalore chifukwa chili chonse kuti chikulepheretseni inu kuvomereza kulephera kwanu. Zina mwazifukwa zimene anthu amapereka ndi izi:

“Anthu ataya nane chikhulupiriro”

“Kuvomeleza kuti ndalephera kukhala mmalo mwa kuvomeleza kuti ndinalakwitsa”

“Ndinalephera kale. Kuli bwino ndingosiya”

“Ndachedwa kale”

“Ndine chitsanzo choipa, kulibwino ndingosiya”

“Ndasemphana kambiri ndi chifuniro cha Mulungu, ndizovuta kukonzaso zinthu”

“Sindikudziwa ngati ndingapezenso chifuniro cha Mulungu”

## **KULAPA TCHIMO LANU:**

Pemphero lamphamvu limene yona anapemphera likupezeka mu chaputala 2 cha buku la Yona. Yona navomereza tchimo lake ndikupempha chikhulukiro kwa Mulungu. Pamene mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu, muyenera kubwera pamaso pa Mulungu kuti mulape komanso kupempha Mulungu kuti akukhulukireni. Onetsetsani kuti mwadzikhulukira nokha. Sikoyenera kuti mubwere pagulu kuti mulape machimo anu pokhapokha ngati tchimo lanu lakhudza anthu ena amene mukuyera kupempha chikhulupiriro chao. Chofunika ndi chakuti mulape pamaso pa Mulungu.

## **ZINDIKIRANI PAMENE MWALAKWITSA:**

Kudzera mupemphero, Mau a Mulungu ndi chitsogozo cha Mzimu Woyera, zindikirani pamene munasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Yona anazindikira pamene anasemphana ndi chifuniro Cha Mulungu atangoyamba ulendo wake osemphana ndi kumene Mulungu anamuuzza kuti apite.

Nthawi zina palibe chimene mungapange kuti mukonze zimene mwalakwitsa kuposa kungolapa. Mwachitsanzo, Mfumu Davide itazindikira ntchimo lake ndi mkazi wa Uriya, palibe chimene anakapanga koposa kungolapa. Iye anali atalakwitsa kale ndipo panalibe chimene anakachita kuti akonze zinthu kupatula kungolapa. Koma pali zolakwitsa zina zimene inu mukhoza kuchitapo kanthu kuti mukonze zolakwikwazo ndipo ngati zili choncho, inuyo muyenera kuchitapo kanthu.

### **VUMBULUTSO...FUNANI CHITSOGOZO CHATSOPANO KWA MULUNGU:**

Pamene mwavomereza kulakwitsa kwanu, kupempha chikhululukiro, kuzindikira pamene mwalakwitsa ndikukonza zolakwitsa zonse, muyenera kupempha Mulungu kuti akupatseni chitsogozo chatsopano. Muyenera kuchotsa cholepheretsa china chilichonse kuti masamve kulankhula kwa Mulungu. Zolepheretsa zikhoza kukhala zinthu ngati; tchimo loukira, kuchita zinthu mwachifuniro chanu komanso kuganiza molakwika. Muyenera kukonzekeretsa makutu anu auzimu pakupemphera ndi kuwerenga mau a Mulungu kuti muzitha kumva pamene Mulungu akulankhula. Pamene Yona amafuna chitsogozo chatsopano kwa Mulungu, Mulungu anamulankhula kachiwiri nati kwa iye “Dzuka nupite ku Nenevi” (Yona 3:1-2). Mulungu atalankhula ndi Yona kachiwiri, iye anamvera pakupita mzinda waku Nenevi kukalalika uthenga Wabwino. Chifukwa chakulalika kwake, chitsitsimutso chachikulu chinachitika ndipo mzinda onse unalapa.

Baibulo liri ndi nkhani zambiri za anthu ngati Yona. Anthu amenewa analephera koma anavomereza kulephera kwao komanso ndi kupempha chikhululukiro kwa Mulungu. Pamene anakachita izi, Mulungu anawakhululukira ndi kuwapatsa chitsogozo chatsopano. Ndipo Mulungu akhoza kuchitanso izi pa Inu. Mulungu sakuyang’aniranso mbiri yakale lanu. Chimene akuyang’ana ndi chimene inuyo muli lero lino. Chimene Mulungu akuona ndi chimene inuyo mukhoza kukhala ngati mutamvera chifuniro chake.

### **KUFOTOKOZERA MWACHIDULE**

Chithunzi chili pansichi, chikufotozera ndondomeko zimene mukhoza kutsata pamene mwasephana ndi chifuniro cha Mulungu.

PAMENE MWASEMPHANA NDI CHIFUNIRO CHA MULUNG

Muyenera kuzindikira kulephera kwanu

Lapani machimo anu

Zindikirani pamene mwalephera

Konzani zimene mwalephera

Vumbulutso: funani chitsogozo chatsopano kuchokera kwa Mulungu



## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

---

---

---

2. Perekani zitsanzo zitatu za anthu amphamvu mu Baibulo amene agonjetsa kulephera kwao ndikubwelera ku chifuniro cha Mulungu.

---

---

---

3. Perekani zitsanzo za anthu atatu mu Baibulo amene anasemphana ndi chifuniro cha Mulungu ndipo mapeto awo anali olephera.

---

---

---

4. Tchulani ndondomeko zisanu zothandiza kuti mubwerere kuchifuniro cha Mulungu pamene mwalephera.

<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

### ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

1. Pa Luka 15:11-32, Yesu anafotokoza nkhani ya mnyamata amene anasiya atate ake ndi kupita kudziko lachilendo. Werengani nkhani imeneyi mosamalitsa makamaka gawo limene limafotokoza zakubweleranso kwa atate ake. Mukawerenga nkhani imeneyi, mupeza kuti mnyamatayu anatsata ndondomeko zonse zimene zimafunika kutsatidwa pokonza zinthu zolakwika.
2. Werenga zitsanzo za anhtu amene nthawi ina ya moyo wao anasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Kodi ndi anthu ati amene anakonza zolephera zao? Kodi anasinthabwani zolephera zao kukhala chipambano? Kodi ndi anthu ati amene sanakonze zolephera zao? Kodi zotsatira zake zinali chiani?

Abrahamu:	Genesis 20-21
Mose:	Eksodo; see also Acts 7:20-44
Balamu:	Numeri 22
Uzaya:	II Mbiri 26
Samisoni:	Oweruza 13-16
Davide:	II Samueli 11-12; Salimo 51.
Saulo:	I Samuel 8-15
Yona:	Buku la Yona
Petro:	Matthew, Mark, Luke, John, Acts
Yohane	Marko: Machitidwe 12:12, 25; 15:39; II Timoteyo 4:11

Mukhoza kuonjezera zitsanzo zina pa mndandanda umenewu pamene mukuwerenga Baibulo.

3. Yesu Khristu anafotokoza mafanizo awiri okhudza chifuniro cha Mulungu. Werengani mafanizo amenewa pa Luka 12:42-48 ndi Mateyu 21:28-32. Fotokozerani mwachidule zimene mwawerenga.

---

---

---

---

## CHAPUTALA 11

### CHIFUNIRO CHA MULUNGU NDI MAZUZO

#### ZOLINGA:

Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kupeza zifukwa zisanu zakukumana ndi mazuzo.
- Kuzindikira kuti mazuzo akhoza kukhala chifuniro cha Mulungu.
- Kusiyanyitsa pakati mazuzo ndi Mulungu komanso mazuzo opanda Mulungu.
- Kutchula zotsatira zabwino zamazuzo ngati chifuniro cha Mulungu.

#### VESI YOTSOGOLERA.

**Koteronso iwo akumva zowawa monga mwa cifuniro ca Mulungu aike moyo wao ndi kucita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika. (1 Petro 4:19)**

#### MAU OYAMBA

Munamva kulankhula kwa Mulungu, mwakhala mukufuna chitsogozo kuchokera kwa Iye ndipo chinaperekeredwa. Tsopano mwayamba ulendo wamoyo otsogozedwa ndi Mulungu. Koma ngati zotsatira zachiganizo chimene munapanga, mukukumana ndi mavuto amene sakanabwera ngati simunakatenga njira yatsopano yoyenda mu chifuniro cha Mulungu.

Kodi munamvetseradi bwino mau a Mulungu kapena munalakwitsa? Kodi nyengo zovuta mukukumana nazozizi ndi chizindikiro choti mukukhala mosemphana ndi chifuniro cha Mulungu? kodi Mulungu amalora kuti anthu okhulupira akumane ndi zowawa kapena mazuzo?

Pamene Yesu Khristu anali kutumikira pa dziko lapansi, ophunzira ake kapena omutsata ake ambiri anamuthawa iye atangoyamba kufotokoza za mazuzo amene adzakumane nao pamtanda (Yohane 6:55-66). Iwo anali kuyembekezera kuti Mesiya adzalamulira ndi mphamvu komanso ulemelero. Koma Iye amafotokoza za mazuzo. Chifukwa chakuti iwo sanamvetse, ambiri mwa Iwo amathawa.

Ngati simungamvetse chizunzo ngati mbali imodzi ya chifuniro cha Mulungu, nanunso munkhoza kumtembenikira Mulungu kapena kumusiya kumene pamene mudzakumane ndi nyengo zowawa. Mulungu sanalenge mazuzo, koma chizunzo chinalowa pa dziko lapansi

chifukwa cha tchimo la munthu (Genesis 3). Koma Mulungu akhoza kugwiritsa ntchito chinthu chimene zolinga zake ndi kubweretsa zoipa kuti akakwanilitse zolinga zake zabwino.

## **ZIFUKWA ZOKUMANIRA NDI CHIZUZO**

Baibulo limafotokoza zinthu zambiri zokhudza mavuto, chizuzo ndi nyengo zonse zowawa. Mukufotokozero mwachidule, pali njira zisanu zimene chizuzo chikhoza kubwera pa moyo wa munthu okhulupirira.

## **KUCHOKERA KWA ANTHU ENA OKUZUNGULIRANI**

Mazunzo akhoza kuchokera kwa anthu amene akuzungulirani inu. Yosefe ndi chitsanzo chabwino cha izi. Ngakhale kuti panalibe chimene iye analakwitsa, iye anagulitsidwa ku ukapolo ndi abale ake, ananamiziridwa ndi mkazi wa Potifara komanso anayiwalidwa ndi anthu amene anawathandiza ali mundende.

**Tsopano musaphwetekwe mtima, musadzikwiwira inu nokha, kuti munandigulitsira ine kuno, pakuti Mulungu ananditumiza ine patsogolo panu kuti ndisunge moyo. Ndipo Mulungu anatumiza ine patsogolo panu kuti ndikhazike inu mutsale m'dziko lapansi, ndi kusunga inu amoyo ndi cipulumutso cacikuru. (Genesis 45:5,7)**

## **NYENGO ZA MOYO.**

Njira yachiwiri imene mazuzo amabwelera ndi kudzera nyengo zathu zamoyo watsiku ndi tsiku. Chitsanzo chabwino ndi Naomi amene anakumana ndi imfa ya mwamuna wake komanso ndi ana ake. Nkhaniyi ukupezeka mu buku la Rute.

Imfa ndi mbali imodzo ya moyo wathu kufikira nthawi imene Yesu Khristu adzabwerenso kachiwiri ndikugonjetsa imfa. Imfa inalowa pa dziko lapansi chifukwa cha tchimo la munthu mmodzi. Ndipo imfa ndi chinthu chachilengedwe chimene munthu wina aliyense adzakumane nacho munthawi yoikikayo (Ahebri 9:27)

## **UTUMIKI WANU**

Chifukwa china chokumanira ndi chizunzo ndi chifukwa chomtumikira Mulungu. Chipangano Chatsopano chimakamba za kukumana ndi Mazuzo chifukwa cha dzina la Ambuye. (Machitidwe 9:16), chifukwa cha Khristu, (Afilipi 1:11-12) chifukwa chakuchita bwino (I Petro2:19-20; 3:17), chifukwa cha moyo wanu wangwiro (I Peter 3:14), chifukwa chakuti ndi inu okhulupirira (I Petro 4:15-16), ndi chifukwa chachifuniro cha Mulungu (I Petro 4:19).

Mtumwi Paulo ndi chitsanzo chabwino cha kukumana ndi mazuzo chifukwa cha utumiki. Anthu ena amaona ngati kukumana ndi mazuzo ndi chizindikiro cholephera komanso chopanda chikhulupiriro. Koma ngati izi zili choncho, ndiye kuti Paulo mtumwi anali munthu olephera kwambiri mu mbiri yonse ya mpingo komanso opanda chikhulupiriro.

Mtumwi Paulo anafotokoza kuti anathodwa kwakukulu komanso anakumana ndi nsautso waukulu (1 Akorinto 1:8). Iye akupereka chithunzithunzi china chimene sichikupereka lonjezano lina lilironse la mtendere komanso kuchita bwino. Pamene Mtumwi Paulo anaitanidwa ku utumiki, iye anauzidwa za mazuzo akulu amene adzakumane nao chifukwa cha khristu Yesu (Machitidwe 9:16).

Yankho la Paulo pankhani yamazuzo ndi lakuti kuti kwapatsidwa kwa inu kwaufulu cifukwa ca Kristu, si kukhulupirira kwa iye kokha, komatunso kumva zowawa cifukwa ca iye ”  
(Afilipi 1:29)

Paulo sanali yekha pa utumiki wake wachizunzo. Mpingo onse wachipangano Chatsopano unakumananso ndi chizunzo. Pa Ahebri chaputala 11 pali mbiri ya chizunzo chimene okhulupirira anakumana nacho. Koma ambiri mwa amayi ndi abambo amenewa anapulumsidwa ndi mphamvu ya Mulungu, zitseko zandende zinatseguka ndipo anatuluka ngati mfulu. Iwo anagamulidwa kuti aponyedwe mung’ anjo yamoto, koma iwo anatuluka osakhudzidwa ndi moto.

Koma ena mwa amayi ndi abambo amene anali okhulupirira sanalanditsidwe kumazunzo awo. Iwo anazunzidwa, kumangidwa ngakhale kuphedwa kumene chifukwa cha umboni wa uthenga wabwino (Ahebri 11:36-40). Timatsindika za chikhulupiriro cha anthu amoyo, koma Mulungu amaonetseranso mphamvu yake pamene okhulupirira akumwalira. Ichi ndi chikhulupiriro chenicheni chimene chimaonekera ngakhale munyengo zoipa osangoti munyengo yabwino pamene chiombolo cha Mulungu chimaonekera.

### **MKHONDO YOCHOKERA KU ZINTCHITO ZA SATANA:**

Mazunzo okhoza kulowanso mmoyo wanu chifukwa cha ntchito za Satana. Chitsanzo cha bwino ndi nkhani ya Yobu. Buku la Yobu likuyankha funso lakuti “ndi chifukwa chiani anthu olungama amakumana ndi mavuto”

Umboni ochokera kwa Mulungu unali oti Yobu anali munthu olungama (Yobu 1:2). Yobu sanakumane ndi mavuto chifukwa chakuti anachimwa ngati mmene anzake amafotokozerana. Iwo amakhulupirira kuti ngati Yobu angalape, ndiye kuti nyengo zake zisintha. Anzake a Yobu



amatenga zinthu molingana ndi mmene amazionera iwo ngati choonadi chimene chimagwira ntchito pa Munthu wina aliyense. Izi zili ngati kunena kuti “chifukwa chakuti Mulungu anamasula Petro mumdende, chomwechonso achita izi pamoyo wanu”. Koma izi sizoonza chifukwa anthu ambiri aphedwa ali kundende ngakhale kuti anali ndi chikhulupiriro chachikulu.

Tiyenera kusamalitsa ndi mmene timaonera mazunzo amene anthu ena akukumana nao chifukwa tikhoza kuwaganizira kuti akuzunzika chifukwa cha uchimo, kusakhulupirika kapena chifukwa cha kusakhulupirira. Baibulo limaphunzitsa kuti munthu ochimwa amakolora chivundi chifukwa chakufesa kuthupi (Agalatiya 6:8) Koma sitinganene kuti anthu olungama pamene akumana ndi zovuta ndiye kuti akukolora zimene anafesa.

Yobu sanakumane ndi mavuto chifukwa chakuti anachimwa ayi, iye anali munthu olungama. Ndipo anali Mulungu amene amachitira umboni wachiyero cha Yobu komanso angakhale pamaso pa anthu zimachitira umboni. Kunali kumwamba kokha kumene kumadziwa choyambitsa chenicheni cha mazuzo a Yobu. Nkhondo yauzimu inali ikuchitika mumtima mwake, mmaganizo ake angakhale mukudzipereka kwake kwa Mulungu.

Nkhondo yaikulu imakhala ikuchitika mdziko lauzimu chifukwa cha inu. Nkhondo imeneyi imaonekera mu nyengo zolimba za moyo wanu. Koma mfundo yaikulu yopezeka mu nkhani ya Yobu ndi yakuti palibe chinthu chimene chingachitike pamoyo wa munthu opanda Mulungu kudziwa. Mulungu samabweretsa chizunzo pamoyo wanu. Chizunzo chimachokera kwa Satana, koma malire ake amakhazikitsidwa ndi Mulungu.

### **MACHIMO ANU OMWE:**

Njira yachisanu imene chizunzo chimalowera mmoyo wanu ndi chifukwa cha uchimo wanu omwe. Yona ndi chitsanzo chimodzi cha mazunzo amenewa. Chifukwa chakusamvera Mulungu, Yona anatenga njira yosemphana ndi kumene Mulungu anamuza kuti akalalikire uthenga Wabwino mu mzinda wa Nenevi. Iye anakumana ndi mphepo yamphamvu panyanja imene zotsatira zake ndi zinali kukathera m’ mimba mwansomba chifukwa chauchimo wake.

Mavuto ayenera kuonedwa ngati chenjezo kuti tiunikirensa njira zathu pamaso pa Mulungu. Chifukwa mwina ngati Yona, mukhoza kukhala kuti mukukumana ndi mavuto chifukwa cha uchimo wanu. Baibulo limaonetsa kuti Mulungu amalanga iwo akusamvera mau ake. Kulanga kumatanthauza kupereka mwambo, kukonza kapena kudzudzula.

**Chalango ciri conse, pakucitika, sicimveka cokondweretsa, komatu cowawa; koma citatha, cipereka cipatso ca mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa naco, ndico ca cilungamo. (Ahebri 12:11)**

Mulungu amagwiritsa ntchito mazunzo pofuna kukukonzani komanso kukubwenzeretsani kuchifuniro chake pamoyo wanu.

**Ndisanazunzidwe ndinasokera; Koma tsopano ndisamalira mau anu. Kundikomera kuti ndinazunzidwa; Kuti ndiphunzire malemba anu. Ndidziwa kuti maweruzo anu ndiwo olungama, Yehova, Ndi kuti munandizunza ine mokhulupirika. (Masalmo 119:67,71,75)**

### **KAONEDWE KOYENERA KAMAZUNZO**

Msautso sichizindikiro chakuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Baibulo limafotokoza kuti nsautso wa olungama uchuluka (Salimo 34:9) Pamene mukumana ndi nsautso osati chifukwa chakuti mwachimwa, muyenera kukhala ndi kaonedwe kabwino ka mazunzo anuwo. Muyeso weniweni wauzimu wanu ndi mmene mumachitira mukakumana ndi nyengo za nsautso.

**Ukalefuka tsiku la tsoka Mphamvu yako icepa. (Miyambi 24:10)**

Baibulo likuonetsa mmene muyenera kuonera zinthu pamene mwakumana ndi msautso chifukwa cha chifuniro cha Mulungu.

**koma akamva zowawa ngati Mkristu asacite manyazi; koma alemekeze Mulungu m'dzina ili. (1 Petro 4:16)**

Muyenera kupereka moyo wanu onse kwa Mulungu pozindikira kuti Mulungu chikozero chake ndi chabwino munyengo zonse.

**Koteronso iwo akumva zowawa monga mwa cifuniro ca Mulungu aike moyo wao ndi kucita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika. (1 Petro 4:19)**

Muyenera kukhala okondwera pamene mukumana ndi chizunzo chifukwa chachifuniro cha Mulungu.

Paulo akufotokoza kuti:

**kondwerani m'ciyembekezo, pirirani m'masautso; limbikani cilimbikire m'kupemphera, (Aroma 12:12)**

**ndipo tigwiritsa nchito, ndi kucita ndi manja athu a ife tokha; polalatidwa tidalitsa; pozunzidwa, tipirira; (1 Akorinto 4:12)**

**m'zonse tidzitsimikizire ife tokha monga atumiki a Mulungu, m'kupirira kwambiri, m'zisautso, m'zikakamizo, m'zopsinja, 2 Akorinto 6:4 koma**

**Potero usacite manyazi pa umboni wa Ambuye wathu, kapena pa ine wandende wace; komatu umve masautso ndi Uthenga Wabwino, monga mwa mphamvu ya Mulungu; (2 Timoteo 1:8)**

**kuti asasunthike wina ndi zisautso izi, pakuti mudziwa nokha kuti adatiika ife ticite izi., (1 Atesalonika 3:3)**

**Koma iwe, khala maso m'zonse, imva zowawa, cita nchito ya mlaliki wa Uthenga Wabwino, kwaniritsa utumiki wako. (2 Timoteo 4:5)**

**Okondedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: koma popeza mulawana ndi Kristu zowawa zace, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wace mukakondwere kwakukurukuru. (1 Petro 4:12-13)**

Muyenera kupirira zowawa ngati msirikali:

**Umve zowawa pamodzi nane monga msilikari wabwino wa Kristu Yesu. (2 Timoteo 2:3)**

Paulo akufotokozera mwachidule mmene muyenera kuchitira mukakumana ndi chizunzo:

**ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:16-18)**

Paulo akutenga chizunzo ngati chinthu chotitumikira. Iye akufotokoza kuti chizunzo chimatithandiza pamene maso athu alunjika pa mphoto yapachimaliziro osati pa chizunzo kapena vuto lathu.

## **ZOTSATIRA ZABWINO ZA CHIZUNZO**

Zotsatira zabwino malinga ndi chifuniro cha Mulungu ndi izi:

## **CHIKHULUPIRIRO CHANU CHIMAYESEDWA:**

Chilichonse mudziko lauzimu chimayesedwa. Ichi ndi chifukwa chake mphamvu yachikhulupiriro chanu iyenera kuyesedwa:

**Ndipo mukamuitana ngati Alate, iye amene aweruzwa monga mwa nchito ya yense, wopanda tsankhu, khalani ndi mantha nthawi ya cilendo canu; (1 Petro 1:17)**

chimakhala chiyeso cha chikhulupiriro chanu pamene mupemphera ngati Yesu, kuti chikho chachizunzo chimupitirire, koma mapeto ake izi osachitika. Mmaloko mwake mumakakamizidwa kumwera chikho chamazuzo. Koma kudzera muchikhukulupiro, timaphunzira kuti zizitanthauza kuti mapemphero athu samayankhidwa koma kuti samayankhidwa munjira imene sitimayembekezera kapena timafuna.

#### **ZIMATHANDIZA KUTI TIKATONTHONZE ATHU ENA:**

**Wolemekezeka Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, Atate wa zifundo ndi Mulungu wa citonthozo conse, woo titonthoza ife m'nsautso yathu yonse, kuti tidzathe ife kutonthoza iwo okhala m'nsautso iri yonse, mwa citonthozo cimene titonthozedwa naco tokha ndi Mulungu. (2 Akorinto 1:3-4)**

Pamene mupereka chitonthozo cha Mulungu kwa ena:

**Mwa ici limbitsani manja ogooka, ndi maondo olobodoka; ndipo lambulani miseu yolunjika yoyendamo mapazi anu, kuti cotsimphinaco cisapatulidwe m'njira, koma ciciritsidwe. (Ahebri 12:12-13)**

#### **MUMAPHUNZIRA KUSAKHULUPIRIRA INU MWINI:**

Paulo akufotokoza cholinga cha chizunzo chake ku Asiya:

**Pakuti sitifuna abale, kuti mukhale osadziwa za cisautso cathu tinakomana naco m'Asiya, kuti tinathodwa kwakukuru, koposa mphamvu yathu, kotero kuti tinada nkhwana ngakhale za moyo wathu; koma tokha tinakhala naco citsutso ca imfa mwa ife tokha, kuti tisalimbike pa ife tokha, koma pa Mulungu wakuukitsa akufa; (2 Akorinto 1:8-9)**

Mumayamba kuzindikira kuti:

**Koma tiri naco cuma ici m'zotengera zadothi, kuti ukulu woposa wamphamvu ukhale wa Mulungu, wosacokera kwa ife; (2 Akorinto 4:7)**

## **ZIMATHANDIZA KUTI MUKUNZE MAKHALIDWE ABWINO:**

Makhalidwe amenewa amakuthandizani kuti mufanizidwe ndi chifaniziro cha Yesu. Ndipo ichi ndiye cholinga cha chikonzero cha Mulungu (Aroma 8:28-29; Ahebri 2:10,18)

## **NTCHITO ZA MULUNGU ZIMAONEKERA:**

Ophunzira a Yesu anafunsa kuti anachimwa ndi ndani ataona munthu wakhungu chibadwireni chake. Iwo anafunsa kuti kodi ndi makolo ake a munthuyo kapena amene anachimwa? Koma Yesu anawayankha nati:

**Yesu anayankha, Sanacimwa ameneyo, kapena atate wace ndi amace; koma kuti nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye. (Yohane 9:3)**

## **MPHAMVU YA MULUNGU IMAKHALA PA IFE:**

**Ndipo ananena kwa ine, Cisomo canga cikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufoko. Cifukwa cace makamaka ndidzadzitamandira ndikukondweratu m'maufoko anga, kuti mphamvu ya Kristu ikhale pa ine. (2 Akorinto 12:9)**

## **ZINTHU ZONSE ZOSAKHAZIKIKA ZIMACHOTSEDWA PAMOYO WANU:**

Zotsatira za chizunzo ndi zakuti zonse zimene ndi zosakhazikika zimachotsedwa pamoyo wanu. Mumasiya kudalira anthu, zinthu zakuthupi kapena zochitika zina ndi zina chifukwa zonsezi zimakhala kuti zakanika nthawi yansautso.

Mulungu akulonjeza kuti:

**amene mau ace anagwedeza dziko pamenepo; koma tsopano adalonjeza, ndi kuti, Kamodzinso ndidzagwedeza, si dziko lokha, komanso m'mwamba. Ndipo ici, cakuti kamodzinso, cilozera kusuntha kwace kwa zinthu zogwedezeka, monga kwa zinthu zolengedwa, kuti zinthu zosagwedezeka zikhale. (Ahebri 12:26-27)**

Munthawi ya mafunde amoyo, chinachilichonse chimene maziko ake si Mulungu simagwa. (Salimo 119:89 ndi Mateyu 7:24- 27)

## **CHIDWI CHANU CHA ZOCHITA CHIMASINTHA:**

Pamene mwakumana ndi nsautso, nthawi zambiri chidwi chanu chimagona pa chimene chayambitsa komanso zotsatira za nsautso kapena chizunzocho. Koma Mulungu akufuna kuti asinthe chidwi chathu kuti chichoke pa zinthu zosakhazikika ndi ndikukhazikika pa zinthu zamuyaya.

**Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:17-18)**

**Okonedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: koma popeza mulawana ndi Kristu zowawa zace, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wace mukakondwere kwakukurukuru. (1 Petro 4:12-13)**

**Ngati tipirira, tidzacinso ufumu ndi iye: ngati timkana Iye, Iyeyunso adzatikana ife: (2 Timoteo 2:12)**

### **CHIKHALIDWE CHATHU CHAKALE CHIMASINTHA:**

Mulungu analankhula ndi mtundu wa moab nati:

**Moabu wakhala m'mtendere kuyambira ubwana wace, wakhala pansenga, osatetekulidwa, sananke kundende; cifukwa cace makoleredwe ace alimobe mwa iye, pfungo lace silinasinthika. (Yeremiya 48:11)**

Chifukwa chakuti anthu aku moabu anali asanakumane ndi msautso kapena chiyesero cha chikhulupiriro chao, iwo sanali anthu osinthika. Iwo anakhala moyo otayilira ndipo anakhazikika pachuma chao. Sanakule muuzimu ngati mtundu wa anthu ndipo panalibe kusinthika kwina kulikonse pakati pao. Ndipo fungo lao lakale anali nalobe. Fungo la Moabu linali losasinthika.

Mazunzo amathandiza kuchotsa chikhalidwe chakale. Pamene mukutakasidwa, kukumana ndi mavuto, fungo lanu lachikunja limasinthika ndipo mumayamba kumveka fungo lauzimu.

### **MULUNGU AMAKHALA AKUKUKONZEKERETSANI UTUMIKI:**

Ngati mukufuna kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu, kapena mufuna kufananizidwa ndi Yesu Khristu ndikukhala chotengeramo chake, Mulungu akhoza kuyankha zonsezi pogwiritsa ntchito chizunzo kapena nsauto.

**Taona ndakuyenga, koma si monga siliva, ndakuyesa iwe m'ng'anjo ya masautso. (Yesaya 48:10)**

kudzera muchizunzo kapena nsauto, mumachoka pokhala mwana wa Mulungu ndikukhala osankhidwa wake wa Mulungu. Mazunzo obwera chifukwa cha chifuniro cha Mulungu amakukonzekeeretsani kuti mukagwire ntchito moyenera.

### **MUMAKONZEKERETSEDWA KUTI MULAMULIRE NDI KHRISTU:**

**Ngati tipirira, tidzacinanso ufumu ndi iye: ngati timkana Iye, Iyeyunso adzaticana ife:  
(2 Timoteo 2:12)**

**MAZUNZO AMABWERETSA MADALITSO AUZIMU:**

Yesu anati:

**Odala ali akuzunzidwa cifukwa ca cilungamo: cifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. Odala muli inu m'mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse cifukwa ca Ine. Sekerani, sangalalani: cifukwa mphototho yanu ndi yaikuru m'Mwamba: pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inu. (Mateyu 5:10-12)**

**MUMAPHUNZIRA KUMVERA KUDZERA MUMAZUNZO:**

**Angakhale anali Mwana, anaphunzira kumvera ndi izi adamva kuwawa nazo;  
(Ahebri 5:8)**

**MAU A MULUNGU AMAYESEDWA MKATI MWANU:**

**Mau a Yehova ndi mau oona; Ngati siliva woyenga m'ng'anjo yadothi, Yoiyeretsa kasanu ndi kawiri. (Masalmo 12:6)**

**MAZUNZO AMATITHANDIZA KUTI TIDZICHEPETSE:**

**Amene anakutsogolerani m'cipululu cacikuru ndi coopsaco, munali njoka zamoto, ndi zinkhanira, mouma mopanda madzi; amene anakuturutsirani madzi m'thantwe lansangalabwi; amene anakudyetsani m'cipululu ndi mana, amene makolo anu sanawadziwa; kuti akucepetseni, ndi kuti akuyeseni, kuti akucitireni cokoma potsiriza panu; (Deuteronomo 8:15-16)**

**MAZUNZO AMAPANGITSA KUTI MUKULE:**

**Pakupfuula ine mundiyankhe, Mulungu wa cilungamo canga; Pondicepera mwandikulitsira malo: Ndcitireni cifundo, imvani pemphero langa. ( Masalmo 4:1)**

**MUMAKHALA CHIFUPI NDI MULUNGU:**

Mazunzo amathandiza kuti mukhale ndi ubale waukulu ndi Mulungu. Atakumana ndi nsautso waukulu, Yobu anazindikira choonadi chimenechi. Ndipo anati:

**Kumva ndidamva mbiri yanu, Koma tsopano ndikupenyani maso; Cifukwa cace ndekha ndidzinyansa, ndi kulapa M'pfumbi ndi mapulusa. (Yobu 42:5-6)**

Ambiri mwa ife timamudziwa Mulungu mwapamwambamwamba. Pamene zinthu zikuyenda Mulungu samakhalanso ofunika pamoyo wathu. Koma zinthu zikayamba kuvuta ndi pamene Mulungu amakhala ofunikira pamoyo wathu. Yobu anamudziwa Mulungu mozama pamene anakumana ndi nsautso. Izi sizikutanthauza kuti iye samamudziwa Mulungu ayi, koma kumudziwa kwake kunali kungokhala ndi chidziwitso chabe cha Mulungu. Koma iye atakumana ndi nsautso, anamudziwa Mulungu kudzera munyengo zimene anadutsamo.

Paulo nayenso akufotokoza mfundo yomweyi:

**Kuti ndimzindikire iye, ndi mphamvu ya kuuka kwace, ndi ciyanjano ca zowawa zace, pofanizidwa ndi imfa yace; (Afilipi 3:10)**

Mukhodza kudziwa Mulungu kudzera muchiyanjano cha chizunzo.

Munyengo yonse yansautso wake, Yobu amafunsa Mulungu mafunso. Iye amaona ngati kuti gwero lan nsautso wa wake linali Mulungu. sikutu ndi zolakwika kufunsa Mulungu mafunso. Mwachitsanzo, ngakhale kuti Yesu amadziwa kuti cholinga chake chobwelera pa dziko lapansi chinali kudzapulumutsa munthu kumachimo. Koma utafika nsautso, iye amafula nati, Mulungu wanga Mulungu wanga, mwandisirani? Mau amane analakhula litatha funso limeneli ndi amene ali ofunika kwambiri chifukwa iye anati “mzimu wanga ndiupereka mmanka mwanu”

Ngakhale kuti Yobu anali ndi mafunso, koma iye anati:

**Iye adzakhanso cipulumutso canga, Pakuti wonyoza Mulungu sadzafika pamaso pace. (Yobu 13:16)**

**Koma ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi moyo, Nadzauka potsiriza papfumbi. Ndipo khungu langa litaonongeka, Pamenepo wopanda thupi langa, ndidzapenya Mulungu; (Yobu 19:25-26)**

Mafunso onse atatha, Yobu anachoka pokhazikika pa “iye” ndikukhazikika pa “Inu.” Muyenera kupereka nsautso wanu komanso mafunso onse osayankhidwa mmanja mwa Mulungu.

**Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, Osacirikizika pa luntha lako; (Miyambi 3:5)**

Mulungu amaonetsera pang'ono cholinga cha nsautso wanu, koma ndi zotheke kuti simungathe kumvetsa chinachilichonse.



## **Kubisa kanthu ndi ulemerero wa Mulungu; (Miyambi 25:2)**

**Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)**

Pali zinthu zina zobisika zimene ndi za Mulungu yekha. Ndipo ngati Yobu, mwina simungathe kumvetsa cholinga cha nsautso wanu.

**Yehova alongosola mayendedwe a mwamuna; Munthu tsono angazindikire bwanji njira yace? ( Miyambi 20:24)**

Pamapeto azonse Mulungu atalankhula ndi Yobu pogwiritsa ntchito zitsanzo zachilengedwe zimene Yobu sanathe kufotokozerana. Mfumdo imene Mulungu amatsindika ndi yakuti ngati yobu sanamvetse zitsanzo zakuthupi zimene ndi zooneka ndi maso, iye sakanamvetsa zinthu zosaoneka ndi maso za dziko lauzimu. Yobu atakumana ndi Mulungu, zinali zopanda ntchito kuti mafunso ake analibe mayakho. Nkhawa zonse zobwera chifukwa chakuganiza kwa umuthu zinamuthera. Mayankho amafunso ake anali chikhulupiriro.

Pamene mwamudziwa Mulungu mwakuya kudzera muchizunzo, mumadziona mmene muyenera kudzionera. Zotsatira zokumana ndi Mulungu maso ndi maso zimakhala zoposa mafunso onse ndi kukambirana komwe kungachite.

Pamene Yobu anafika pamaso pa Mulungu, panalibe yankho lina lilironse limene anakanapereka. Iye anapatsidwa choonadi china chokhudza chizunzo. Mafunso ake onse anakhala opanda kanthu pamaso pa Mulungu ndipo panalibeso kukaika kwina kulikonse kumene anakhala nako.

## **NAMONDWE WAMOYO**

Chizunzo nthawi zina chimafaniziridwa ndi namondwe. Pamene mukumana ndi chizunzo, mumakhala kuti mwakumana ndi namondwe mauzimu. Ndipo izi zimakhudza moyo wanu kuthupi, kuuzimu ngakhale maganzidwe anu amene.

Baibulo limafotokoza za namondwe amene ophunzira anakumana naye. Werengani nkhani imeneyi pa Marko 4:35-41. Namondwe amaneyu inalinkhondo yochokera kwa Satana. Yesu anauza ophunzira kuti apite tsidya lina lanyanja ndipo iye anali nao limodzi pakati pao. Satana amafuna kuwarepheretsa kupita tsidya lina chifukwa cha zozizwa zimene zimayenera kuchitika dera limene iwo amapita (Marko 5) Koma Yesu anaonetsera ulamuliro pa namondwe amaneyu pamene anadzudzula mphamvu ya mdaniyo. Bata linabweleranso panyanja ndipo iwo anapitiriza ulendo wao popanda chovuta china chilichonse.

Namondwe wa Satana ndi china chilichonse chimene chimakulepheretsani inu kukwaniritsa chifuniro cha Mulungu pamoyo wanu. Izi sizimabwera chifukwa chakuti mwachimwa komanso sichifuniro cha Ambuye kuti mukumane ndi zimenezi. Pamene mwakumana ndi mavuto ngati amenewa muyenera kugwititsa ntchito ulamuliro wanu pa mdani wanuyo. Yesu watipatsa ulamuliro pa mphamvu ina iliyonse ya mdani.

Pali nkhani ziwiri za namondwe wakuthupi zimene zikuonetsera chizunzo ngati zotsatira za uchimo komanso chizunzo ngati chifuniro cha Mulungu. Werengani nkhani ya Yona pa chaputala 1 komanso ya Paulo pamachitidwe 27. Ndipo gwiritsani ntchito chithunzi chili pansichi.

<b>Yona</b>	<b>Paulo</b>
Yona anadziika yekha mu namondwe lake	Paulo sanagwe munamondwe chifukwa cha vuto
Iye analipire ndalama kuti ayende panyanja	Iye anawaretsa kuti asayende panyanja
Iye anali choyambitsa nomondweyo	Anali yankho osati choyambitsa
Analibe mdalitso wa Ambuye	Anali ndi mdalitso wa Mulungu
Oyendetsa ngalawayo anali ndi mantha	oyendetsa ngalawayo anali ndi nsangala.
Kuti apulumutsidwe:	Kuti apulumutsidwe:
Yona amayenera kuponyedwa mmadzi	Onse amayenera kukhala mungalawoyo.

Pali kusiya pakati pakukumana ndi namondwe chifukwa cha chifuniro cha Mulungu ndi kukumana ndi namondwe chifukwa chakuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Ngati mukumana ndi namodwe chifukwa chakuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu, iyi ndi nyengo imene mumachita kuipanga nokha. Mwachitsanzo, okhulupilira amene wakwatira munthu amakumana ndi mavuto chifukwa chakuti asemphana ndi mfundo za Baibulo.

Pamene mwayambitsa namondwe pamoyo wanu, mumakhala kuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu ndipo simukumvera Malamulo ake. Nthawi zambiri simumadziwa kukula kwa zotsatira za nyengo yanu. Mumakhala kuti mwagona pamene namondwe amakhala akukulirabe pakati panu. Mdalitso wa Mulungu sumakhala nanu ndipo onse okuzunguliranai amakhalanso amantha. Namondwe ameneyi si nkhondo yochokera kwa Satana ayi, koma ndi chidzudzulo chochokera kwa Mulungu amene amakukondani ndipo akufuna kuti mubwelerenso ndikuyamba kuchitsa chifuniro cha Mulungu. Mukhoza kulengeza malonjezano amphamvu pa m'daniyo, koma izi sizimasintha nyengo zanu.

Pamene mwazindikira kuti nyengo yanu ya chizunzo ikubwera chifukwa cha tchimo, choyenera kuchita ndi kupempha Mulungu kuti atikhululukire.

Pamene mukumana ndi nsautso chifukwa cha chifuniro cha Mulungu, nyengo yake imakhala yosiyana. Izi zimachitika osati chifukwa chakuti mwachita ntchimo kapena kuti mwalakwitsa ayi. Inuyo mumakhala yankho ku vuto limene lakuzungulirani. Ngati Paulo, mukhoza kutenga ulamuliro wauzimu chifukwa mdalitso wa Mulungu uli pa inu komanso mukhoza kulimbikitsa anthu ena chifukwa ndinu yankho ku namondwe osati choyambitsa cha namwodwe. Simuyenera kutsika ngalawa chifukwa chothawa nsautso. Koma muyenerabe kukhala mungalawa yansautso chifukwa ndi chifunoro cha Mulungu.

## **TIKUYENERA KUYEMBEKEZERA CHIFUZUNZO**

Pamene mukumana ndi chizunzo muyenera kuzindikira kuti simuli nokha ayi:

**Podziwa kuti zowawa zomwezo zirimkukwaniridwa pa abale anu ali m'dziko. 1 Petro 5:9**

Namodwe pamoyo wa munthu ndi chinthu chosathawika ndipo ndi zovuta kupewa. Chitsanzo chabwino cha mfundo imeneyi ndi Mateyu 7:24-27. Nsautso ndi zinthu zimene zimabwera pa anthu amene moyo wao wamangika pa Mulungu komanso ngakhale iwo amene sanatero. Koma maziko amoyo wa munthu ndi amene amaonetsera zotsatira za namondwe pamoyo.

Tiyenera kuyembekezera chizunzo ngati mbali imodzi ya chifuniro cha Mulungu:

**Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Kristu Yesu, adzamva mazunzo. (2 Timoteo 3:12)**

**kuti kwapatsidwa kwa inu kwaufulu cifukwa ca Kristu, si kukhulupirira kwa iye kokha, komatunso kumva zowawa cifukwa ca iye, Afilipi 1:29**

**. . . kuti mu-kawerengedwe oyenera ufumu wa Mulungu, umenenso mumvera zowawa; (2 Atesalonika 1:5)**

**Pakutinso, pamenetinali ndi inu tinakuuziranitu kuti tidzamva zisautso; monga kudacitika, monganso mudziwa. (1 Atesalonika 3:4)**

**Pamenepo adzakuperekani kunsautso, nadzakuphani; ndipo anthu a mitundu yonse adzadana nanu, cifukwa ca dzina langa. Mateyu 24:9**

**Koma zisanacitike izi, anthu adzakuthirani manja, nadzakuzunzani, nadzapereka inu ku masunagoge ndi ndende, nadzamuka nanu kwa mafumu ndi akazembe, cifukwa ca dzina langa. (Luka 21:12)**

**Kumbukilani mau amene Ine ndinanena kwa inu, Kapolo sali wamkuru ndi mbuye wace. Ngati anandilondalonda Ine, adzakulonda-londani inunso; ngati anasunga mau anga, adzasunga anunso. (Yohane 15:20)**

Mbali imodzi yophunzitsa anthu ongobadwa kumene mumpingo oyamba inali kuwaphunzita kuti adzakumana ndi nsautso. Ichi ndi chinthu chimene tikusemphana nacho mu mpingo wa lero.

**Nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri. (Macitidwe 14:22)**

Kuitana kwa Yesu Khristu ndi kwakuti tidzikanize tokha komanso kukumana ndi chizunzo:

**Nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri. (Macitidwe 14:22)**

### **PAMENE MTSINJE WAUMA**

Pali nkhani ina yopatsa chidwi ya Chipangano Chakale ya munthu amene anakumana ndi chizunzo chifukwa cha chifuniro cha Mulungu. Iyi ndi nkhani ya Eliya amene anakumana ndi nsautso osiyanasiyana munthawi imene anali kupereka uneneri wa Mulungu kwa Israeli. Koma nkhani imene tikufuna kuti titsindike ndi imene ikupezeka pa 1 Mafumu 17. Musanapitilire ndi phunziro ili, werengani nkhanayi.

Mulungu atamulamula Eliya kuti akhale ku mtsinje wa Keriti, amamudyetsa iye modabwitsa. Makungubwi amabwera kudzadyetsa Iye ndipo iye anali kumwa madzi mumtsinje ngakhale kuti kunali njala ndi chilala munthawi imeneyi. Koma mukupita kwa nthawi, mtsinje uja unamphwa. Koma ndi chifukwa chiani Mulungu anatumiza Eliya ku mtsinje umene amadziwa kuti ukaphwa?

Nthawi zina chifuniro cha Mulungu chimatitengera kumitsinje youma. Koma pamene mwakumana ndi nsautso sizikukutanthauza kuti tasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Eliya sikuti anali atasemphana ndi chifuniro cha Mulungu ayi. Mulungu anamutsogolera Eliya ku Keriti ndikumpatsanso madzi ndi zosowa zonse. Uwu unali mdalitso ochokera kwa Mulungu, koma itafika nthawi yoti ayende chitsogolo, Mulungu analora mtsinje kuti uwume. Izi zinamudabwitsa Eliya.

Mwina mkhutheka Kutu Mulungu akukutsogolerani ku “mtsinje wa Keriti.” Mukudziwa kuti munamva mau a Mulungu achitsogozo. Mulungu anakudalitsani pa mtsinje pokupatsani zosowa zanu zonse. Koma mwina mtsinje wanu wauma simukumvanso kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu mkati mwanu. Mwina mkhutheka kuti anthu akutembenukirani kapena kuti utsogoleri umene uli pamwamba panu Watseka mtsinje kuti usayendenso. Kapena pa zifukwa zina mtsinje wanu wauma.

Pamene mtsinje wanu wauma mukhoza kuchita zinthu zingapo:

1. Muuzimu mukhoza kukhala mbali mwa mtsinje ndi kumadandaula zimene zakukuchitikirani. Mukhoza kutaya nthawi yanu moyo wanu onse kukhalira kulira komanso kudandaula chimene chakuchitikirani. Mwina mukhoza kumafunsa ngati Mulungu anakutengeranidi kumalo kumene muli. Kodi ngati iye amadziwa kuti mtsinje udzauma ndi chifukwa chiani anakutengerani kumalo amenewo? Kapena mwina munasephana ndi chifuniro cha Mulungu?
2. Mukhoza kuzindikira kuti Mulungu anakutengeranidi ku mtsinje, ndipo wakonzeka kuti akutengelereni kugawo lina la chifuniro chake. Iye akufuna amvetsere kuchokera kwa inu.

Ngati mtsinje sungaume, ngati Mulungu sangalore kuti tidutse nyengo zowawa, ndizovuta kuti amvetsere kuchokera kwa ife. Chimodzimodzi ngati Eliya, Iye sakanasuntha malo amene Mulungu anamuika ndikuyamba kuchita zinthu zatsopano ngati mtsinje sukanauma. Izi zikuonetsera kuti mtsinje youma imatitsogolera ku zinthu zina zatsopano. Eliya asanakuma ndi nyengo za kumtsinje, iye anali atangotumikira kwa anthu ochepa chabe. Koma atadutsa munyengo imeneyi imene inakuza moyo wake, iye anatumikira kwa anthu miyandamiyanda. Iye

anaima, pa phiri la Kalimel ndi kulankhula pamaso pa mafuko opembedza mafano nawalankhula za Mulungu m' modzi weniweni.

Pamene mwakumana ndi nyengo za mtsinje owuma, chikhulupiriro chanu chiyenera kuimabe chifukwa mumakhala kuti mwaima mphepete mwa mtsinje oti mulandire vumbulutso lanu lochokera kwa Mulungu. Simukuyenera kufunsa mafunso ambiri. Chimene muyenera kuchita ndi kupita chitsogolo kuti muyende mudongosolo lina la chikonzero cha Mulungu.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

---

---

---

2. Kodi ndi njira ziti zisanu zimene chizunzo chimabwelera pa okhulupirira?

---

---

---

---

3. Tchulani ubwino iwiri wa chizunzo chobwera chifukwa cha chofuniro cha Mulungu.

---

---

---

4. Tchulanai kaonedwe kazinthu koyera kamene okhulupirira ayenera kukhala nako pamene akumana ndi chizunzo:

5. Werengani ziganizo izi. Ngati chiganizo chili cholondola, lembani T kutsogolo kwa chiganizocho. Ndipo lembani F kutsogolo kwa chiganizo chimene sicholondola.

- a. \_\_\_\_ Sichifuniro cha Mulungu kuti mukumane ndi chizunzo.
- b. \_\_\_\_ Ngati mukukumana ndi mavuto ndiye kuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu.
- c. \_\_\_\_ Paulo anali atasemphana ndi chifuniro cha Mulungu pamene amakumana ndi namondwe panyanja.
- d. \_\_\_\_ Pamene mukumana ndi chizunzo chifukwa cha kusemphana ndi chifuniro cha Mulungu mumakhala kuti choyambitsa ndinu nomwe chifukwa chakusamvera.
- e. \_\_\_\_ Mulungu amatilanga chifukwa chakuti amatikonda ndipo cholinga chake ndikutibwenzeretsa ife kuti tiyende malinga ndi chifuniro cha Mulungu.
- f. \_\_\_\_ Mtsinje sukanauma zinakhala kuti Eliya sanasemphane ndi chifuniro cha Mulungu.
- g. \_\_\_\_ Nthawi zina Mulungu amagwiritsa ntchito chizunzo ndi cholinga tiyike chidwi chake pa Iye ndikutipatsa chitsogozo chatsopano.
- h. \_\_\_\_ Baibulo limaphunzitsa kuti ndi anthu ochimwa okha amene amakumana ndi chizunzo.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

## ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani buku la Chibvumbulutso pa mutu wachizuzo. Ndipo lembani zimene mupeze pa nkani ya chizunzo.

---

---

---

---

---

---

2. Santhulani mitu ili pansiyi yokhudza chizunzo

### ZOWAWA:

II Timoteyo 2:3

Machitidwe 14:20; Aroma 5:3; 12:12; I Atesalonika 3:4, II Atesalonika 1:4

### KUZUNZIDWA:

Mateyu 5:10-12, 44; 13:21; Marko 4:17; Luke 11:49; 21:12; John 15:20; I Akorinto

4:12; II Akorinto 4:9; Machitidwe 8:1; 11:19; 13:50; II Atesalonika 3:12; Aroma 8:35;

Agalatiya 6:12

### MAZUNZO:

I Petro 5:10; Afilipo 1:29; 3:8; 4:12; II Akorinto 1:6; II Timoteyo 2:12; 3:12;

Agalatiya 5:11; 6:12; Machitidwe 9:16; I Atesalonika 3:4; II Atesalonika 1:5

### NSAUTSO:

Salimo 34:19; 119:67,71,75; Mateyu 24:9; Acts 20:23; II Akorinto 2:4; 4:17; 6:4; I

Atesalonika 3:3; II Timoteyo 1:8; 3:11; 4:5; II Akorinto 1:6; Yakobo 5:10; Ahebri10:32-33 ndi chaputala 11



## CHAPUTALA 12

### MAGAWO ASANU NDI AWIRI AMAVUMBULUTSO

#### ZOLINGA

Pamene mwamaliza phunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi Yotsogolera osaonera.
- Kulemba magawo asanu ndi awiri a vumbulutso la dongosolo la Mulungu.
- Kuzindikira chifaniziro cha izi mu zitsanzo za Baibulo

#### Vesi Yotsogolera:

**Ndipo makutu ako adzamva mau kumbuyo kwa iwe akuti, Njira ndi iyi, yendani inu m'menemo: potembenukira inu kulamanja, ndi potembenukira kulamanzere. (Yesaya 30:21)**

#### MAU OYAMBA

Mu phunziro ili, mwaphunzira zambiri zokhudza kuzidindikira kulankhula kwa Mulungu. Taonanso zinthu zomuyenera munthu kuti azindikire mau a Mulungu. Mwaphunziranso tanthauzo la chifuniziro cha chifuniro cha Mulungu ndi njira zimene Mulungu amagwiritsa ntchito polankhula ndi munthu.

Chenjezo lokhudza kugwiritsa ntchito njira zachikunja zofunira chitsogozo komanso kupanga chiganizo zokhudza mtchitidwe okaikitsa. Tinaonanso zinthu zimene muyenera kuchita pamene mwalephera kuchita chifuniro cha Mulungu. Mfundo ina imene taona ndi yokhudza chizunzo chobwera chifukwa cha chifuniro cha Mulungu.

Chaputala chomaliza chifokoza magawo asanu ndi awiri amene muyenera kudutsamo molingana nd dongosolo lachikonzero cha Mulungu. Mumadutsa magawo onsewa pamene mukhale mukuyenda ndi Mulungu.

#### VUMBUMBULUTSO LA CHIDZIWITSO

Mu dziko limene ndi losokonekera, Mulungu analonjeza mavumbulutso kwa ana ake ,vumbulutso lachidziwitso. Izi zikutanthauza kuti iye adzaonetsera dongosolo lake la chikonzero cha moyo wanu, komanso adzakuonetserani chidziwitso cha nyengo za moyo wanu.

Ndipo makutu ako adzamva mau kumbuyo kwa iwe akuti, Njira ndi iyi, yendani inu m'menemo: potembenukira inu kulamanja, ndi potembenukira kulamanzere. Yesaya 30:21

Pamene Mulungu waonetsera chikonzero chake, pali magawo asanu ndi awiri amene muyenera kudutsamo kuti vumbulutso likhazikike mwainu. Magawo amanewa akupezeka pa Luka 1:26-47. Werengani ndime imeneyi musanapitilire ndime imeneyi ndi phunziro ili. . Ndime imeneyi imakamba za vumbulutso limene Mariya analandita kuti adzakahala mayi wa Mesiya, Yesu Khristu.

Nkhani imeneyi ili ndi magawo asanu ndi limodzi amene Mariya ayenera kudutsamo pamene chikonzero cha Mulungu chikuonetseredwa. Magawo amenewa akhoza kuonedwa pena paliponse pamene pali vumbulutso la chikonzero cha Mulungu. Awa ndi magawo amene muyenera kudutsamo pamene mukkhale mukulandira mavumbulutso a chidziwitso cha dongosolo kapena chikonzero cha Mulungu pa moyo wanu.

### **GAWO LAKUSOWA MTENDERE/ KUSAUTSIKA**

**Ndipo pakulowa mngelo anati kwa iye, Tikuoneni, wocitidwa cisomo, Ambuye ali ndi iwe. Koma iye ananthunthumira ndi mau awa, nasinkhasinkha kulankhula uku nkutani. (Luka 1:28-29)**

Pamene angero anaonekera kwa Mariya iye ananthunthumira kapena kuti anasowa mtendere mkati mwa mzimu wake. Pame Mulungu akufuna kukupatsana chinthu chatsopano, nthawi zambiri munthunthumira mkati mwanu. Iye amalora kuti musautsike ndi nyengo zimene mukudutsamozo ndi cholingo choti maso anu akhale pa iye.

Mwina mkutheka kuti mukufunsa mafunso chifukwa cha nyengo zosautsa zimene mukudutsamo. Mwasautsika ndipo simukumvetsa chikuchititsa kuti musautsike mmoyo wanu. Chimene Mulungu akufuna ndi chakuti chidwi chanu chikhale pa Mulungu. Mwina mkutheka kuti ngati muli okondwa komanso okhutitsidwa mkati mwanu, mukhoza kusiya kufunafuna chitsogozao chatsopano kuchokera kwa Mulungu. Ichi ndi chifukwa chimene Mulungu amakulolerani kuti musautsike mu gawo loyamba la kulandira mavumbulutso.

### **GAWO LACHIWIRI: VUMBULUTSO**

**Ndipo mngelo anati kwa iye, Usaope, Mariya; pakuti wapeza cisomo ndi Mulungu. Ndipo taona, udzakhala ndi pakati, nudzabala mwana wamwamuna, nudzamucha dzina lace Yesu. (Luka 1:30-3)**

Pamene chidwi chanu mwaika pa Mulungu chifukwa chakusautsika, ndipamene Mulungu amaonetsera chikonzero chake pa inu. Ili ndi gawo lachiwiri lamavumbulutso.

**Undiitane Ine, ndipo Ine ndidzakuyankha iwe, ndipo ndidzakusonyeza iwe zazikuru, ndi zolakika, zimene suzidziwa. (Yeremiya 33:3)**

Chifukwa chakuti mzimu wa Mariya unasautsika, chidwi chake chinasuntha ndikukhazikika pa Mulungu ndipo Mulungu anaotsera chikonzero chake pa iye kuti adzakhala mayi wa Mesiya, Yesu Khristu.

### **GAWO LACHITATU: CHIDODO**

**Undiitane Ine, ndipo Ine ndidzakuyankha iwe, ndipo ndidzakusonyeza iwe zazikuru, ndi zolakika, zimene suzidziwa. (Yeremiya 33:3)**

Mariya anatenga nthawi kuti avomereze vumbulutso lija, iye anadzifunsa kuti izi zingatheke bwanji?

Pamene Mulungu wakuonetsera chikonzero chatsopano pa moyo wanu, nthawi zambiri mumadabwitsika. Mumatha kuona ngati inuyo simungakwanitse kapena kuti sindinu oyenera. Mumaona ngati ndi chinthu chachikulu kuti muchite. Mumaganizira zifukwa zimene chikonzerocho sichingathekere. Ndipo mapeto ake mumachita chidodo.

Zinthu ziwiri zimachitika mu gawo limeneli:

- Mumapereka zifukwa kuti simukwanitsa komanso mafunso.
- Mulungu amayankha zinthu zimenezi pofotokozero chikonzero chake.

Anthu ena amatenga nthawi yaitali akuchita chidodo. Ena amatenga zaka zambiri akupereka zifukwa zimene sangakwanitsire. Koma ngati simungasunthe mu gawo lakuchita chidodo, simungakwaniritse vumbulutso la Mulungu.

### **GAWO LACHINAYI: KUVOMEREZA:**

**Ndipo Mariya anati, Onani, mdzakazi wa Ambuye; kukhale kwa ine monga mwa mau anu. Ndipo mngelo anacoka kwa iye. (Luka 1:38)**

Mwachangu, Mariya anavomereza chikonzero cha Mulungu ndikusiya chidodo chake. Izi zikutanthauza kuti anasiya chifuniro chake ndi kuvomereza chitsogozo chatsopano chochokera kwa Mulungu.

## **GAWO LACHISANU: CHITSIKIMIZO**

**Ndipo wodala ali iye amene anakhulupirira; cifukwa zidzacididwa zinthu zimene Ambuye analankhula naye. (Luka 1:45)**

Ili ndi gawo limene Mulungu amapereka chitsikimikizo cha chikonzero chake. Mwachitsanzo, Mariya anaima ndipo ichi chinali chitsimikizo pathupi lake. Ngati mwavomereza chikonzero cha Mulungu, sipatenga nthawi kuti mulandire chitsikimizo cha chichikonzerocho.

## **GAWO LACHISANU NDI CHIMODZI: MATAMANDO:**

**Ndipo Mariya anati, Moyo wanga ulemekeza Ambuye, (Luka 1:46 )**

Mariya anakondwera ndi chikonzero cha Mulungu. Werengani nkhani imeneyi pa Luka 1:45-55. Pamene mwavomereza chikonzero cha Mulungu pa moyo wanu, izi zimabweretsa chimwemwe mmoyo wanu ndipo zotsatira zake ndi kumukweza Mulungu.

## **MAU OMALIZA: VETSERANI MAU AKE**

Mu phunziro ili, mwaphunzira ndondomeko zothandiza kuti muzindikire kulankhula kwa Mulungu kapena kuti mau ake. Pamene mukumva mau ake, kumbukirani lonjezo ili:

**Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezere. (Yeremiya 29:11)**

Mulungu apitirira kukutsogolerani kufikira imfa:

**Pakuti Mulungu ameneyo ndiye Mulungu wathu ku nthawi za nthawi: Adzatitsogolera kufikira imfa. (Masalmo 48:14)**

Chitsogozo chake chidzapitilirabe mu dziko ndi kumwamba kwatsopano;

**Cifukwa Mwanawankhosa wakukhala pakati pa mpando wacifumu adzawaweta, nadzawatsogolera ku akasupe a madzi a moyo, ndipo Mulungu adzawapukutira misozi yonse pamaso pao. (Cibvumbulutso 7:17)**

Mulungu samakhale chete, ngati mungamvetsere, mukhoza kumumvabe pakati pa phokoso ndi chinam'balala cha dziko lapansi ndi chisokonekero cha mau a dziko lapansi. Iye amalankhula ndipo inu mukhoza kudziwa chifuniro chake.

**Koma Mulungu wa mtendere amene anabwera naye woturuka mwa akufa 1 Mbusa wamkuru wa nkhosa 2 ndi mwazi wa cipangano cosatha, ndiye Ambuye wathu Yesu, 3 akuyeseni inu opanda cirema m'cinthu ciri conse cabwino, kuti mucite cifuniro cacej ndi kucita mwa ife comkondweretsa pamaso pace, mwa Yesu Kristu; kwa Iyeyu ukhale ulemerero ku nthawi za nthawi. Amen. (Ahebri 13:20-21)**

**MAYESO ODZIYESA NOKHA**

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

---

---

---

---

2. Tchulani magawo asanu ndi limodzi mavumbulutso a chikonzero cha Mulungu

---

---

---

---

---

---

---

---

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

## ZONJEZERA POPHUNZIRA

Santhulani ma gawo asanu ndi limodzi alandira vumbulutso la Mulungu mmoyo wa Mose ndi Gideoni:

### **Mose: Eksodo 1-15**

Kusautsika:	Nyengo yake kwa Igupto (atapha munthu)
Vumbulutso:	chitsamba chikuyaka moto
Chidodo:	munthu wachibwibwi/osadziwa kulankhula
Kuvomereza:	anavomereza kupita
Chitsikimizo:	zozizwa pamaso pa Falao
Matamando:	chimwemwe ataoloka nyanja ya mtchere

### **Gideoni: Oweruza 6**

Kusautsika:	akumenya tiligu vesi 13
Vumbulutso:	Mngero anamuonekera iye mu vesi 12 and 14
Chidodo:	"banja langa ndi laling'ono, ndine osauka" vesi 15
Kuvomereza:	Vesi 17
Chitsikimikizo:	"ndionetsereni chizindikiro" vesi 17- 23
Matamando:	Vesi 24. Anamanga gome kuti alemekeze Mulungu.

Kodi mukhoza kupeza zitsanzo zina m' Baibulo?

Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili

## MAYANKO AMAYESO ODZIYESA NOKHA

### CHAPUTALA1:

1. Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine. (Yohane 10:27)
2. Mau a “rhema” ndi mau opereka moyo a Mulungu amene amaperekedwa ndi cholinga chokumana ndi chosowa china chake.
3. Mau a “logos” ndi Mau a Mulungu opezeka mu Baibulo. Palibe chimene chiyenera kuonnjezedwa kapena kuchotsedwa mu Baibulo.
4. Pamene mwazindikira mau a Mulungu, mumadziwa chifuniro chake pamene akulankhula nanu.
5. Ahebri 3:7 kapena 5.
6. Chikonzero chachikulu cha Mulungu pamoyo wanu, chitsogozo popanga ziganizo komanso zisankho pamene mukudutsa munyengo za moyo wanu.
7. Chimagwirizana ndi mau olembedwa mu Baibulo “logos.”
8. Tchimo.
9. Wakuchita .... Wakumva.

### CHAPUTALA 2:

1. Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:1-2)
2. Choyenereza ndi chinthu chimene uyenera kuchita kuti china chichitike.
3. Choyenereza choti munthu adziwe chifuniro cha Mulungu ndi: kubadwa mwatsopano, kukhala ndi Mzimu Woyera, kukula muuzimu ndi kusandurika.
4. Mzimu Woyera amavumbulutsa chifuniro cha Mulungu polankhula mkati mwa mzimu wanu.
5. Kuvomereza kuti ndinu ochimwa, kuvomereza machimo anu, kulapa, ndikuvomereza Yesu ngati mbuye ndi mpulumutsi.
6. Muyenera kukhala ndi ubale wapadera ndi Mulungu kuti mukazindikire mau ake.
7. Zimatanthauza kukhwima muzinthu zauzimu ndi cholinga choti mukule muuzumu.

8. Kusintha ndikufanizidwa ndi chifanizo cha Yesu Khristu.
9. Chiganizochi ndi cholondora werengani Aroma 12:1-2.

### **CHAPUTALA 3:**

1. Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. Chikondi. (Yohane 6:38)
2. Perekani zifukwa zimene zaperekedwa mu chaputala 3.
3. Chifuniro cha iye Mwini (Boulema), cha ife mwini ndi chamakhalidwe.
4. Chifuniro cha iwe mwini, chifuniro cha Satana, chifuniro cha Mulungu.
5. a. zabodza; b. zoon. c. zabodza. d. zoon. e. zabodza.

### **CHAPUTALA 4:**

1. Inu Yehova, ndidziwa kuti njira ya munthu siri mwa iye mwini; sikuli kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ace. (Yeremiya 10:23)
2. Mau akuti kutengera amatanthauza kuchita zinthu zimene anthu ena akuchita ndi cholinga
3. a. Zabodza. b. Zabodza. c. Zabodza, d. Zoon. f. Zabodza. g. Zoon. h. Zoon. Zoon.

### **CHAPUTALA 5:**

1. Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. Anatzindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa makonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. Mitundu iwiri ya chifuniro cha Mulungu imene yakambidwa mu chaputala ichi ndi: chifuniro chovumbulutsidwa mu Baibulo ndi chosalembedwa mu Mau a Mulungu. (Aefeso 1:9-10)
2. Mfundo imene igwirizane ndi nyengo imeneyi ikupezeka pa II (Akorinto 6:14-15). Okhulupirira sayenera kuphatikana ndi anthu osakhulupirira.
3. Mulungu akufuna kuti mudziwe chifuniro chake  
Chifuniro cha Mulungu ndi chadongosolo.



Chifuniro cha Mulungu chimakhala pa munthu wina aliyense komanso payekhapayekha.

Chifuniro cha Mulungu chimayang'ana patsogolo.

Chifuniro cha Mulungu ndi chosemphana ndi njira za munthu.

Chifuniro cha Mulungu ndi chabwino.

4. Zabodza.
5. Chithunzi A.
6. Chifuniro changwiro, chifuniro chabwino, chifuniro chovomerezeka, kusemphana ndi chifuniro cha Mulungu.

### **CHAPUTALA 6:**

1. (Aefeso 5:17) Cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani.
2. Wina aliyense mwa anthu anagwiritsidwa ntchito: Mose ndi thanthwe, Eliya pa phiri; Filipino akubwelera ku Samaria; mkumano wa Davide ndi chimphona.
3. Ma a Mulungu olembedwa                      zozizwitsa  
Pemphero    maloto  
Aphungu    masomphenya  
Zitseko zotsekeka ndi zotseguka              kulankhula kwa Mzimu mkati mwanu  
Angelo    mpatso za Mzimu Woyera
4.                      a. Zabodza; b. Zabodza; c. Zabodza, e. Zoon. f. Zoon.

### **CHAPUTALA 7:**

Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, Osacirikizika pa luntha lako; Umulemekeze m'njira zako zonse, Ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako. (Miyambi 3:5-6)

1. Mtendere.
2. Werengani Miyambo 3:5-6.
3. Muyenera kuonetsera Mulungu mu zochitika, mayankhulidwe ndi mmaganizidwe. Ayenera kukhala oyamba mmoyo wanu
4. Pemperani  
Santhulani malemba.

Mvetserani kulankhula kwa Mzimnu mkati mwanu.

Funsiranai uphungu wachikhristu.

Unguzani nyengo zanu.

Gwiritsani ntchito zifunguro za Baibulo kuti mupeze chitsogozo.

Sankhani njira ya mzeru.

5. a. Zabodza; b. Zabodza, c. Zabodza.

### CHAPUTALA 8:

1. Cifukwa cace mungakhale mudyu, mungakhale mumwa, mungakhale mucita kanthu kena, citani zonse ku ulemerero wa Mulungu. (1 Akorinto 10:31)
2. Mchitidwe kapena khalidwe lokaita ndi zinthu zimene sizinakambidwe mu Baibulo kuti ndi zolondola kapena zolakwika.
3. Kodi ziperekeka ulemelero kwa Mulungu?  
Kodi cholinga chake ndi chiani?  
Kodi ndi zofunika?  
Kodi zibweretsa kukula munzimu?  
Kodi zibweretsa chizolowezi chaukapolo?  
Kodi ndi kulekelera?  
Kodi zibweretsa mayesero?  
Kodi pali maonekedwe a choipa?  
Kodi ndi zosemphana ndi chikumbumtina changa?  
Kodi zikhudza anthu ena?
4. M'bale ofooka ndi okhulupirira amene chifukwa cha chikhulupiriro, chikumbumtima ndi chidziwitso chofooka amakhudzika ndi machitiwe a m'bale olimba muchikhulupiriro. Amachimwitsidwa chifukwa cha chikumbumtima chake chauzimu komanso moyo wake wauzimu umatha kukhudzidwa.
5. M'bale olimba muchikhulupiriro ndi amene amamvetsetsa ufulu wake mu magawo ena ake. Chikumbumtima chake sichimagwedezeka ndi maganizo a anthu ena.

6. Kusiyanitsa zinthu zimene malamulo ake alipo ndi zimene anthu amachita mwa ufulu.  
Kukhazikitsa chikumbumtima chanu.  
Kupereka mwayi kwa anthu ena kuti ufulu wao upereke malire ku chikumbumtima chanu.  
Ufulu uzikhala ndi malire chifukwa chachikondi.  
Kukonza kusamvetsetsana.

### **CHAPUTALA 9:**

1. Mtima wa munthu ulingalira njira yace; Koma Yehova ayendetsa mapazi ace. (Miyambi 16:9)
2. Chifaniziro chimapereka chitsanzo choti chitsatidwe.
3. Chifaniziro cha kapangidwe ka chiganizo ndi chitsanzo choyenera kutsatidwa pamene tikupanga ziganizo.

### **CHAPUTALA 10:**

1. Ha! Akadandimvera anthu anga, Akadayenda m'njira zanga Israyeli! (Masalmo 81:13)
2. Werenganinso chaputala 10.
3. Werengani zinthu zimenezi mu chaputala 10.
4. Kuzindikira kufooka kwanu.  
Kulapa.  
Kuzindikira pamene mwalakwitsa.  
Kubwelera kuti mukonze zolakwikazo.  
Kufunafuna Mulungu kuti akupatseni chitsogozo chatsopano.

### **CHAPUTALA 11:**

1. Koteronso iwo akumva zowawa monga mwa cifuniro ca Mulungu aike moyo wao ndi kucita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika. (1 Petro 4:19)
2. Anthu ena amene akuzungulirani.
3. Werengani ubwino wa chizunzo mu chaputala 11.
4. Werengani za kaonedwe ka chizunzo mu chaputala 11.

5. a. Zabodza, b. Zabodza, c. Zoonaa; d. Zoonaa; e. Zoonaa; g. Zoonaa; g. false;

**CHAPUTALA 12:**

1. Koteronso iwo akumva zowawa monga mwa cifuniro ca Mulungu aike moyo wao ndi kucita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika. (1 Petro 4:19)
2. Kusautsika, Vumbulutso, chidodo, chitsikimizo, matamando.